

**UKADAULO
WA
KUPHUZITSA**

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

ZAMKATI MWA BUKULI

| | |
|---|-----|
| Kagwiritsidwe ntchito Ka bukuli..... | 3 |
| Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira limodzi Pagulu..... | 4 |
| Mau oyamba..... | 5 |
| Zolinga za Maphunzirowa..... | 6 |
| 1. Kufotokoza chiyambi chakuphuzitsa | 7 |
| 2. Mphuzitsi amachokera kwa Mulungu..... | 18 |
| 3. Mphuzitsi amachokera kwa Mulungu Uthenga Wake: Gawo I..... | 30 |
| 4. Mphuzitsi amachokera kwa Mulungu: Uthenga Wake- Gawo II..... | 36 |
| 5. Mphuzitsi amachokera kwa Mulungu: Njira- Gawo I..... | 55 |
| 6. Mphuzitsi amachokera Kumwamba: Njira – Gawo II..... | 67 |
| 7. Zothandiza pophuzutsa..... | 84 |
| 8. Kuunikira ophuzira anu..... | 91 |
| 9. Kufotokozera zolinga..... | 108 |
| 10. Kukonza phunziro..... | 116 |
| 11. Kuunikira ophuzira..... | 129 |
| 12. Kupanga ndi kusanka ndondomeko ya kaphuzitsidwe..... | 135 |
| 13. Kuphuzitsa anthu osadziwa kuwerenga..... | 143 |
| 14. Maphuziro a aphuzitsi..... | 148 |
| 15. Mfundo zakulalika | 156 |
| 16. Kukonzekera kulalika..... | 163 |
| Mayankho amafunso odziyankha nokha..... | 177 |

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: Ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Ntchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

MAU OYAMBA

Mutu waphunziro limeli ndi “ukadaulo ophunzitsa” kuphunzitsa ndi mchitidwe opereka uphungu kwa munthu wina. Kuphunzitsa maphunziro a Baibulo ndi kupereka chidziwitso kwa munthu komanso kuonetsera mmene munthu angagwiritsire ntchito chidziwitso chake pa utumiki komanso pa moyo wao wa tsiku ndi tsiku. “ukadaulo” ndi njira zimene zimagwiritsidwa ntchito pofuna kukwaniritsa zolinga. Tikafika dziko la za usilikali, ukadaulo umathandiza kuti munthu aphunzire mmene angagwiritsire ntchito zida zawo ndi cholinga choti agonjetse adani. Mfundo yomweyinso imagwira ntchito mu dziko lauzimu. Ngati tingagwiritse ntchito ukadaulo wauzimu, ndiye kuti tikhoza kugonjetsa adani athu amene ndi dziko, thupi komanso Satana ndi mphamvu zake zonse.

Mu phunziro la ukadaulo, muphunzira mmene mungagwiritsire ntchito zida zauzimu. Chida chimenechi ndi lupanga la Mzimu amene ndi mau a Mulungu. (Aefeso 6:17). Muphunzira ukadaulo ophunzitsa ndi kulalika mau a Mulungu ndi cholinga choti mugonjetse adani anu. Phunziro ili ligwiritsa ntchito mau a Mulungu amene ndi Baibulo limene ndi vumbulutso limene chiphunzitso chinachilichonse chikuyenera kutsamirapo. Pamene tikuphunzitsa zinthu za Baibulo, kuyambira mphunzitsi, mutu waphunziro ndi njira zophunzitsira zikuyenera kugwirizana ndi Baibulo.

Kuphunzitsa sikungomupanga munthu kuti adziwe zinthu kapena chiphunzitso. Koma ophunzira ayenera kukumana ndi Mulungu pamene akuphunzira. Pamene tikuphunzitsa pamakhalanso kusintha kwa chikhaliidwe kapena kuti makhalidwe a munthu. Moyo watsopano umene umayenera kuperekedwa kwa ophunzira ndi moyo wa Khristu Yesu (Yohane 3). Ophunzira akuyenera kuphunzitsidwa mmene angakhalire ngati mzika za ufumu wa Mulungu.

Nthawi zambiri timakhala okhutitsidwa ndi ndondomekozo zimene dziko lapansi zimagwiritsa ntchito pophunzitsa osati kugwiritsa ntchito mfundo zimene mau a Mulungu amagwiritsa ntchito. Phunziro ili likhazikika pa uthenga wa Baibulo ngati njira yophunzitsira. Muphunzira kugwiritsa ntchito njira zimene Yesu amagwiritsa ntchito. Mumvetsetsa udindo wa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera pamene mukuphunzitsa.

Ngati mukuphunzira maphunziro a Haverstine International motsata ndondomeko yake yoyenera, ili ndi phunziro lachiwiri mu gawo la maphunziro otchedwa kuchulukitsa. Ili ndi gawo limene limaona zakuchulukitsa kugawana ndi ena choonadi chazimu. Maphunziro ena mu gawo limeneli la maphunziro ndi awa: “kaonedwe ka zinthu Malingana ndi Baibulo.” Ndongomeko zakuchulukitsa ndi Mfundo za mphamvu”

ZOLINGA ZAMAPHUNZIRO

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kufotokozero kusiyana pakati pa udindo wa mphunzitsi, mphatso ya umphuzitsi ndi lamuro kwa ophunzira onse kuti aphunzitse.
- Kufotokozero cholinga cha mphuzitsi wamkulu amene ndi Yesu. kufotokozero udindo wa Mulungu Mwana, Tate ndi Mzimu Woyera pakuphunzitsa.
- Kugwiritsa ntchito mfundo za Baibulo zophunzitsa.
- Kufotokozero cholinga cha mphuzitsi.
- Kutchula zinthu zomuyenereza mphunzitsi.
- Kusanthula anthu ophunzitsidwa.
- Kufotokozero zolinga za maphunziro
- Kufotokozero ubale pakati pa kuphunzitsa ndi kulalika.
- Kulalika uthenga wa M'baibulo.
- Kupanga zinthu zothandizira pophunzira.
- Kuunguza kaphunzitsidwe ndi malalikidwe anu.
- Kuphunzitsa anthu ena kuti aphunzitse.
- Kusankha ndi kukhazikitsa dongosolo la maphunziro a Baibulo.
- Kupeza njira zothandiza anthu amene sadziwa kulemba ndi kuwerenga.

CHAPUTALA 1

KUFOTOKOZERA CHIYAMBI CHA KUPHUNZITSA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kupeza ndime ya Chipangano Chatsopano imene imalamura okhulupilira kuti aphunzitse.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “phunzitsa” mphunzitsi” ndi chiphinzitsa”
- Kufotokoza chifukwa chokhalira ndi aphunzitsi.
- Kufotokoza kusiyana kwa mphatso ya utsogolera ya mphuzitsi ndi mphatso yolankhula ya kuphunzitsa.
- Kupeza amene ayenera kuphunzitsidwa.
- Kuzindikira zolinga ziwiri zophunzitsira.
- Kutchula machenjezo awiri amene aperekedwa kwa aphunzitsa.

VESI YOTSOGOLERA

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

MAU OYAMBA

Kodi munayamba mwafotokoza anthu ena zinthu zina zimene samadziwa? Kapena munayamba mwaonetsapo munthu wina kachitidwe ka zinthu zinazake? Ngati zili choncho ndiye kuti munaphunzitsapo. Mu phunziro ili muphunzira chafukwa chimene okhulupilira wina aliyense anayenera kudziwa kuphinzitsa. Muphunzira zolinga za kuphunzitsa, kufunika kwa aphunzitsi komanso za anthu amene ayenera kuphunzitsidwa.

Muphunzira za kusiyana kwa mphatso ya utsogolera ya uphunzitsi ndi udindo wa mphuzitsi, komanso tiphunzira za kutumidwa kwa okhulupilira onse kuti aphunzitse. Tionanso za udindo waukulu oti tiphunzitse ndi machenjezo ena opita kwa aphunzitsi.

KUTUMIDWA KUTI TIPHUNZITSE

Kuyambira pa chiyambi cha mbiri ya Babulo, Mulungu analamura anthu ake kuti aphunzitse mau ake:

Ndipo mau awa ndikuuzanilero, azikhala pamtima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansu m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pouka inu. (Deteronome 6:6-7)

Kuphunzitsa mau a Mulungu unali udindo wa munthu wina aliyense mu Chipangano Chakale.

Yesu ataukitsidwa ndipo atatsala pang'ono kupita kumwamba, anauza ophunzira ake kuti:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

Onse amene amatumikira ambuye ali ndi kuthekera kophunzitsa:

Ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kucita ndeu, komatu akhale woyenera, waulere pa onse, wodziwa kuphunzitsa, woleza, And the servant of the Lord must be...apt to teach... (Timoteo 2:24)

Okhulupilira onse amene ndi okhwima akuyenera kutenga gawo pophunzitsa anthu ena. Paulo anadzudzula anthu ena chifukwa chakuti anali osakhwima muuzimu komanso osaphunzitsika.

Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala onga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. (Ahebri 5:12)

Okhulupilira amenewa anali osakula muuzimu kotere kuti samatha kuphunzitsa anthu ena. Iwo amafunikabe kuti aphunzitsidwe (alandire mkaka). Koma okhulupirira wina aliyense ayenera kuphunzitsa ndipo ichi ndi chifukwa chake mutu wakuphunzitsa ndi ofunika kwambiri kwa anthu onse okhulupirira.

KUFOTOKOZERA TANTHAUZO LA KUPHUNZITSA

Mau oti kuphunzitsa amanthauza kuti kupereka chidziwitso, kuonetsera, kukonzekeretsa kapena kuti kutsogolera maphunziro a munthu wina. Mphuzitsi ndi munthu amene amaphunzitsa. Pamene kuphunzitsa ndi mtchitidwe ophunzitsa kapena kukonzekeretsa anthu ena.

NDI CHIFUKWA CHIANI TIMAFUNIKA APHUNZITSI?

Kuphunzitsa ndi kulalika ndi njira zimene Mulungu wasankha kuti akafikire mafuko onse a dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. Werengani nkhani ya mdindo wa ku Itiyopiya (Machitidwe 8:26-40. Munthu amaneyu anali malo oyenera auzimu chifukwa iye anali ku Yerusalemu. Yerusalemu anali malo amene chipembedzo cha mu kachisi chimachitika. (Machitidwe 8:27) Mdindo ameneyu anali malo amenewa pa chifukwa choyenera pakuti iye anabwera kudzapembedza Mulungu. Iye amawerenganso buku loyenera. Iye amawerenga gawo la buku la Yesaya 53:7(Machitidwe 8:30). Komabe iye amafunika munthu kuti amutambasulire malemba kuti amvetse. Tikhoza kunena kuti Iye amafunika mphunzitsi. Mulungu anatumiza Filipo kuti amaphunzitse ndipo mdindoyu anaulandira Uthenga Wabwino ndi kubaditizidwa.

Popamba aphunzitsi, anthu osapulumsidwa ali ngati nkhosha zopanda m'busa. Iwo samvetsa njira imene akuyenera kutenga:

Ndipo anaturuka Iye, naona khamu lalikuru la anthu, nagwidwa cifundo ndi iwo, cifukwa anali ngati nkhosa zopanda mbusa; ndipo anayamba kuwaphunzitsa zinthu zambiri. (Marko 6:34)

Ngakhale okhulupirira amene amavutika nthawi zina kuti amvetse zinthu akakhala kuti sanaphunzitsidwe moyenera.

Anthu anga aonongeka cifukwa ca kusadziwa; popeza unakana kudziwa, Inenso ndikukaniza, kuti usakhale wansembe wanga; popeza waiwala cilamulo ca Mulungu wako, Inenso ndidzaiwala ana ako. (Hoseya 4:6)

ZOLINGA ZENIZENI ZOPHUNZITSIRA

Pali zolinga ziwiri zenizeni za kuphunzitsa ndi kulalika Baibulo. Zolinga zimenezi ndi kufaritsa uthenga Wabwino komanso kupanga ophunzira. Mulungu amagwiritsa ntchito okhulupirira amene ali gawo limodzi la mpingo kuti akwaniritse zolinga zimenezi.

Mpingo ndi gulu la anthu limene lamva Uthenga Wabwino ndi kuchitapo kathu pa kuitana kwa Mulungu komanso ndi anthu amene ayanjanitsidwa ndi Khristu Yesu kudzera mu chikhulupiriro. Mpingo ukhoza kufotokozeredwa ngati gulu la anthu amene alapa machimo awo ndi kuvomereza Yesu ngati mpulumutsi.

Mpingo wa mdera ndi gulu la anthu amene amakumana ndi cholinga chofuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu mudera lawo. Mpingo wina uliwonse wa mdera ndi mbali imodzi ya thupi la Khristu. Thupi la Khristu Yesu limapangidwa ndi okhulupirira a nthawi zonse mu madera onse a dziko lapansi.

Mpingo umatchedwa thupi la Khristu Chifukwa mpingo ndi njira imene Mulungu amagwiritsa ntchito pofuna kukwanitsa zolinga zake. Yesu ndiye mutu wampingo ndipo okhulupirira ndi thupi la Khristu Yesu, limene limakwaniritsa zolinga za Mulungu pa dziko lapansi.

Cholinga chenicheni cha Mulungu pa dziko lapansi chimafokotozeredwa mu buku la Aefeso.

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

Tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wace, cikhululukiro ca zocimwa, monga mwa kulemera kwa cisomo cace, (Aefeso 1:7)

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti munthu wina aliyense akhale pa ubale ndi Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu. Njira yokwaniritsira cholinga chake ndi kugwiritsa ntchito mpingo:

kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: (Aefeso 3:10-11)

Okhulupirira wina aliyense akuyenera kugawana ndi anthu ena uthenga Wabwino komanso kutsogolera anthu ena kuti kuti akhale ndi ubale Wabwino ndi Yesu Khristu. Izi ndi zimene zimatchedwa kuti evangelizimu (kufalitsa uthenga).

Werangani vesi yotsogolera ya phunziro limeneli:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

Pamene munthu wavomeleza Uthenga Wabwino, akuyenera kuphunzitsidwa zinthu zonse zimene Yesu analamura. Ayeneranso kukhala ndi makhaliidwe atsopano a ufumu wa Mulungu umene iwo ndi gawo la ufumu umuo. Chiphunzitsi chimenechi chimatchedwa kupanga ophunzira. Evangelizimu ndi kupanga ophunzira ndipo zinthu ziwirizi ndiye zolinga zenizeni za kuphunzitsa ndi kulalika Baibulo.

NDI NDANI AYENERA KUPHUNZITSIDWA

Timaphunzitsa magulu awiri a anthu:

MAFUKO A DZIKO LONSE

Tikuyenera kuphunzitsa anthu onse osakhulupilira. Munthu wina aliyense wa dziko lapansi akuyenera kumva Uthenga Wabwino. Koma izi zikhoza kukwaniritsidwa pophunzitsa Mau a Mulungu.

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:19)

KWA ANTHU ONSE OKHULUPIRIKA

Tikuyenera kuphunzitsa amayi ndi abambo onse amene ndi okhulupirika komanso amene atembenuka mtima mwa Khristu Yesu.

Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:20)

Anthu amenewa akuyenera kupitiriza ndondomeko imeneyi pakuphunzitsa anthu ena.

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (II Timoteyo 2:2)

Munthu wina aliyense amene waphunzitsidwa akuyenera kuphunzitsa anthu ena amene akuyenera kuphunzitsanso anthu ena. Iyi ndi ndondomeko ya kupitirira kuphunzitsa anthu ena. Izi zimathandiza kuchulukitsa anthu ofaritsa Uthenga Wabwino pa dziko lapansi.

Koma iye amene aphunzira mau, ayenera kucereza womphunzitsayo m'zonse zabwino. (Agalatiya 6:6)

MITUNDU YA APHUNZITSI

Padziko lapansi pali mitundu yambiri ya aphunzitsi. Pali aphunzitsi a sukulu za boma amene amaphunzitsa magulu a anthu osiyanasiyana kuchokera pamene munthu ali mwana kufikira ku sukulu ya ukachenjede. Ntchito ina liliyonse imakhala ndi aphunzitsi amene amaphunzitsa anthu kuchita zinthu zosiyasiyana. Koma pamene tikukamba za aphunzitsi mu phunziro limeneli, sikuti tikukamba za aphunzitsi a maphunziro a dziko lapansi, tikukamba za aphunzitsi amene Mulungu amakhazikitsa mu mpigo komanso ntchito ya okhulupirira pophunzitsa.

Taona kale kuti okhulupirira onse akuyenera kuphunzitsa uthenga wabwino kwa anthu ena (evangelizimu) komanso kuti akuyenera kupanga ophunzira. Koma Mulungu amapereka mphatso yapadera ya uphunzitsi kwa anthu ena.

Ndipotu Mulungu anailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (I Akorinto 12:28)

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Pali kuthekera kosiyanasiyana kumene Mulungu amapereka ndipo izi zimatchedwa “mphatso zauzimu.” Mphatso zimenezi zimathandiza okhulupirira kuti akwanitse cholinga cha Mulungu mu utumiki. Pali mphatso ziwiri zauzimu zakuphunzitsa. Pali mphatso yakuphunzitsa yautsogoleri komanso pali udindo wautsogoleri ophunzitsa. Anthu amene ali ndi mphatso imeneyi amakhala ndi kuthekera kulankhula mau a Mulungu mwamphamvu kotere kuti anthu amene akuphunzitsidwa amatha kugwiritsa ntchito zinthu zimene aphunzitsidwa. Kuthekera kwao kumakhala koposa okhulupirira wina aliyense. Iwo amakhala ndi kud zodza komanso amamva kukakamizidwa kuti aphunzitsa komanso alalike.

Mulungu amaikiza ena mwa aphunzitsi paudindo wa utsogoleri ndi cholinga choti atsogolere utumiki wa mpingo. Machitidwe 13:1-4 amaonetsera za udindo wautsogoleri ophunzitsa. Koma pali anthu ena amena amadzodzedwa ndi Mulungu ndi cholinga choti aphunzitsa osati akhale ndi udindo wautsogoleri. Iwo samayendetsa nawo dongolo la mpingo.

Si wina aliyense amene ali ndi mphatso yautsogoleri yauphunzitsi. Komanso si onse amene ali ndi mphatso yauzimu yo phunzitsa. Paulo analemba:

Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? Ali aphunzitsi onse? Ali onse ocita zozizwa? (I Akirinto 12:29)

Mayankho amafunso osewa ndi Ayi. Siwina aliyense amene ali ndi mphatso zauzimu zimenezi. Thupi la Khristu ndi chimodzimodzi ndi thupi la munthu. Munthu wina aliyense ali ndi malo ake chimodzimodzi thupi la munthu limene chiwalo chinachilichonse chimakhala ndi ntchito yake.

Pakuti monga m'thupi limodzi tiri nazo ziwalo zambiri, ndipo ziwalo zonsezo siziri nayo nchito imodzimodzi; comweco ife, ndife ambiri, tiri thupi limodzi mwa Kristu, ndi ziwalo zinzace, wina ndi wina. Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga

mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapenayakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; (Aroma 12:4-7)

Ndi zofunika kuti muzindikire mphatso zanu chifukwa chakuti ngati thupi lonse likugwira ntchito, cholinga cha Mulungu chimakwaniritsidwa:

kucokera mwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kucititsa kwa ciwalo conse pa muyeso wace, licita makulidwe a thupi, kufikira cimango cace mwa cikondi. (Aefeso 4:16)

Koma kumbukirani kuti ngakhale kuti mulibe mphatso yauphunzitsa, koma Mulungu waitana okhulupirira onse kuti aphunzitse uthenga Wabwino kwa anthu onse a dziko lapansi komanso kupanga ophunzira.

KODI TIMAPHUNZITSA CHIYANI?

Mau a Mulungu ndi a ulamuliro kotere kuti chiphunzitso chinachilichonse chikueyenera kukhazikika pa Baibulo. Mau onse a Mulungu akuyenera kuphunzitsidwa. Pamene mukuphunzitsa mau a Mulungu, simukuyenera kuphunzitsa ziphunzitso za wanthu kapena nzeru za umunthu. Mukuyenera kuphunzitsa chikhalidwe komanso moyo umene anthu ayenera kukhala nawo. Mukuyenera kuphunzitsa chikhalidwe cha ufumu wa Mulungu chimene okhulupilira atsopano akuyenera kukhala nacho. Mukhoza kugwiritsa ntchito mabuku ena pophunzitsa koma mabuku amenewa akuyenera kukhala ogwirizana ndi Baibulo

Patsogolo pa phunziro ili, muphunzira mwatsatanetsane za chiphunzitso cha Baibulo pamene mukhale mukuphunzira zimene Yesu anaphunzitsa komanso zimene mpingo unapitiriza kuphunzitsa Yesu atabwela kumwamba.

MAU OCHENJEZA

Pali machenjezo amene Mulungu akupereka okhudza kuphunzitsa:

CHIPHUNZITSO CHIKUYENERA KUKHAZIKIKA PA MAU OSATI ZIPHUNZITSO ZA ANTHU:

Koma andilambira Ine kwacabe, Ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu. (Marko 7:7)

Kuphunzitsa ziphunzitso kapena malamuro a anthu n zili chabe. Izi zikutanthauza kuti palibe phindu lina lilironse komanso palibe chimene chimakwaniritsidwa. Chiphunzitso cha Baibulo sichimakhazikika pa nzeru ya munthu:

Zimenenso tilankhula, si ndi mau ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu. (1Akorinto 2:13)

Mzeru ya Mulungu imakwaniritsa cholinga cha Mulungu mmoyo wa anthu amene akuphunzitsidwa:

kwa iwo amene Mulungu anafuna kuwazindikiritsa ici 6 cimene ciri cuma ca ulemerero wa cinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Kristu mwa inu, ciyembekezo ca ulemerero; (Akolose 1:27-28)

APHUNZITSI AYENERA KUKHALA CHIMENE AMAPHUNZITSA:

Cifukwa cace yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu comweco, adzachulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakucita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzachulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:19)

Aphunzitsi akuyenera kukhala mogwirizana ndi zimene amaphunzitsa chifukwa chakuti adzaweruzidwa malinga ndi zimene amaphunzitsa.

Musakhale aphunzitsi ambiri, abale anga, podziwa kuti tidzalangika koposa. (Yakobo 3:1)

Aphuzitsi akuyenera kukhala ndi chidziwitso cha mau a Mulungu. Izi zikutanthauza kuti iwo ayenera kukhala zimene amaphunzitsa osati kungodziwa chabe zinthu zimene amaphunzitsazo. Paulo akulankula za anthu amene:

pofuna kukhala aphunzitsi a lamulo ngakhale sadziwitsa zimene azmena, kapena azilimbikirazi. (I Timoteo1:7)

Kumvetsetsa kumabwera pamene tigwiritsa ntchito mau a Mulungu mmoyo wanu.

PADZAKHALA APHUZITSI ABODZA:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. (II Petro 2:1)

Aneneri ena achinyengo amakhala ndi anthu ambiri owatsatira chifukwa chakuti amaphunzitsa zinthu zimene anthu akufuna kumva.

Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola ciphunzitso colamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziuniikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pacoonadi, nadzapatukira kutsata nthanu zacabe. (II Timoteo 4:3-4)

Aphuzitsi ambiri amakhala ndi zolinga zolakwika. Iwo amaphunzitsa ndi zolinga zongofuna kupanga ndalama.

amene ayenera kutsekedwa pakamwa; ndiwo amene apasula mabanja banja lonse, ndi kuphunzitsa zosayenera cifukwa ca cisiro conyansa. (Tito 1:11)

Simukuyenera kuvomeleza chiphunzitso cha aphunzitsi onyenga:

Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa.

Monga tinanena kale, ndipo ndinenanso tsopano apa, ngati wina akulalikirani uthenga wabwino wosati umene mudaulandira, akhale wotembereredwa. (Agalatiya 1:8-9)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Tchulani ndime ziwiri zimene zimatuma okhulupirira kuti aphuzitse

3. Fotokozerani matanthauzo a mau awa:

Phunzitsa: _____

Mphuzitsi _____

Kuphunzitsa _____

4. Ndi chifukwa chiani aphunzitsi ndi ofunika

5. Fotokozani kusiyana kwa mphatso yautsogoleri yophunzitsa ndi mphatso yolankhula yophunzitsa.

6. Kodi chiganizo ichi ndi cholondora kapena ayi? Si okhulupilira onse amene ali ndi mphatso yautsogoleri yophunzitsa, koma okhulupirira onse amayenera kuphunzitsa. chiganizo chimenechi ndi _____

7. Kodi tikuyenera kuphunzitsa ndani? _____

8. Kodi zolinga ziwiri zophunzitsa Baibulo ndi chiani?

_____ ndi _____

9. Tchulani machenjezo awiri amene atchulidwa mu chaputala chimenechi okhudza kuphunzitsa.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. II Petro chaputala 2 ndi buku la Yuda amafotokoza makhalidwe amene tikhoza kugwiritsa ntchito pofuna kuzindikira aphunzitsi a bodza.
2. Ngati simukuzindikira mphatso zauzimu zimene Mulungu anakupatsani, pezana phunziro la Harvest International lotchedwa “*Utumiki wa Mzmu Woyera.*” Izi zikuthandizani kuti muzindikire mphatso yanu ya Mzimu Woyera.
3. Phunziro la *Harvestime International lotchedwa Kufalitsa Uthenga wabwino ngati chotupitsa*” limafotokozera mmene mungafaritsire Uthenga wabwino mopitilira ngati mmene chotupitsa chimafalikira ku mkate.
4. Phunziro la Harvestime International lotchedwa ndondomeko zochulukitsa” limafotokoza mmene mungapangire ophunzira amene ngaobadwa kumene.
5. Werengani zitsanzo zili munsimuzi zokhudza aphunzitsi mu Chipangano Chatsopano. Kodi ndi ndani amene mukuona kuti anali ndi mphatso yautsogoleri yophunzitsa. Komanso ndi ndani wina amene anali ndi mphatso yophunzitsa chabe.

-Apolo: Machitidwe 18:24-25

-Priska ndi Akula: Machitidwe 18:26

-Machitidwe Atumwi 20:20-21,27; 21:28

-Opanda dzina: Machitidwe 13:1

-Petro: Machitidwe 5:28-29

6. Mu phunziro lino taphunzira kuti Mulungu kuchokera pa chiyambi analamula anthu ake kuti aphunzitse mau ake. Pitirizani phunziro la kuphunzitsa mu Chipangano Chakale powerenga ndime izi za Baibulo.

Deteronome 4:9,10,14; 6:9,20; 5:31; 11:19; 17:11; 20:18; 24:8; 31:19; 33:10

Eksodo 4:12,15; 18:20; 24:12; 35:34

Levitiko 10:11; 14:57

Salimo 119:99

Miyambo 9:9; 16:23

Mika 3:11

II Mbiri 17:7

Ezara 7:10

Oweruza 3:2; 13:8

I Samueli 12:23

II Samueli 1:18

I Mafumu 8:36

II Mafumu 17:27

7. Zina mwa zinthu zimene Mulungu amafuna tiphunzitse ndi izi

Salimo 18:34; 25:4-12; 27:11; 32:8; 34:11; 45:4; 51:13; 71:17; 86:11; 90:12; 94:10,12;
05:22; 119:12,68,99,102,104,124,135,171; 143:10; 144:1

II Sameuli 22:35

Yesaya 2:3; 28:9,26; 48:17

I Mbiri 25:7

Mika 4:2

8. Werengani ndime za chiphunzitso.

Salimo 2:10

Miyambo 5:13; 1:2-8; 4:1,13; 6:23; 8:10,33; 9:9; 10:17; 12:1; 13:1; 15:33; 19:20,27;
21:11; 23:12,23; 24:32

Yesaya 8:11

Luka 1:4

Aroma 2:18

Afilipo 4:12

II Timoteyo 3:16

9. Pali zotsatira zokana chiphunzitso cha Mulungu. Werengani ndime izi:

Miyambo 1:7; 5:12,13,23; 13:18; 15:5,32; 16:22

Miyambo 17:23; 32:33

Salimo 50:17

CHAPUTALA 2

MPHUZITSI AMACHOKERA KWA MULUNGU

ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokozerani ntchito ya Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera pakuphunzitsa.
- Kuzindikira Yesu Khristu ngati mphuzitsi wamkulu komanso ngati chitsanzo choti titsanze.
- Kupeza makhalidwe amene akuyenera kuonekera mwa mphunzitsi.
- Fotokozerani cholinga cha Yesu ngati mphuzitsi ochokera kwa Mulungu.
- Fotokozerani mwachidule anthu amene Yesu anaphunzitsa komanso nthawi imene anawaphunzitsa.
- Perekani umboni osonyeza kuti tinatumizidwa ndi Yesu kuti tiphunzitse komanso kuti anatumidwa ndi Mulungu Tate.
- Pezani cholinga chanu ngati mphuzitsi ochokera kwa Mulungu.

VESI YOTSOGOLERA:

Iyeyu anadza kwa Yesu usiku, nati kwa iye, Rabi, tidziwa kuti Inu ndinu mphuzitsi wocokera kwa Mulungu; pakuti palibe munthu akhoza kucita zizindikilo zimene inu mucita, ngati Mulungu sakhala naye, (Yohane 3:2)

MAU OYAMBA

Mu chaputala ichi, muphunzira udindo wa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera pa kuphunzitsa Baibulo. Muphunzira mwatsatanetsatane cholinga cha Yesu Khristu ngati mphuzitsi ochokera kwa Mulungu. Kuchokera phunziro limeneli, muzindikira cholinga cha Mulungu pa inu ngati mphunzitsi.

KULUMIKIZIDWA NDI MULUNGU PAKUPHUNZITSA

Pamene mukuphunzitsa mumapatsidwa mphamvu ndi Mulungu. Izi zikuthandauza kuti pali mphamvu zapadera zimene zimakhala kuseli kwa chiphunzitso. Mlumikizi wauzimu pamene mukuphunzitsa ndi Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

MULUNGU TATE:

Taona kale mu chaputala 1 kuti Mulungu anakhazikitsa anthu ena mumpingo amene ali ndi mphatso yauzimu yophunzitsa (Aefeso 4:11). Pamene mukuphunzitsa chiphunzitso cha Baibulo, zimene mumaphunzitsa ndi Mau a Mulungu. Muphunzira zambiri zokhudza izi mu chaputala

chimenechi pamene mukhale mukuphunzira za uthenga wa mphuzitsi amene amachokera kwa Mulungu.

Ndi Mulungu Tate amane anatumiza Yesu pa dziko lapansi ndi choilinga choti atiphuzitse za Mulungu Tate komanso ndi kupereka Chipulumutso kwa anthu onse.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:16-17)

YESU KHRISTU

Yesu Khristu amane ndi mwana wa Mulungu ndi mphuzitsi wamphamvu wa nthawi zonse. Yesu anatumizidwa pa dziko lapansi ndi Mulungu Tate.

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Yohane 3:2)

Chifukwa chakuti Yesu anatumizidwa pa dziko ngati mphuzitsi oyimira Mulungu, Iye ndi chitsanzo chabwino champhuzitsi wa Baibulo. Yesu ndi amene amatumiza okhulupirira kuti akaphuzitse.

Cifukwa cace Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu. (Yohane 20:21)

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano. (Mateyu 28:18-20)

MZIMU WOYERA

Pamene Yesu anabwelera kumwamba ataukitsidwa, Mulungu Tate anatumiza Mzimu Woyera kuti akakhale mphuzitsi mwa okhulupilira. Mzimu woyera amakhala mkati mwa mzimu wathu ndipo amatiphunzitsa zinthu zokhudza Mulungu:

Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (Yohane 14:26)

Zina mwa ntchito za mzimu Woyera pa kuphunzitsa zikuonekera mu ndime zili munsimuzi:

1. Amakumbutsa zinthu zonse zimene Yesu anaphunzitsa (Yohane 14:26)

2. Amathandiza kukumbukira zinthu zimene mwaphunzira(Yohane14:26)
3. Amatsogolera ku choonadi chonse(Yohane16:13)
4. Amalengeza chikonzero cha Mulungu cha mtsogolo (16:13)
5. Amavumbulutso zinsisi zikuluzikulu za Mulungu (I Akorinto 2:13)
6. Ndi mzeru yothandiza kuphunzitsa Baibulo (1 Akorinto 2:10)
7. Amaphunzitsa zimene mukuyenera kulankhula mu nthawi yamavuto (Luka 12:12)
8. Amadzodza kuti mukathe kuphunzitsa ndi kutumikira (Luka 4:18, I Yohane 2:27)
9. Amathandiza kupemphera pakati pa ophunzira (Aroma 8:26)

Mzimu Woyera amakhalanso akugwira ntchito mmoyo wa aphuzitsi:

1. Pamene mukuphunzitsa, Mzimu Woyera ndi amene amatsutsa ochimwa ndipo amapangitsa kuti anthu alandire Uthenga Wabwino (Yohane 16:7-11)
2. Mzimu Woyera amawatsogolera kuti abadwe mwatsopano (Yohane 3:5,6,8)
3. Amathandiza kuti akhale moyo wauzimu osati wakuthupi (Agalitiya 5:16)
4. Amachitira umboni mu mtima mwao pa chonadi cha Mulungu (Machitidwe 5:29-32)

MPHUZITSI WAMKULU

Yesu ndi chitsanzo cha mphuzitsi chimene tikuyenera kutsanza. Iye ndi chitsanzo chabwino cha mphuzitsi wa Baibulo. Ndipi chifukwa cha ichi, ndi zofunika kuphunzira zambiri zokhudza iye zimene mungakwanitse. Choyamba tikuyenera kuona makhalidwe abwino a Yesu ngati mphuzitsi amene akuyenera kuonekera mwa inu ngati ophunzitsa.

CHIPATSO CHA MZIMU WOYERA

Chipatso cha Mzimu Woyera chimaonekera mu moyo wa Yesu Khristu. Chipatso cha Mzimu woyera ndi makhalidwe abwino amene Mzimu Woyera amafuna tikhakhale nawo ife ngati okhulupirira.

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

Werengani mabuku Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane ndipo fufuzani mmene makhalidwe amenewa amaonekera mwa Khristu Yesu. Mphunzitsi wina aliyense wa mau a Mulungu akuyenera kukhala ndi makhalidwe amene Yesu anaonetsera komanso chipatso cha Mzimu Woyera zimene zimaonetsera ngati munthu ali pa choonadi mu utumiki.

Mateyu 12:23 Ndipo makamu onse a anthu anazizwa, nanena, Uyu si mwana wa Davide kodi? (Mateyu 12:23)

MAKHALIDWE A YESU

Kupatula kuti Yesu anali ndi chipatso cha Mzimu Woyera, Yesu ndi chitsanzoso cha Khalidwe labwinko limene likuyenera kuonekera mmoyo wa mphuzitsi wa Mau Mulungu. Ndime zili munsimuzi zikuonetsera chikhalidwe cha Yesu:

- Yesu amakhudzika ndi anthu komanso zosowa zawo: Mateyu 15:32; Mark1:32-35; 8:2-3; Luka 10:54-56; 19:41
- Kukhudzika kumeneku kumamuopangitsa kuti Iye apemphelera anthu amene amawaphunzitsa: Mateyu 11:21-24; 23:37-39
- Zotsatira za izi zinali kukhala okhudzika ndi kuchita chifuniro cha Mulungu: Luka 2:49; 4:43; Yohane 4:34; 9:4
- Yesu analibe khalidwe loweruza anthu: amene Iye amawaphunzitsa (Mark2:17; Yohane 8:1-11). Iye amalandira anthu malingana ndi mmene aliri ndi kuwapanga kuti afike mlingo wa chikhulupiliro umene amayenera kukhala. Iye sanamuweruze Tomasi chifukwa chapanda chikhulupiriro. (Yohane 20:24-29) Iye samudzudzule mdindo amene amaona kuti kunali koyenera kuti Yesu apite kunyumba yake ndi kupemphelera mwana wake wamkazi (Mateyu 9:18-26) ngakhale kuti Iye anali atawonetsera kale kuti izi sizinali zofunika kuti Iye achite kupita kunyumba yamkuluyu (Mateyu 8:5-13)

Ngakhale kuti Yesu samaweruzira anthu, koma Iye samalekelera tchimo. Izi zikutanthauza kuti iye samavomeleza tchimo kapena kungoyang'anira: Mateyu 11:21-24; 15:3-9; 12:12-13; Marko10:17; Luka 5:31-32; 19:45-46

- Iye anaonetsa ulamiliro ndi kulimba mtima mukuphunzitsa kwakwe: Mateyu: 21:23-27; Marko8:38; 11:24-33; Luka5:24.
- Koma chofunikwa kwambiri ndi chakuti anali ndi mtima otumikira ngati kapolo kwa anthu amene amawatumikira: Mateyu 0:25-28; 23:2-12; Marko10:42-45; Luka22:25-27

CHOLINGA CHA MPHUZITSI WAMKULU

Pamene tikukamba za cholinga cha utumiki wa Yesu tikukamba zinthu izi:

- Chifukwa chimene iye amaphunzitsira
- Nthawi imene amaphunzitsa komanso malo amene amaphunzitsa.
- Anthu amene amaphunzitsa.
- Mmene amaphunzitsira.

Ndi kofunika kuti tiwone mmene Yesu amaphunzitsira, nthawi imene amaphunzitsa komanso malo amene Yesu amaphunzitsa kotere kuti machaputala akubwera akhazikika pa mmene Yesu amaphunzitsira komanso tionanso cholinga cha utumiki wake:

NDI CHIFUKWA CHIYANI IYE AMAPHUNZITSA:

Yesu amaphunzitsa chifukwa chakuti Iye anatumidwa ndi Mulungu kuti atero. Cholinga cha utumiki wa Yesu Khristu chikufotokozeredwa mu ndime izi:

Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula cilamulo kapena ane, neri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. (Mateyu 5:17)

Ndipo m'mene Yesu anamva anati, Olimba safuna sing'anga ai, koma odwala. (Mateyu 9:13)

(Yesu amatanthauza kuti uthenga wake udzabweretsa kugawanika chifukwa chakuti ena adzaulandira komanso ena adzaukana)

Mateyu 5:24 usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nucoke, nuyambe kuyanjana ndi mbale wako, ndipo pamenepo idza nupereke mtulo wako. (Mateyu 15:24) (Mateyu 18:11) ndipo werenganinso Luka 19:10)

Ndipo ananena nao, Tiyeni kwina, ku midzi iri pafupi apa, kuti ndilalikire komwekonso; pakuti ndadzera nchito imene. (Mark1:38)

Ndipo anapita kumudzi kwina. (Luka 9:56)

ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacinatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. 11 Inu ndinu mboni za izi. (Luka 24:46-48)

Yesu ananena nao, Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)

Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)

Pamenepo Pilato anati kwa iye, Nanga kodi ndiwe Mfumu? Yesu anayankha, Munena kuti ndine Mfumu. Ndinabadwira ici Ine, ndipo ndinadzera ici kudza ku dziko lapansi, kuti ndikacite umboni ndi coonadi. Yense wakukhala mwa coonadi amva mau anga. (Yohane 18:37)

Ndadza Ine kuunika ku dziko lapansi, kuti yense wokhulupirira Ine asakhale mumdima. (Yohane 12:46)

Zimene ndinaona Ine kwa Atate, ndilankhula; ndipo inunso mucita cimene mudamva kwa atate wanu. (Yohane 8:38)

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

KODI AMAPHUNZITSA NTHAWI YANJI KOMANSO KUTI?

Yesu anaphunzitsa pa tsiku la Sabata.

(Marko1:21) (werenganinso Luka4:31; 6:6; 13:10).

Iye amaphunzitsa tsiku ndi tsiku.

Ndipo analikuphunzitsa m'Kacisi tsiku ndi tsiku. Koma ansembe akulu, ndi alembi ndi akulu a anthu anafunafuna kumuononga iye; (Luka 19:47)

Iye amaphunzitsa malo achipembedzo opembedzera

Ndipo Yesu anayendayenda m'Galileya monse, analikuphunzitsa m'amasunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumu, naciritsa nthenda zonse ndi kudwala konse mwa anthu. (Werenganinso Mateyu 13:54; Marko1:21; 6:2; Luka 4:15; 6:6; 13:10; Yohane 6:59; 18:20).

Ndipo m'mene Iye analowa m'Kacisi, ansembe akuru ndi akuru anthu anadza kwa Iye analikuphunzitsa, nanena, Mucita izi ndi ulamuliro wotani? Ndipo ndani anakupatsani ulamuliro wotere? (Mateyu 21:23) werenganinso Mateyu 26:55; Marko 12:35; 14:49; Luka19:47; 20:21; 21:37; Yohane 7:14,28; 8:2,20).

ANTHU AMENE IYE ANAPHUNZITSA:

Yesu anaphunzitsa chikhamu cha anthu:

Ndipo m'mene Iye anaona makamu, anakwera m'phiri; ndipo m'mene Iye anakhala pansu, anadza kwa Iye ophunzira ace; ndipo anategula pakamwa, nawaphunzitsa iwo, nati: (Mateyu 5:1-2)

(werengani gawo la zoonjezera pophunzira kuti muone ndime zofotokozera utumiki wa Yesu kwa chigulu cha anthu)

Yesu anaphunzitsa anthu ena paokha.

Werengani Yohane 3 ndi 4 komanso werengani gawo la zoonjezera pophunzira limene likufotokozera utumikwa wa Yesu kwa anthu osiyanasiyana paokhapaokha.

Yesu anaphunzitsa amayi ndi abambo ochokera madera osiyanasiyana a moyo.

- Anaphunzitsa mwini chuma: Mark10:17-22
- Anaphunzitsa anthu asauka: Luka 4:18
- Iye anaphunzitsa anthu osiyanasiyana ocholera magawo osiyanso a moyo. Mwachitsanzo mzimayi waku Samariya munthu oyang'aniridwa pansu (Yohane 4)
- Nikodemo anali munthu wa ulemu wake komanso waulamuliro (Yohane 3)
- Iye anaphunzitsa anthu a mtundu wake omwe.

Ndipo Iye anayankha, nati, Sindinatumidwa kwa ena koma kwa nkhusa zotayika za banja la Israyeli....

Koma iwo anapunda kunena kuti, Amautsa anthuwo, naphunzitsa m'Yudeya lonse, kuyambira ku Galileya ndi kufikira kuno komwe. (Luka23:5)

- Iye anaphunzitsanzo anthu amitundu ina. werengani Yohane 4 pamene Yesu anaphunzitsa mzimayi waku Samariya.
- Anaphunzitsa atsogoleri achipembedzo:
- Iye anaphunzitsa anthu amisinkhu yonse: anaphunzitsa mwini chuma wachichepere (Mark10:17-22) komanso munthu amene anadikira kwa zaka makumi atatu kuti alandire chozizwa (Yohane 5:1-16)
- Cholinga cha utumiki wake chinali cha dziko lapansi lonse, kapena kuti chinali pa anthu onse amitundu, zikhalidwe ndi zilankhuro zonse:

Koma anati kwa iwo, Kundienera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso: cifukwa ndinatmidwa kudzatero. (Luka: 4:43)

Yesu amaphunzitsa mwapadera kwa ophunzira ake:

Ndipo iye sanadya kanthu masiku awo; ndipo pamene anatha anamva njala. (Mark4:2)

Pomwepo Iye anasiya makamuwo, nalowa m'nyumba; ndimo ophunzira ace anadza kwa Iye, nanena, Mutitanthauzire fanizo lija la namsongole wa m'munda. (Mateyu 13:36)

Yesu anaphunzitsa maphunziro apadera kwa ophunzira ake chifukwa chakuti amawaokenzekeretsa kuti akhale atsogoleri mu mpingo.

Koma nthawi zina Yesu amawaphatikiza ophunzira ake ndi gulu la anthu ena ndikuwaphunzitsira limodzi. Werengani 15:1-17:11.

“KOTERO NDIKUTUMANI INU”

Yesu anauza ophunzira ake chinthu chimene ndi chofunika kwa okhulupilira onse. Iye anati:

Monga Atate andituma, ine ndituma inu. (Yohane 20:21)

Izi zikutanthauza kuti okhulupirira atumidwa kupita kudziko lapansi ndi cholinga chofanana chimene Yesu anali nacho. Ngati Yesu Khristu, ndife aphunzitsi ochokera kwa Mulungu. Tikhoza kufotokokera mwachidule cholinga cha utumiki wa Yesu motere: Ngati mmene Mulungu Tate anatumaYesu, nafesonso tatumizidwa kuti tikakwaniritse cholinga chomwe Yesu anali nacho. Cholinga cha Yesu ndi chathu ndi chimodzi. Chifukwa chakuti tiri ndi cholinga chimodzi ndi Yesu, ndi zofunika kuti titsate chitsanzo chake pamene tiphunzitsa.

Cholinga chathu chikuyenera kukhala chopita kwa anthu onse kwina kuli ponse ndi pena paliponse. Tikuyenera kuloranso Mulungu kuti akuze makhalidwe athu kuti akhale ofanana ndi Yesu. Bwerezaninso kuwerenga phunzirio limeneli ndipo pamene mukupanga zimezi, zindikirani kuti mwaitanidwa kuti mukatumikire anthu osochera a dziko lapansi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi ntchito ya Mulungu Tate pakuphunzitsa ndio chiani?

3. Kodi ntchito ya Yesu Khristu pakuphunzitsa ndi chiani?

4. Kodi udindo wa Mzimu Woyera pakuphunzitsa ndi chiani?

5. Malizitsani ziganizo zili munsimuzi polemba mau oyenera pa mpata umene waperekedwa.

_____ anali mphuzitsi wamkulu komanso chitsanzo chabwino chimene anthu akuyenera kutsata.

6. Tchulani makhalidwe ena abwino amene akuyenera kupezeka mwa mphunzitsi

7. Fotokozerani cholinga cha Yesu ngati mphuzitsi ochokera kwa Mulungu

8. Lembani chiganizo chachifupi chokhudza mitu ili munsimuyi. Mu nthawi ya utumiki wake pa dziko lapansi

Kodi Yesu anaphunzitsa kuti?

Kodi Yesu amaphunzitsa nthawi yanji?

Kodi Yesu amaphunzitsa bwanji?

9. Kodi ndi vesi yiti mu Baibulo imene imachitira umboni kuti tatumidwa ndi Yesu ngati mmene Iye anatumidwira ndi Mulungu Tate?

10. Fotokozerani mwachidule cholinga chanu ngati mphuzitsi ochokera kwa Mulungu

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani ndime zili munsimu zokhudza utumiki wa Yesu Kwa ku gulu la anthu.

Mateyu: 5:1-2; 7:28-29; 8:1-2 [anthu pakati pa gulu]; 8:16-17,34; 9:1-8,36-

38; 11:7; 13:1-9; 14:13-23; 15:30-39; 17:14; 19:2; 20:29-34; 21:8-11; 22:23; 26:47

Marko: 1:33-35,45; 2:1-5,7-15,20-21,32-35; 4:1-36; 5:14-17,21-43; 6:2-5,33-46,55-56;
7:24,31-37; 8:1-9; 9:14-27; 10:1,46-52; 11:8-10; 14:43-52; 15:8

Luka: 2:45-52; 4:16-30,40-44; 5:1,15-16,18-26; 6:17-7:1; 7:11-18; 8:1,37,40,56; 9:12-18,37; 12:1; 13:11-17; 18:35-43; 19:1-10,36-40; 22:47; 23:1

Yohane: 2:1-11; 4:39-42; 5:1,13; 6:5-15,22; 7:40; 8:1-9; 12:9,12-13

1. Werengani ndime izi zokhudza utumiki wa Yesu Khristu kwa anthu:

Mateyu: chaputala 8 Kwa munthu wakhate, kwa mpongozi wake wa Petro, chaputla 9: kwa mzimayi odwalika kwambiri, mzibambo wa dzanja lopuwala.

Marko 1:23-26 (mzimbambo wa mzimu onyasa mu sunagogi); 1:40-45 (wakhate); 5:1-20 ("chikhamu"); 8:22-26 (munthu wa khungu); 10:46-52 (Batumeyu wakhungu).

Luka: 7:11-17 (munthu wakufa); 8:2 (Mariya wakumagadala); 9:57-62 (anthu amane anakhala ophunzira ake); 10:25-37 (mkulu wa chilamuro); 10:38-42 (Marita); 12:13-15) (Mzimayi wa mzimu wamatenda 19:1-10 (Zakeyu).

Yohane: 1:47-51 (Natanieli); Chaputala 3 (Nikodemo); 4:4-42 (Mzimayi waku Samariya); 5:1-16(mzibambo ulumala pa Betasaida); 8:1-11 (mzimayi ogwidwa ndi chigoloro); Chaputala 9 (Mzibambo wakhungu chibadwire); Chapter 11 (Lazaro ndi Malita); 13:1-10; 21:15-25 (Petro); 19:25-27 (mayi ake);

2. Yesu akutchedwa mphunzitsitsi malo okwanira 48 mu mauthenga abwino. Pezani malo amenewa mu Baibulo.
3. Harvestime International institute ili ndi phunziro lotchedwa "Utumiki wa Mzimu woyera" limene limapereka zambiri zakufunika kwa Mzimu Woyera pa moyo wa munthu komanso pa Utumiki.
4. Mwaphunzira mu phunziro ili mmmene Yesu khritsu amaphuzitsira malo ena alionse komanso nthawi ina iliyonse. Izi zikuchokera pa mfundo ya Chipangano chakale imene Yesu imene ikupezeka pa Deteronome 6:6-7. Werengani ndime imeneyi mu Baibulo lanu
5. Werengani tchati chili pansichi kuti muonjezere chidziwitso chanu cha mphamvu ya umulungu yopezeka pamene munthu akuphunzitsa.

Makhalidwe a chivumbulutso

I Akorinto 2:9-13

| | |
|--|--|
| <p>koma monga kulembedwa, Zimene diso silinazona, ndi khutu silinazimva, Nisizinalowa mu mtima wa munthu, Zimene ziri zonse Mulungi anakonzereratu iwo aku mkonda iye.</p> <p>Koma kwa ife Mulungu anati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe. Pakuti ndani wa anthu adziwa za munthu, koma mzimu wa munthuyu uli mwa iye? momwemonso za Mulungu palibe wina azidziwa, koma Mzimu wa Mulungu.</p> <p>Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwaifulu.</p> <p>Zimenenso tilankhula, si ndi mau ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu.</p> | <p>Zimene tikudziwa sizikutengera zimene timazidwa paumunthu wathu.</p> <p>Cholinga cha Mzimu Woyera pakuphunzitsa</p> <p>Cholinga cha vumbulutso</p> <p>Mavumbulutso amabwera kudzera mu mau operekedwa mwa mzimu woyera.</p> |
|--|--|

Mbali yathu

Ndipo ine, abale, m'mene ndinadza kwa inu, sindinadza ndi kuposa kwa mau, kapena kwa nzeru, polalikira kwa inu cinsinsi ca Mulungu.

Pakuti ndinatsimikiza mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu koma Yesu Kristu, ndi iye wopacikidwa. Ndipo ine ndinakhala nanu mofoka ndi m'mantha, ndi monthunthumira mwambiri.

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu

Koma tilankhula nzeru mwa angwiro; koma si nzeru ya nthawi yino ya pansi pano, kapena ya akulu a nthawi yino ya pansi pano, amene alinkuthedwa; koma tilankhula nzeru ya Mulungu m'cinsinsi, yobisikayo, imene Mulungu anaikiratu, pasanakhale nyengo za pansi pano, ku ulemerero wathu,

Mbali ya Mulungu

Chionetsero cha mphamvu ya Mzimu Chimene chaonetseredwa ndi Mulungu.

- **Mzimu amaonetsera zinthu zimene zizingazindikiridwe ndi munthu wakuthupi.**
- **Amavumbulutsa zinsisi za Choonadi cha Mulungu.**
- **Ndi yekha amene amvetsetsa malingaliro a Mulungu.**
- **Amapereka kumvetsetsa zokhudza chisomo cha Mulungu.**

Ife ndife atumiki amene Mulungu wapereka watipatsa ntchito kuti tigwire

Ena amadzala mbeu koma ndi Mulungu amene amathilira mbeuyo.

CHAPUTALA 3

MPHUZITSI AMACHOKERA KWA MULUNGU: UTHENGA WAKE – GAWO 1 ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokozerera mwachidule zimene Yesu amaphunzitsa.
- Kupeza ndime zimene zinafotokozerera nsanamira za uthenga Wabwino.
- Kuzindikira kuti okhulupirira ali ndi udindo oti aphunzitse Uthenga umene Yesu anaphunzitsa.
- Kuzindikira kuti kuphunzitsa ndi kulalikira kukuyenera kuyenda limodzo ndi chionetsera cha mphamvu.
- Kuzindikira Baibulo ngati maziko a chiphunzitso.

VESI YOTSOGOLERA

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citseguldwa. (Mateyu 10:7-8)

MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira cholinga cha Yesu pophunzitsa chimene pakadali pano ndi udindo wathu wa ife okhululupilira. Tinaonanso makhalidwe a Yesu amene ayenera kuonekera mmoyo wa okhulupilira. Komu mu chaputala ichi, muphunzira zinthu zimene Yesu amaphunzitsa. Yesu analibe nthawi yaitali kuti aphunzitse ophunzira ake. Iye anali ndi nthawi yochopa chabe kotere iye amakhazikika pa mfundo zikuluzikulu. Zimene Yesu amaphunzitsa zikuyenera kukhala cholinga cha chiphunzitso chanu.

NSANAMIRA YA CHIPHUNZITSO CHA YESU

Nsanamira ya uthenga wa Yesu ikhoza kufotokozeredwa motere: Iye anaphunzitsa zinthu zonse zokhudza Ufumu wa Mulungu.

Anthu onse amakhala mu ufumu wakuthupi wa dziko lapansi. Anthu amakhala mu mzinda kapena kumudzi zimene ndi gawo limodzi la dziko. Dziko limeneli ndi ufumu wa dziko lapansi. Kuonjezera ufumu wa dziko lapansi wakuthupi, palinso maufumu awiri auzimu. Ndipo munthu wina aliyense ndi mzika ya umodzi mwa maufumu amenewa. Maufumu amenewa ndi Ufumu wa Satana ndi Ufumu wa Mulungu. Osakhulupilira onse ndi gawo limodzi la Ufumu wa Satana ndipo kuti Satana ndi amene amalamulira moyo wao. Anthu amenewa ali ndi chikhalidwe chachikunja. Koma anthu onse amena analapa machimo awo ndi kuvomelera Yesu Khristu ngati olamulira wa moyo wao ndi gawo la ufumu wa Mulungu. Mulungu ndiye mfumu yawo ndipo amalamulira moyo wao:

Uthenga wa Ufumu wa Mulungu chinali cholinga chachikulu cha moyo wa Yesu Khristu. Iye anayamba utumiki wake pakulengeza za Ufumu wa Mulungu.

Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)

Iye anamaliza utumiki wake wa dziko lapansi polankula zinthu zokhudza Ufumu wa Mulungu:

Cifukwa anali wowerengedwa mwa ife, ndipo analandira gawo lace la utumiki uwu. (Machitidwe 1:17)

Kuyambira pachiyambi kufikira kumapeto kwa utumiki wake pa dziko lapansi, Ufumu wa Mulungu chinali cholinga chake chachikulu mu utumiki wa Yesu Khristu.

Koma anati kwa iwo, Kundiyenera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso: cifukwa ndinatamidwa kudzatero. (Luka 4:43)

Mafanizo a Yesu Khristu amakhazikika pa Ufumu wa Mulungu. Zozizwa zimene anachita zinali chionetsera cha mphamvu ya Ufumu wa Mulungu. Yesu anaphunzitsa anthu kuti alowe mu Ufumu wa Mulungu pakubadwanso mwatsopano. Yesu anaphunzitsanso mmene anthu angakhalire gawo limodzi la Ufumu wa Mulungu pokuzi chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu. (Werengani Mateyu 5:7). Izi ndi zimene zimatchedwa kupanga ophunzira.

Chifukwa cha kufunika kwa phunziro la Ufumu wa Mulungu, Haverstine Interanational ili ndi phunziro lotchedwa “Chikhalidwe cha Ufumu” ngati simunaphunzire phunziro limeneli ndi kofunika kuti mupeze phunziro limeneli chifukwa limaphunzitsa mwatsatanetsatsane mfundo za Ufumu wa Mulungu.

Phunziro lina lotchedwa maziko a chikhulupiriro limafotokoza nsanamira imene Ufumu wa Mulungu wakhazikika.

Ngati mukhuphunzira maphunziro motsata mndandanda umene unaperekedwa, ndiye kuti maphunziro amenewa munaphunzira kale.

NSANAMIRA ZA UTHENGA WABWINO

Pali ndime ya Chipangano Chatsopano imene imafotokozeri mwachidule nsanamira za Uthenga Wabwino.

Ndipo ndikudziwitsani, abale, Uthenga Wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenenso munalandira, umenenso muimamo, umenenso mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikira kwa inu; ngati simunakhulupira cabe. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristuanafera zoipa zathu, mongamwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo; (I Akorinto 15:1-4)

Nsanamira yaikulu ya Uthenga Wabwino ndi yakuti Yesu Khristu anafera machimo athu. Ndipo malingana ndi malembo, iye anaikidwa mmanda, ndipo anauka kwa akufa malingana ndi Baibulo. Pamene mukhuphunzitsa kapena kulalika Uthenga Wabwino, uthenga wanu ukuyenera

kukhazikika pa mfundo zimenezi. Yesu Khristu ndi nsanamira ya Uthenga Wabwino. Chiphunzitso cha Baibulo chikuyenera kukhazikika pa mmene anthu angalowera mu Ufumu wa Mulungu komanso mmene munthu akuyenera kukhalira moyo wauzimu.

MAU A MULUNGU

Yesu anaphunzitsa mau a Mulungu okhudza choondi:

Ndipo anatomiza kwa Iye ophunzira ao, pamodzi ndi Aherode, amene ananena, Mphunzitsi, tidziwa kuti muli woona, ndipo muphunzitsa njira ya Mulungu moona ndithu, ndipo simusamala munthu ali yense; pakuti simuyang'anira pa nkhope ya anthu. (Mateyu 22:16)

Anaphunzitsanso ndondomeko za chiphunzitso cha Chachikhulupiliro.

Ndipo anawaphunzitsa zinthu zambiri m'mafanizo, nanena nao m'ciphunzitso cace, (Mark4:2)

Mutha kuona kuti njira imene Yesu amagwiritsa ntchito pophunzitsa ndi yakuti amagwiritsa ntchito Chipangano chakale nthawi zambiri. Chiphunzitso cha Baibulo chikuyenera kugwiritsa ntchito mau onse a Mulungu chifukwa chakuti mau a Mulungu ndiye nsanamira ya mmene tingangaphunzitsire makhalidwe a Ufumu wa Mulungu.

Koma zindikira ici, kuti masiku otsiriza zidzafika nthawi zowawitsa. Pakuti anthu adzakhala odzikonda okha, okonda ndarama, odzitamandira, odzikuza, amwano, osamvera akuwabala, osayamika, osayera mtima, opanda cikondi cacibadwidwe, osayanjanitsika, akudierekeza, osakhoza kudziletsa, aukali, osakonda abwino, aciwembu, aliuma olimbirira, otukumuka mtima, okonda zokondweretsa munthu, osati okonda Mulungu; akukhala nao maonekedwe a cipembedzo, koma mphamvu yace adaikana; kwa iwonso udzipatule, Pakuti mwa iwo akhala akukwawira m'nyumba, nagwira akazi opusa, osenza akatundu a zoipa zao, otengedwa nazo zilakolako za mitundu mitundu: (II Timoteyo 3:1-6-17)

KUTUMIDWA KWA OKHULUPILIRA

Okhulupirira anatomidwa ndi Yesu Khristu kuti aphunzitse ndi kulalikira uthenga umene Yesu anaphunzitsa: Uthenga wa ufumu wa Mulungu. Yesu anauza ophunzira ake kuti:

Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)

Chiphunzitso cha Yesu chimatsindika kufunika kochulikitsa. Iwo amene alowa mu ufumu wa Mulungu ali ndi Udindo oti abale kapena kuti kubweretsa anthu ena mu Ufumu wa Mulungu. Iyi ndi njira yothandiza kuti Ufumu wa Mulungu upitilire kufalikira pa dziko lapansi. Anthu obadwa

mwatsopano mu Ufumu wa Mulungu akuyenera kukhala ophunzira a Yesu Khristu. Ophunzira ndi mwana wasukulu amene amaphunzira ndi kuyamba kugwiritsa ntchito zinthu zimene waphuzira kuchokera kwa aphunzitsi ake. Ophunzira akuyenera kukhala mtumwi. Mtumwi ndi munthu amene amatumidwa ndi cholinga chapadera chochokera kwa munthu otuma.

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (II Timoteyo 2:2)

Ndi zofunika kwambiri kuti mukhulupilirike ku kutimidwa koti tikafaritse Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu chifukwa chakuti pamene tidzamaliza ntchito imeneyi ndi pamene Ufumu wa dziko lapansi udzathe.

Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)

CHIONETSERO CHA MPHAMVU

Ufumu wa Mulungu sunangokhazikika pa kulankhula kokha ayi. Koma umayendera limodzi ndi chionetsero cha mphamvu ya Ufumu wa Mulungu. Yesu anati:

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, (Luka 4:18)

Ufumu wa Mulungu umaonetseredwa pamene Yesu amaphunzitsa:

Ndipo pamene Yesu analikuyenda m'mbali mwa nyanja ya Galileya, anaona abale awiri, Simoni wonenedwa Petro, ndi Andrey, mbale wace, analikuponya psasa m'nyanja; popeza anali asodzi a nsomba. (Mateyu4:23)

Cifukwa cace yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu comweco, adzachulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakucita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzachulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:19)

Pamene Yesu anawatuma ophunzira ake kuti alalikire uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu, iye anawauza kuti:

Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)

Uthenga wa Ufumu wa Mulungu ukuyenera kuyenda limodzi ndi chionetsero cha mphamvu ya Mulungu imene imasintha moyo wa anthu. Chifukwa chakufunika kwa phunziro limeneli, Harvestime International Institute ili ndi phunziro limene limatchedwa kuti mfundo za mphamvu. ukadaulo wa kuphunzitsa umene mumphunzire mu chaputala ichi ukuyenera kuyenda limodzi ndi chionetsero cha mphamvu. chifukwa cha ichi, ndi zofunikwa kwambiri kuti muphunzire ndi kugwiritsa ntchito mfundo zimenezi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi nsanamira ya Uthenga umene Yesu amaphunzitsa inali chiani?

3. Perekan ndime ziwiri zimene zimafotokozerwa mwachidule nsanamira za Uthenga Wabwino.

4. Kodi chiganizo ichi ndi cholondora kapena ayi: okhulupirira akuyenera kuphunzitsa uthenga omwe Yesu anaphunzitsa

Chiganizo chimenechi ndi _____

5. Kuphunzitsa ndi kulalikira kukuyenera kuyendera limodzi ndi chionetsero cha mphamvu ya _____

6. Kodi ndi buku liti limene limaphunzitsa Uthenga wa Ufumu wa Mulungu.

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pezani phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “Chikhalidwe cha Ufumu” kuti muphunzire zambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu.
2. Maziko a chikhulupiliro ndi mphunziro lina limene limafotokoza nsanamira zikulu zikulu zimene Uthenga Wabwino wakhazikika.
3. Pezani phunziro lina la Harvestime International Institute lotchedwa Mfundo za Mphamvu kuti mopitilire kuphunzira. Werengani mmene chionetsero cha mphamvu chikuyenera kuyendera limodzi ndi kuphunzitsa ndi kulalika kwanu.

CHAPUTALA 4

MPHUZITSI AMACHOKERA KWA MULUNGU: UTHENGA GAWO II

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kupitiriza kuphunzira uthenga umene Yesu anaphuzitsa.
- Kugwiritsa ntchito phunziro limeneli kuti mugawane ndi ena chiphuzitso cha Khristu.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa iye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa iye monse mulibe mdima. (1 Yohane 1:5)

MAU OYAMBA

Uthenga wa Yesu kwambiri umakhazikika pa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Kodi kodi iye amaphunzitsa chiani kwenikweni?

KODI MUNGAPHUNZITSE BWANJI ZIMENE YESU ANAPHUNZITSA

1. Pezani Baibulo limene limalemba mau amene Yesu analankhula mu malemba ofira koma dziwani kuti ma Baibulo amenewa amakhala a chingerezi. Baibulo limeneli limathandiza kuti musanthule mau onse amene Yesu anaphunzitsa. Werengani ma buku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane komanso ma chaputala ena a Machitidwe. Chifukwa chakuti Baibulo la chichewa lilibe zimenezi, mukhoza kumangodula mzere kungsi kwa Mau onse amene Yesu analankhula.
2. Werengani Machitidwe ndi Makalata (kuyambira Aroma mpaka Yuda) Onani zimene okhulupirira amenewa amaphunzitsa pamene amakwaniritsa kutumidwa kwao ndi Yesu Khristu.
3. Gwritsani ntchito mndandanda uli munsiu kuti muphunzire zimene Yesu anaphunzitsa.

CHIPHUNZITSO CHIMENE YESU ANAPHUNZITSA

Mndandanda umeneu ukutchula ma vesi ndi zinthu zonse zimene Yesu anaphunzitsa nthawi ya utumiki wake pa dziko lapansi. Ziphunzitsa zimenezi zagawidwa malinga ndi mitu ya ziphunzitsa zimene amaphunzitsa.

Pali mabuku anayi mu Baibulo amene amafotokozera chiphunzitsa cha Yesu. Mabuku amenewa ndi a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane. Koma pali chiphunzitsa china cha Yesu chimene chikubwerezedwa mu mabuku onsewa kotere kuti ndime zimenezi zabweretsedwa pamodzi.

Mndandanda umeneu ukuthandizani kuti muphunzitse choonadi chimene Yesu anaphunzitsa ndipo zikuthandizani kuti mufaritse Uthenga Wabwino dziko lonse lapansi.

Zindikirani kuti chifukwa cha mmene ndime zimenezi zalembedwera, chaputala chimenechi chilibe gawo la zoonjezera pophunzira.

UTATU WA MULUNGU

MULUNGU TATE

Mateyu 11:27; 19:17,26; 22:32; 23:9

Mark12:26-27,29; 10:18,27

Luka 10:22; 18:19,27; 20:37-38

Yohane 4:24; 5:17,37; 6:46; 10:29; 14:28,31; 15:8

MULUNGU MWANA, YESU KHRITSU

Chikhalidwe chake cha umulungu

Mateyu 9:5-6; 10:32-33; 11:4-6,27; 12:6,41-42; 16:13,15,17,27; 21:42; 22:42-45; 23:10;

26:53,64; 27:11; 28:18

Marko 2:9-11,28; 8:27,29; 12:10-11,35-37; 14:62; 15:2

Luka 5:23-24; 6:5; 7:22-23; 9:18,20; 10:22; 11:20,31-32; 19:40; 20:17-18,41-44; 22:69-70; 23:3

Yohane 1:51; 3:13; 4:10,26,32; 5:17,19-23,26-27,30-32,34,36-37,39,41; 6:27,29,35,46,51,62;
7:17-

18; 8:14,16-19,23,25,29,42, 50,54-56,58; 9:35,37; 10:25,30,34-38; 12:30,44-45; 13:31-32;

14:1,6,7,9-11,20; 15:23; 16:15,27-28; 17:1-3,5,8,10-11,21-24,28-29; 18:36-37; 19:11

Umunthu wake:

Mateyu 3:15; 8:20; 11:19; 26:10-13,38-39,42,45; 27:46

Mark14:7-9,26,34,36,41; 15:34

Luka 7:34; 9:58; 22:28,42; 24:39,41

Yohane 4:7; 12:7-8; 19:26,28; 20:27; 21:5,12

Cholinga Chake:

Mateyu 4:4; 5:17; 9:12-13; 10:34-36; 11:15; 15:26; 18:11-13; 21:33-40

Mark1:38; 2:17; 4:21-22; 7:16,27; 12:1-9

Luka 2:49; 4:18-19,21,23-27,43; 5:31-32; 8:16,17; 11:30,33; 12:2-3,14,49,51-53; 13:32-33;

19:10; 20:9-16

Yohane 3:19-21; 4:13,14,34; 5:25,28-30; 6:38-40,50,55,56,58; 7:7,16; 8:12,26; 9:3-5,39; 10:1-
5,7,9-18,27-29; 11:4,9,10; 12:26,27,47-50; 13:20; 18:15,16,37

Utumiki wake:

Mateyu 9:15,37,38; 12:25-30; 20:28

Mark2:19; 3:23-27; 10:45

Luka 5:34; 11:17-23

Yohane 2:4; 3:11; 4:35-38; 12:35,36

Udindo wake:

Mateyu 10:29-30; 11:28-31

Luka 4:18,19; 8:52

Yohane 6:37; 7:37; 10:9; 11:25,26; 12:32; 14:1,2,6,13,14,16,27; 15:1,2,4-6,9-11,15-16,18,19;
16:1,4,23,24,33.

MZIMU WOYERA:

Mateyu 10:19,20; 12:31,32; 28:19

Mark3:28,29

Luka 12:10-12

Yohane 3:8; 6:63; 16:7-11,13,14; 20:22

Machitidwe 1:8

UFUMU WA MULUNGU NDI WAKUMWAMBA

Mateyu 4:17; 5:20; 6:33; 7:21; 8:11; 10:7; 11:11-13; 13:3-8,11,18-33; 37-50,52; 16:28; 22:2-
14; 25:14-30; 26:29

Mark4:3-8,11-20,26-29; 9:1; 14:25

Luka 8:5-15; 9:27; 10:11; 11:20; 12:31; 13:18-21,29,30; 17:20,21; 19:12-27; 21:31; 22:18

MPINGO

Mateyu5:13-15; 12:48-50; 16:18,19; 18:17-20; 21:13; 23:16-21; 24:22,31

Mark3:33-35; 11:17; 12:10; 13:20,27

Luka8:21; 11:23; 12:32; 19:26

Yohane 2:16; 4:23,24; 13:35; 17:20,21; 20:23

CHILAMURO, MALEMBA NDI ANENERI

Mateyu 5:17,18; 7:12; 8:4; 11:13; 21:42; 26:54

Mark1:44; 12:10,11; 14:21,29

Luka 5:14; 10:26,28; 16:16,17,29-31; 17:14; 18:31; 21:22; 22:22,37; 24:25,26,44,46

Yohane 5:39,45-47; 7:12,19; 8:17,18; 10:34-36; 15:25

MAU

Mateyu 4:4; 7:24-27; 10:27; 11:15; 13:3-9,19-23; 28:19,20

Mark4:3-9,14-20,23,24; 13:31

Luka 4:4,18,19,43; 6:46-49; 8:5-8,10-15,18; 10:24

Yohane 3:11; 5:24,25,28,46,47; 6:63; 7:17,18; 8:14,31,32,38,45-57; 10:27; 12:47-50;
14:10,21,23-25; 15:7,10,12,14,15,17,20,22; 16:12,13,25,33; 17:6-8,13,14,19,20,25,26; 18:20,37

NTHAWI YAKALE NDI YATSOPANO

Nthawi yakale ikuimira mmne Mulungu anachitira ndi anthu mu Chipangano Chakale. Zina za nthawi imeneyi ndi chilamuro komanso nsembe zosiyanasiyana zochotsa machimo zimene zafotokozeredwa mu buku la Levitiko.

Pamene nthawi yatsopano ikutanthauza mmene Mulungu anachitira ndi anthu mu nthawi imene Yesu anatomikira pa dziko lapansi. Iyi imatchedwa kuti nthawi ya chisomo imene nsembe yomaliza ya Yesu Kristu inaperekedwa pa mtanda paja.

MNENERI ALENGEZA ZA NTHAWI YATSOPANO:

Munthu otchedwa Yohane mbatizi anatomidwa ndi Mulungu kuti alengeze zakubera kwa nthawi yatsopano. Yesu anaphunzitsa zokhudza iye mu ndime zili musimuzi.

Mateyu7:11; 11:7-11,14,18; 21:25

Marko 9:13; 11:30

Luka 7:24-28,33; 20:4

Yohane 5:33,35

ZIPHUNZITSO NTHAWI ZATSOPANO:

chiphunzitso cha Yesu chokhudza nthawi yakale ndi yatsopano chikuepezeka mu ndime zili munsimuzi:

Mateyu 5:17; 11:27; 26:27,28

Marko 14:24

Luka 10:22; 16:16; 22:20

Yohane 4:23; 5:25; 6:32,33,49,58

I Akorinto 11:25

OPHUNZIRA A YESU

Chiphunzitso chili munsimuchi chinapita kwa ophunzira a Yesu Kristu.

Mateyu13:11,16,17,51; 16:8-11; 17:7; 18:18; 21:2,3; 23:10; 24:9; 26:38,40,45

Mark4:11,12,35; 6:31; 8:17-20; 11:2,3; 13:9,11,13; 14:27,32, 34,41; 16:15

Luka 8:10,22; 10:23-24; 19:30,31; 21:14-19; 22:28-30,35,36,38; 24:49

Yohane 6:61,67,70; 12:30; 14:25,31; 15:12,16-20,27; 16:2,3,27,32; 20:21-23

CHIPHUZITSO CHOPITA KWA OPHUNZIRA OWERENGEKA

Petro ndi Andreyo

Mateyu 4:19

Mark1:17

Mateyu:

Mateyu 9:9

Mark2:14

Petro:

Mateyu 16:17-19,23; 17:25-27; 26:34

Mark8:33; 14:30,37

Luka 5:4,10; 22:31,32,34,51

Yohane 1:42; 13:7,8,10,36,38; 18:11; 21:15-19,22

Thomasi:

Yohane 20:27,29

Filipo:

Yohane 14:9

Yudasi:

Yohane 13:27

KUTUMIZA OPHUNZIRA

Mau apadera anaperekedwa kwa ophunzira pamene anawatumiza kuti akafaritse Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu.

MAU OLANKHULIDWA KWA OPHUNZIRA KHUMI NDI AWIRI

Mateyu 10:5-42

Mark6:10,11

Luka 9:3-5

MAU OLANKULIDWA KWA OPHUNZIRA MAKUMI ASANU NDI AWIRI

Luka10:3-12,16,19,20

PEMPHERO LA YESU KHRISTU

Ndime zimenezi zikuonetsera mapemphero amene Yesu anapemphera ndipo analembedwa mu Baibulo. Kupatula kuphunzira zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza pemphero, ndi zofunika kuunikira mmene anagwiritsira ntchito zinthu zimene anaphunzitsa mmoyo wake wapemphero.

Mateyu 6:9-13; 11:25,26; 26:36,39,42

Marko 14:36

Luka 10:21; 11:2-4; 22:42

Yohane 11:41,42; 17:1-26

ZINTHU ZIMENE ZINACHITIKA MMOYO WA YESU

Yesu anaphunzitsa za zinthu zimene zimayenera kuchika mmoyo wake komanso anagwiritsanso ntchito zochitika zapadera kuti afaritse Uthenga Wabwino. Zina mwa zinthu zimenezi ndi izi:

MAZUZO NDI MAYESERO

Mateyu 17:12; 13:57; 26:38

Marko 6:4; 9:12; 14:34

Luka 4:24; 9:22; 17:25; 22:28; 24:46

NGONERO OMALIZA WA AMBUYE

Mateyu 26:18,26-29

Mark14:13-15,22,24,25

Luka 22:8,10-12,15-20

I Akorinto 11:24,25

KUPEREKEDWA:

Mateyu 17:22; 26:2,21,23-25,46,50,55

Mark14:18,20,21,42,48,49

Luka 22:21,22,48,52,53

Yohane 13:18,19,26; 18:4,5,7,8,23

KUPACHIKIDWA

Luka 9:44; 22:37

Yohane 3:14; 8:28; 12:31,32.

MAU OLANKHULIDWA PAMTANDA

Mateyu 27:46

Mark15:34

Luka 23:34,43,46

Yohane 19:26,27,28,30

MAU OYANKHULIDWA PA MTANDA:

Mateyu 27:46

Mark15:34

Luka 23:34,43,46

Yohane 19:26,27,28,30

IMFA, CHIUKITSO NDI KUKWERA KUMWAMBA:

Mateyu 12:40; 17:19,22,23; 20:18,19; 26:12,31,32

Mark9:31; 10:33,34; 14:8,27,28

Luka 5:35; 9:22; 12:50; 18:31-33

Yohane 2:19; 3:13; 6:62; 7:33,34; 8:21; 10:17,18; 12:7,23,24; 13:33; 14:19,29; 16:5-7,16,19-22,25,26,32; 20:17

MUA OLANKHULIDWA ATAUKITSIDWA:

Mateyu 28:9,10,18-20

Mark16:15-18

Luka 24:17,19,25,26,36,38,39,41,44,46-49

Yohane 20:15-17,19,21-23,26,27; 21:5,6,10,12,19,22

Machitidwe 1:4,5,7,8

ULOSI

Yesu anaphunzitsaso zinthu zokhudza ulosi. Ulosi ndi mavumbulutso a zinthu zimene sizinachitike. Kapena kuti ndi uthenga ochokera kwa Mulungu okhudza tsogolo. Zina mwa zinthu zimene Yesu anaphunzitsa ndi izi:

KUBWERANSO KACHIWIRI KWA YESU:

Mateyu 24:6-47; 25:1-13; 26:64

Mark2:20; 8:38; 13:7-36; 14:62

YERUSALEMU:

Mateyu 5:34,35; 23:37-39; 24:2

Mark13:2

Luka 13:34,35; 19:42-44; 21:20-24; 23:28-31

Yohane 4:21

AYUDA:

Mateyu8:11,12; 10:6; 11:16-19; 15:24,26; 21:31,32; 22:2-7

Mark7:27

Luka 7:31-35; 21:24; 22:67,68

Yohane 4:22; 7:19,21; 8:37-47,49; 9:41; 10:26,32; 18:20,36

ALEMBI, AFARISI, NDI ASADUKI:

Mateyu 12:34; 15:7-9,14; 16:6; 23:2-7,13-15,25-27,29-36

Mark7:6; 8:15; 12:38-40

Luka 11:39,40-44,46-52; 12:1; 20:46,47

Yohane 5:42

AMITUNDU:

Mateyu 8:11; 21:43; 22:8-10; 24:14; 28:19

Marko13:10; 16:15

Luka 13:29; 24:46,47

Yohane 10:16

APHUNZITSI ONYENGA NDI CHIPHUNZITSIO CHAO CHONYENGA:

Mateyu 7:15-18,20; 24:4,5,11,23,24,26

Mark13:5,6,21,22

Luka 6:39,43,44; 17:1,2,22,23; 21:8

Yohane 10:1,8

TCHIMO:

Tanthauzo la Tchino lapafupi ndi: kusemphana ndi ndi Mulungu kapena kuti kumphany malamuro a Mulungu. Yesu anaphunzitsa zokhudza tchimo:

SATANA NDI TCHIMO:

Mateyu 4:10; 12:26,27; 13:19; 16:23; 25:41

Mark3:23,26; 4:15; 8:33

Luka 4:8; 10:18; 11:18,19; 22:31

Yohane 8:34-36; 14:30

KUNYOZA MULUNGU:

Mateyu 12:31,32; 15:19

Mark3:28,29; 7:21,22

Luka 12:10

KUKAIKIRA:

Mateyu 14:31; 17:17,20

Marko 2:8; 9:19; 16:16

Luka 9:41

Yohane 3:11,12,18; 4:48; 5:38,40,43-47; 6:64; 8:24,45-47; 12:47,48; 15:22,24

CHINYENGO:

Mateyu 6:2,16; 15:7,8; 23:13-15,25,27-29

Marko 7:6; 12:40

Luka 11:44; 12:1; 20:47

KUDZIKUZA:

Mateyu 23:5-7,12

Marko7:21,22; 12:38,39

Luka 11:43; 14:11; 20:46

MKWIYO:

Mateyu 5:22

KUMPHA:

Mateyu 5:21; 15:19; 19:17,18

Marko 7:21; 10:19

Luka 18:20

Yohane 8:44

CHIGOLORO, DAMA NDI CHIKHUMBITSO CHONYASA:

Mateyu 5:27,28,32; 15:19; 19:9,11,12,17,18

Marko 07:21,22; 10:11,12,19

Luka 16:18; 18:20

CHILEKANO:

Mateyu 5:31,32; 19:8,9

Marko 10:3,5,11,12

Luka 16:18

KUBA:

Mateyu 15:19; 19:17,18

Marko 7:21,22; 10:19

Luka 18:20

KUCHITIRA UMBONI WADODZA, CHINYENGO NDI BODZA:

Mateyu 15:19; 19:17,18

Marko 7:21,22; 10:19

Luka 18:20

Yohane 8:44

MAGANIZO OIPA, KUIPA MTIMA NDI KUPUSA:

Mateyu 6:23; 9:4; 15:19; 20:15

Marko 7:21,22

Luka 11:34

KUSILIRA:

Marko 7:21,22

Luka 12:15-21

CHISAWAWA NDI KUKHUMBA ZINTHU ZATHUPI:

Mateyu 6:19-21,24; 12:39; 13:3,22; 16:4; 24:38,39

Marko 4:3,7,18,19; 8:12

Luka 8:14; 9:60; 10:41,42; 11:29; 14:16-24; 16:1-9,13,15; 17:26-29; 21:34

Yohane 4:48; 6:27

CHIDODO:

Chidodo ndi kucedwa kuchita chinthu.

Mateyu 24:45-51

Luka 12:42-47; 13:25-28; 14:16-20

KUWERUZA:

Mateyu 7:1-5; 12:7

Mark4:24

Luka 6:37,41,42

Yohane 8:7,10,11,15

KUSAPENYA KWA MTIMA:

Mateyu 13:13-15; 15:14; 16:2,3

Mark4:12; 8:18,21

Luka 8:10; 12:54-56

KUGWA:

Kugwa kumatanthauza kusiya kutsata Yesu.

Mateyu 12:43-45

Luka 11:24-26

CHODETSA:

Chodetsa ndi chinthu chimene chimadetsa chinthu choyera Mateyu 7:6.

CHIDZUDZURO:

Mateyu 10:14,15; 11:22,23; 12:34,41,42; 13:13-15; 16:4; 18:7; 21:19; 23:13-15,25,27,29,33-36

Marko 6:11; 8:12; 11:14

Luka 6:24-26; 9:5; 10:10-15; 11:29,32,42,44,46,47,49-52

UNGWIRO

Yesu anagwiritsa ntchito nthawi yake yambiri pa dziko lapansi kuphunzitsa za ungwiro, mmene munthu angakhalire ndi ubale wabwino ndi Mulungu, ndi anthu ena komanso ndi iye mwini

KUITANIRA ANTHU KU UNGWIRO:

Mateyu 4:19; 8:22; 9:9; 14:29

Marko 1:17; 2:14; 4:24; 10:21; 19:21

Luka 5:27; 9:59,60; 18:22

Yohane 1:38,39,43; 12:26; 21:19

CHIKHULUPILIRO:

Mateyu 8:10,13,26; 9:22,28,29; 14:27; 15:18; 17:20; 21:22

Marko 4:40; 5:34,36; 6:50; 7:29; 9:23; 10:52; 11:22-24; 16:16-18

Luka 7:9,50; 8:25,48,50; 17:6,19; 18:8,42

Yohane 3:18; 6:20,29; 7:38; 9:35; 11:15,25,26,40,42; 14:1,12; 16:31; 20:27,29

CHIPULUMUTSO KUDZERA MWA CHIKHULUPILIRO:

Marko 16:16

Yohane 3:14-16,18; 5:24; 6:40,47; 11:25,26

KULAPA:

Mateyu 4:17; 21:28-32

Marko 1:15

Luka 13:2-5; 15:4-32

UBATIZO:

Mateyu 21:25; 28:19

Marko 11:30; 16:16

Luka 20:4

Yohane 3:5

Machitidwe 1:5

KUKONZEDWANSO MWATSOPANO:

Mateyu 9:16,17

Marko 2:21,22

Luka 5:36-39

Yohane 3:3,5-8,10

NTCHITO:

Mateyu 5:16; 7:16-27; 12:33; 13:3,4,8,23; 21:19

Marko 3:33-35; 4:3,4,8,20; 11:14

Luka 6:43,44,46-49; 10:30-37; 13:6-9

Yohane 7:17; 10:37,38; 15:8,16

LAMURO LALIKURU:

Mateyu 7:12; 22:37-40

Marko12:29-31

Luka 6:31

CHIKONDI:

Mateyu 5:43-47; 7:12

Luka 6:27,28,32-35

Yohane13:34,35; 14:23,24; 15:12,13,17

CHARITY NTCHITO ZA CHIFUNDO:

Mateyu 5:42; 6:1-4; 19:21

Mark10:21; 12:43,44

Luka 6:30,38; 11:41; 12:33,34; 14:12-14; 16:9; 18:22; 21:3,4

KUKHULULUKIRANA NDI KUYANJANA:

Mateyu 5:23-26; 6:14,15; 9:2,5,6; 16:18,19; 18:18,22-35

Mark2:5,9-11; 11:25,26

Luka 5:20,23,24; 6:37; 7:40-48; 12:58,59; 17:3,4; 23:34; 24:46,47

Yohane 20:23

CHIFUNDO:

Mateyu 5:7; 9:13; 18:15-17,27,33

Luka 6:36

KUDZIKANIZA NOKHA:

Mateyu 10:37-39; 16:24-26

Marko 8:34-37

Luka 9:23-25; 14:26,27-33; 17:33

Yohane 12:25

CHIYERO KOMANSO KUKHALA NDI MTIMA UMODZI:

Mateyu 5:8,27,28; 6:22-24; 9:4; 12:34,35; 15:10,11,16-20

Mark7:18-23; 10:15

Luka 4:12; 6:45; 11:34-36,41; 16:13; 18:17

KUSALANKHULA ZONYASA:

Mateyu 5:33-37; 12:36,37; 23:20-22

KUGONJETSJA THUPI:

Mateyu 5:29,30; 6:16-18; 17:21; 18:8,9

Mark9:29,43-49

KUMVERA NDI KUDZIPEREKA:

Mateyu 26:39,42; 28:19,20

Mark14:36

Luka 22:42

Yohane 7:17,18; 8:29,50; 14:15,21; 15:14; 18:11

KUMVERA MAULAMULIRO:

Mateyu 17:25-27; 22:19-21

Marko12:15-17

Luka20:24,25

KUKHULUPIRIKA NDI KUYANG'ANIRA:

Mateyu 24:42-47; 25:13; 26:41

Mark13:33-37; 14:38

Luka 12:35-40,42-44,47,48; 16:10-12; 21:36; 22:40,46

KUPILIRA NDI KUGWIRIRITSA:

Mateyu 5:13; 10:22; 13:3-9,18-23; 24:13

Mark4:3-9,13-20; 9:50; 13:13

Luka 9:62; 14:34,35

Yohane 8:31,32

KUDEKHA:

Luka 21:19

Machitidwe 1:7

KULUMBA MTIMA:

Mateyu 8:26; 14:27; 17:7

Mark4:40; 5:36; 6:50

Luka 8:50

Yohane 6:20

KUSALIMBANA NDI OTSUTSANA NAFE:

Mateyu 5:38-41,43-45; 26:52

Luka 6:27-30

KUDZICHEPETA NDI KUSALIRA ZAMBIRI:

Mateyu 5:3,5; 11:25,26; 18:3,4; 20:25-27; 23:8,11,12

Mark9:33,35; 10:15,42-44

Luka 9:48; 14:8-11; 18:14,17; 22:25-27

Yohane 13:7,8,10,12-17

KUDALIRA CHITHANDIZO CHA MULUNGU:

Mateyu 6:25-34

Luka 12:6,7,22,24-32

KUYAMIKA:

Mateyu 8:4

Mark1:44; 5:19

Luka 5:14; 7:40-48,50; 8:39; 17:17,18

KULOLERANA:

Mark9:39-41

Luka 9:50

UDINDO:

Luka 17:7-10

UNGWIRO:

Mateyu 5:48; 7:13,14; 19:21

Marko10:21

Luka6:40; 12:57; 13:24; 18:22

CHIPHUNZITSO CHAPAPHIRI:

Mateyu 5:3-12; 11:6; 13:16

Luka 6:20-23; 7:23; 10:23; 11:28

CHIPHUNZITSO CHAPADERA

Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri zimene zaikidwa pamodzi ngati chiphunzitso chapadera. Zina mwa zinthu zimenezi ndi izi:

CHIOMBOLO CHA MACHIMO ATHU:

Mateyu 17:12; 20:18,19,28; 26:24,31,39,42

Mark9:12; 10:33,34,45; 14:21,24,36

Luka9:22,56; 13:34,35; 18:31-33; 19:10; 21:28; 22:19,22,37,42; 24:26,44,46,47

Yohane 3:13-16,18; 5:39; 6:38-40,51; 8:24,28,56; 10:7,9-11,15-18,36; 11:25,26; 12:24,27,32,47;
13:7,8; 14:19; 15:13; 16:7,20,22,33; 17:1-4,19-21,23; 18:11; 19:30

I Akorinto11:24,25

UMODZI PANSI PA CHIPULUMUTSO:

Mateyu 20:1-15

PEMPERO:

Mateyu 6:5-13; 7:7-11; 18:19,20; 21:22; 26:41

Mark11:24; 14:38

Luka 11:2-13; 18:2-8,10-14; 22:40,46

Yohane 4:24; 14:13,14; 15:7; 16:23,24;

CHILAMURO NDI MZIMU:

Mateyu 15:3-8,10,11,16-20; 23:16-26,28

Mark7:6-8,14,15,18-23

Luka11:39,40,42,44

Yohane 6:63; 7:24

KUDZODZEDWA:

Mateyu 5:13; 20:23; 22:14; 24:22,31

Mark10:40; 13:20,27

Luka 18:7

Yohane 6:37,43-45,64,65; 15:16

KUYAMIKA:

Mateyu 10:32,33

Mark5:19; 8:38

Luka 8:39; 9:26; 12:8,9

UDINDO WA MUNTHU WINA ALIYENSE:

Mateyu 13:12; 22:11-13

Mark4:23-25

Luka 8:18; 12:47,48

Yohane 9:41

KUGWIRA NTCHITO NDI KUDZITUKULA WEKHA:

Mateyu 20:6; 25:14-30

Luka 19:12-26

SABATA:

Mateyu 12:3-5,8,11,12

Mark2:25-28; 3:4

Luka 6:3-5,9; 13:15,16; 14:3,5

UKWATI:

Mateyu 19:4-6; 22:30

Mark10:6-9; 12:25

Luka 20:34,35

ANA:

Mateyu 18:3-6,10,14; 19:14; 21:16

Mark9:37,42; 10:14,15

Luka9:48; 18:16,17

OSAUKA:

Mateyu11:5; 19:21; 26:11

Mark10:21; 14:7

Luka 4:18,21; 6:20; 14:13,14; 18:22

Yohane 12:8

OLEMERA:

Mateyu 19:23,24

Mark10:23-25

Luka 14:12; 16:19-31; 18:24,25

CHISONI:

Mateyu 5:4; 10:38; 11:28; 16:24; 23:38,39; 24:7,8; 26:38,39,42

Mark4:16,17; 8:34; 13:19; 14:34,36

Luka 6:21; 9:23; 14:27; 21:22-26; 22:42; 23:28-30; 24:38

Yohane 12:27; 14:1,27; 16:5,6,20-22; 18:11

MTENDERA NDI MPUMURO:

Mateyu 9:22; 10:13; 11:28-30; 26:45

Mark4:39; 5:34; 6:31; 9:50; 14:41

Luka 7:50; 8:48; 10:5,6,41,42; 12:29; 19:42; 24:36

Yohane 14:1,23,27; 16:33; 20:19,21,26

CHIMWEMWE:

Mateyu 5:11; 6:17; 9:2; 13:44; 14:27; 18:12,13; 25:21,23

Mark6:50

Luka 6:21-23; 10:20; 11:36; 15:4-10,32

Yohane 4:36; 8:56; 13:17; 15:11; 16:20-22,24; 17:13

MZERU:

Mateyu 7:24; 10:16; 11:15,25; 13:51; 15:16; 16:2,3; 21:16; 24:45-47

Mark4:12; 7:14,16; 8:17,18,21

Luka 6:47,48; 8:10; 10:21; 12:42-44,54-56; 16:1-8

Yohane8:12; 9:41; 12:46

IMFA NDI PARADIZO:

Mateyu 8:22; 9:24; 10:8,28; 16:28; 17:9,23; 22:32

Mark5:39; 9:1,31; 10:34; 12:25-27; 14:34

Luka 7:22; 9:27,60; 12:4,5,20; 16:31; 18:33; 20:35-38; 23:43; 24:46

Yohane 5:21,25,28,29; 6:39,40,49,58; 10:17,18; 11:4,14; 12:24; 15:13

MAU APADERA KWA ANTHU:

Gawo lomaliza la chiphunzitso cha Yesu ndi mau amene analankhula kwa anthu mwapadera nthawi imene anali kuphunzitsa pa dziko lapansi. Zina mwa zinthu zinthu zimenezi ndi izi.

NATANIELI:

Yohane1:47,48,50

MZIMAYI WAKU SAMARIYA:

Yohane 4:7,16-18

ZAKEYU WAMISONKHO:

Luka 19:5,9

AKHUNGU AKU YERIKO:

Mateyu 20:32

MAFUNSO KWA ALEMBI:

Mark9:16

ANA A ZEBEDAYO:

Mateyu 20:21-23

Mark10:36,38-40

ABALE AKE A YESU:

Yohane 7:6-8

MAFUNSO KWA ALEMBI:

Mark12:34

MARITA:

Luka 10:41,42

WANSEMBE WAMKULU NDI AKULU:

Mateyu 21:24,25,27

Mark11:29,30,33

Luka 20:3,4,8

OPHUNZIRA, A FARISI NDI A HERODI:

Mateyu 22:18

Luka 20:23

WANSEMBE WAMKULU:

Yohane 18:21

PILATO:

Yohane 18:34

CHAPUTALA 5

MPHUNZITSI AMACHOKERA KWA MULUNGU: NJIRA – GAWO 1

ZOLINGA:

pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kufotokoza mmene Yesu anagwiritsira ntchito njira zophunzitsa zili munsimuzi:

- Zozizwa
- Ulamuliro
- Chikondi ndi chifundo
- Kuchita maubale komanso kutengera.
- Kuchitapo kanthu.
- Kutuma anthu ena.
- Zinthu zomuzungulira.
- Zinthu zooneka ndi maso.
- Mfundo ya kuphunzira pang'onopang'ono.
- Kuika ophunzira mmagulu.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)

MAU OYAMBA

Mu chaputala chino tiphunzira mmene Yesu amaphunzitsira. Kapena kuti chaputala chimenechi chikhazikika pa njira zimene Yesu amagwiritsa ntchito pophunzitsa. Njira zakaphunzitsidwe ka Yesu ndi ndondomeko zimene Yesu amatsata pophunzitsa.

Nthawi zambira mpingo wakhala ukugwiritsa ntchito njira zachikunja pophunzitsa ndikuleka kugwiritsa ntchito njira zimene zimapezeka mu Baibulo. Njira zabwino zophunzitsa ndi zimene Yesu anagwiritsa ntchito ndipo zinali zopinduritsa. Chaputala ichi chikhazikika pa njira zimene zimayendera limodzi ndi chiphunzitsa cha Yesu makamaka kuphunzitsa ndi mau.

ZOZIZWA

Taona kale kuti uthenga wamphuzitsi ukuyenera kuyendera limodzi ndi chionetsero champhamvu ya Mulungu. Chionetsero cha mphamvu chimakopa anthu kuti amve mau a Mulungu:

Ndipo pofika dzuwa la Sabata, anayamba kuphunzitsa m'sunagoge; ndipo ambiri anamva Iye, nazizwa, nanena, Uyu adazitenga kuti izi? Nzeru yopatsidwa kwa munthuyu njotani, ndi zamphamvu zotere zocitidwa ndi manja ace? (Mark6:2) (werenganiso Mateyu 13:54)

Yesu amagwiritsa ntchito zozizwa ndi cholinga choti akonzekeretse anthu kuti alandire Uthenga Wabwino. Pa Yohane 9 pali nkhani ya kuchiritsidwa kwa munthu wakhungu kuyambira chibadwa chake. Ngati zotsatira za umboni wamachiritso ake, umboni wa mphamvu ya Mulungu unafarikira kwa anthu onse a mdera lake (8:9), atsogoleri achipembedzo ndi banja lake. Yesu anagwiritsa ntchito machiritso amenewa ndi cholinga chofuna kuphunzitsa Uthenga ochokera kwa Mulungu kwa atsogoleri achipembedzo.

Zozizwa za Yesu zimakumana ndi zosowa za anthu. Pamene mukhale mukuwerenga zambiriri zokhudza zozizwa za Yesu mu gawo la zoonjezera pophunzira, mupeza kuti zozizwa zimene Yesu anachita zinakumana ndi zosowa za anthu zamagawo osiyanasiyana monga kuthupi, maganizidwe a anthu, zauzimu ndi zina zambiri. Ziwanda zimachotsedwa, akufa amaukitsidwa, anjala amadyetsedwa ndipo iwo akufunikwa kumasuridwa amamasuridwa.

Palibe njira yabwino imene imaonetsera komanso kuchitira umboni za Uthenga wa Baibulo kuposa chionetsero cha mpamvu. Mpamvu ya Mulungu imakumana ndi zosowa za anthu komanso imasintha moyo. Ichi ndi chifukwa chake Yesu anapereka mphamvu Yake kwa ophunzira:

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; (Marko 6:7)

Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu10:7-8)

Woika lamulo ndi woweruza ndiye mmodzi, ndiye amene akhoza kupulumutsa ndi kuononga; koma iwe woweruza mnzako ndiwe yani? (Yakobo 4:12)

ULAMULIRO

Yesu amaphunzitsa ndi ulamuliro. Ulamuro umatanthauza kugwiritsa ntchito mphamvu kapena kulamulira. Chimodzimodzi ndi zozizwa, kuphunzitsa ndi ulamuliro kumakopa omvera:

Ndipo anazizwa ndi ciphunzitso cace; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi. (Marko1:22) (werenganinso Mateyu 21:23)

Mfundo zina zakaphunzitsidwe kamakono zimanena kuti mphunzitsi akuyenera kukhala ngati ophunzira osati kuphunzitsa ndi ulamuliro. Koma Yesu anaphunzitsa ndi ulamuliro. Ulamuliro wa Yesu uanaperekedwa ndi Mulungu ndipo Yesu anatipatsa Ife ulamuliro wauzimu.

Cifukwa cace Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu. (Yohane 20:21)

Yesu analonjeza ulamuliro ndi mphamvu kwa okhulupilira ndi cholinga choti ziwathandize kulakira uthenga wabwino komanso kuchitira umboni wa Uthenga Wabwino.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe1:8)

Maphunziro athu, kuthekera kwathu kwakuthupi komanso udindo wathu sizimene zimatipatsa ulamuliro pophuzitsa Baibulo. Ulamuliro wathu pophuzitsa umachokera kwa Yesu.

CHIKONDI NDI CHIFUNDO

Yesu sanaweruze anthu amene amawaphunzitsa. Koma iye amawonetsera chikondi ndi chifundo kwa anthu amenewa. Pamene mzimayi anagwidwa ndi chigololo, iye sanamuweruze ayi (Yohane 8:11). Pamene Mariya anagwiritsa ntchito zonunkhulitsa zamtengo odula, iye sanamuweruze kuti akuononga ndalama zimene anakatha kugwiritsa ntchito pothandiza anthu osauka. Iye anamvetsetsa zolinga za mzimayi amaneyu ndipo anamuonetsera chikondi mmalo momuweruza

Koma Yesu podziwa, anati kwa iwo, Mumbvutiranji mkaziyu? popeza andicitira Ine nthawi yabwino. Pakuti nthawi zonse muli nao aumphawi pamodzi nanu; koma simuli ndi Ine nthawi zonse. Pakuti mkaziyo, m'mene anathira mafuta awa pathupi panga, wandicitiratu ici pa kuikidwa kwanga. Indetu ndinena kwa inu, kumene kuli konse uthenga uwu wabwino udzalalikidwa m'dziko lonse lapansi, ici cimene mkaziyo anacitaci cidzakambidwanso cikumbukiro cace. (Mateyu 26:10-13).

Yesu anaonetsa chifundo pa munthu wakhungu(Mark10:46-62) komanso pa ana (Mark10:13-16) pamene ophunzira ake sanasamale za anthu amenewa. Yesu anaonetsa chikondi kwa mwini chuma wachichepere ngakhale kuti iye anasankha chuma mmalo motsata Iye(Mark10:17-22). Yesu anachiritsa khutu la msirikari amene anabwera kudzamumanga iye (Luka 22:50-51). Chifundo chimene anali nacho Yesu chimamupangitsa iye kuti apembedzera anthu amene amawatumikira. (Marko 6:34) ngakhale mizinda imene (Luka 19:41)

1 Akorinto 13 amaonetsera kuti utumiki ophunzitsa umakhala opanda pake ngati suchitika mwa chikondi. Mphuzitsi akuyenera kuonetsera chikondi komanso kukhudzika kwa ophunzira ndipo kupanda kutero zipamakhala popanda phindu.

KUCHITA UBWENZI NDI KUTENGERA CHITSANZO CHABWINO

Pamene Yesu anaitana ophunzira ake, Iye anali ndi cholinga chapadera:

Ndipo anaika khumi ndi awiri, kuti akhale ndi Iye, ndi kuti akawatume kulalikira, ndi kuti akhale nao ulamuliro wakuturutsa ziwanda. (Marko 3:14-15)

Choyamba ophunzira anaitanidwa kukhala ndi ndi Yesu ndi cholinga choti aphunzire kudzera moyo wachitsanzo wa Yesu. Chidziwitso chao chinakula kudzera mukukhala ndi Yesu ndipo kenako anayamba kuwafotokera kuti amavetsetse. Ophunzira a Yesu amayenera kutengapo mbali osati kungomvetsera chabe zimene amaphunzitsa. Iwo amayenera kuti awone zimene Yesu amachita kenako ndi kutengapo mbali pa utumiki. Yesu amakhala komanso kuonetsera zinthu zimene amaphunzitsa. Chitsanzo chake chakukhala zimene munthu akuphunzitsa ndi chitsanzo chabwino chimene munthu angatsate ngati njira yothandiza kuphunzitsa.

Yesu amaonetsera ophunzira ake mmene angagwiritsire ntchito zimene amaphunzitsa. Akafuna kuphunzitsa mphunziro lokhudza pempero, iye amapemphera. Ndipo akafuna kuphunzitsa kufunika kwa malemba iye amanena mau ochokera mu chipangano chakale. Pofuna kuonetsera kufunika kofaritsa uthenga Wabwino, iye amafaritsa Uthenga wabwino. Pofuna kufotokozera za mphamvu ya Mulungu iye amaonetsera mphamvuyo.

MAYANKHO

Kuchokera pa nthawi imene iye anauza ophunzira ake oyamba kuti amutsate, Iye nthawi zonse amafuna anthu kuti achitepo kanthu apa uthenga wake. Iye anauza amayi ndi abambo kuti asenze mtanda wao ndikutsata Iye (Marko 8:34-35). Iye anawatumiza kuti akachitire umboni kwa anthu apabanja pawo (Marko 5:19) komanso pakati apa atsogoleri achipembedzoa (Luka 5:14) Iye anauza anthu ena kuti agulitse zinthu zawo zonse (Marko 10:21). Pali malamuro ambiri amene Yesu anapereka kwa anthu.

Kuphunzitsa kumakhala kosakwanira ngati munthu sakhala muzimene zikuphunzitsidwazo. Kotero ndi zofunika kuti ophunzira achitepo kanthu pa zinthu zimene akuphunzira. Akuyenera kukhala anthu ochita mau osati kungakhala anthu odziwa kumva kokha.

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. Pakuti ngati munthu ali wakumva mau wosati wakucita, iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira nkhope yace ya cibadwidwe cace m'kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nacoka, naiwala pompaja nali wotani. Koma iye wakupenyereza m'lamulo langwiro, ndilo laufulu, natero cipenyereza, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakucita nchito, adzakhala wodala m'kucita kwace. (Yakobo 1:22-25)

Kukula moyo wauzimu sikumayesedwa malinga ndi zimene ophunzira wamva koma kumayesedwa malinga ndi zimene wamva ndi kuchitapo kanthu. Kotere kuti ndi zofunika kuphunzitsa kuti ophunzira asangodziwa zinthu koma akhala mu zinthu zimene aphunzitsidwa.

Ophunzira akuyeneradi kudziwa Mulungu osati kudziwa zinthu zokudza Mulunguyo. Kuphunzira kuli ndi gawo lakuchitapo kanthu osati kungomva chabe ayi. Yesu anaonetsera zinthu zimenezi mu utumiki wake.

TAONANI Teofilo inu, mau aja oyamba ndinakonza, za zonse Yesu anayamba kuzicita ndi kuziphunzitsa, (Machitidwe1:1)

Yesu anati:

Cifukwa cace yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu comweco, adzachulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakucita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzachulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:19)

Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kuti akuyenera kuphunzitsa komanso kuchitapo kanthu:

Ndipo atumwi anasonkhana kwa Yesu; namuza ziri zonse adazicita, ndi zonse adaziphunzitsa, (Marko 6:30)

Pakuyenera kukhala mwai kwa ophunzira kuti atengepo mbali pamene mukuphunzitsa. Muphunzira zambiri zokhudza izi mu chaputala 10. Koma izi sizikuyenera kungochitika ndi cholinga chofuna kusangalatsa ophunzira ayi. Izi zili chomwechi chifukwa Yesu anafotokoza kuti Uthenga wabwino uli ndi mtengo wake:

Ndipo anadziitanira khamulo la anthu pamodzi ndi ophunzira ace, nati kwa iwo, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace, nanditsate Ine. Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakataya moyo wace cifukwa ca Ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa. (Mark8:34-35)

KUTUMA

Kuchokera pachiyambi, Mulungu anapera udindo kwa anthu. Iye anapereka udindo kwa anthu kuti apereke maina kwa zinyama, amange chombo, chihema, kachisi, komanso khoma. Yesu nayenso anapereka ntchito kwa ophunzira ake. Iye amawauza ophunzira ake kuti adyetse gulu la anthu (Mateyu 14:16) Iye anatuma ophunzira ake kuti alalikire Uthenga Wabwino ndi kuchiritsa odwala (Mateyu 10:9-10). Iye amayembekezera ophunzira ake kuti abale zipatso zauzimu. (Yohane 15).

Yesu anawaokonzekeretsa ophunzira ake kuti atenge malo ake pamene Yesu anapita kumwamba. Pang'ono ndi pang'ono Yesu anayamba kupereka udindo ophunzitsa ndi kulalika. Mukuyenera kuphunzitsa ngati kuti mukukonzekeretsa anthu amene akudzatenga malo anu. Kuti mukonzekeretse ophunzira, mukuyenera kuwapatsa mwai ophunzira kuti aphunzitse mau a Mulungu.

ZINTHU ZOTIZUNGULIRA

Yesu amagwiritsa ntchito zinthu zakuthupi kapena zimene zamuzungulira kuti aphunzitse phunziro lauzimu. Yesu anapanga kuphunzira kukhala gawo la moyo wake kwa tsiku ndi tsiku. Iye amaphunzitsa anthu malo amene amakhala, kugwira ntchito. Chomwechonso, Mulungu akupitilira kuphunzitsa ife kudzera mu nyengo za moyo monga mavuto ndi zinthu zina za tsiku ndi tsiku. Iyi ndi njira imene Harvestime International imagwiritsa ntchito ndi chifukwa chake maphunziro amenewa mumachita malo amene mumakhala.

Yesu samadalira kukhala ndi zipinda zikuluzikulu zolowamo anthu kapena gome kuti aphunzitse ngati mmene tinaonera mu chaputala 2, Iye amagwiritsa ntchito mwai wina uli onse umene wakumana ndi munthu kuti aphunzitse. Ndipo amagwiritsa ntchito nyengo zamoyo kuti aphunzitse phunziro lina lake. Iye atakumana ndi anthu akupita kumanda anamudzutsa munthu wakufayu (Luka 7:11-15). Pamene iye anali ndi ludzu iye anapereka chitsanzo cha madzi amayo (Yohane 3), Iye ataona mzimayi osauka akupereka chopereka chake mkachisi, iye anaphunzitsa uthenga wa chopereka(Mark12:41-44).

Kumakhala kosavuta kuti anthu aphunzire pamene zinthu zimene zawazungulira zagwiritsidwa ntchito. Zinthu zimene anthu akueyenera kuphunzira zikuyenera kuyankha mavuto a anthu atsiku ndi tsiku. Uthenga ukuyenera kukumana ndi zosowa za anthu.

Zinthu zimene anthu akukumana nazo zimasiyana malingana ndi chikhalidwe cha anthu komanso zimatengera anthu amene akuphunzitsidwa. Ichi ndi chifukwa chake mukuyenera kumudziwa ophunzira wanu ndi cholinga choti mugwiritse ntchito mau a Mulungu. Muphunzira zambiri zokhudza izi mu mpunziro lotchedwa kuunikira anthu ophunzitsidwa komanso kukonzekera phunziro.

KUGWIRITSA NTCHITO ZINTHU ZOONEKA NDI MASO

Yesu anagwiritsa ntchito zinthu zooneka ndi maso. Chinthu chooneka ndi maso ndi chizindikiro, kapena chionetsero cha zinthu zimene zikuphunzitsidwazo. Mwachitsanzo, pamene yesu amafuna kuphunzitsa anthu khalidwe lokhala ngati la mwana kuti munthu akalowe ufumu wa Mulungu....

Ndipo anatenga kamwana, nakaika pakati pao, nakayangata, nanena nao, Munthu ali yense adzalandira kamodzi ka tiana totere cifukwa ca dzina langa, alandira ine; ndipo yense amene akalandira Ine, salandira Ine, koma Iye amene anandituma Ine. (Marko 9:36-37)

Pamene Yesu amafuna kufotokoza tanthauzo la imfa Yake, anagwiritsa ntchito vinyo ndi mkate(Marko14:22-25). Pamene Yesu amafuna kuphunzitsa phunziro la kudzichipetsa, anachapa mapazi a ophunzira ake (Yohane 13:1-17). Yesu anagwiritsa ntchito zinthu zooneka ndi maso monga maluwa (Mateyu 5:28) pofuna kuonetsera zinthu zimene amafuna ataphunzitsa. Chaputala 7 cha buku ili chikufotokoza zinthu zothandiza pophunzitsa komanso mmene mungazipezera zinthu zimenezi malingana ndi kupeza kwanu kwa ndalama. Koma ngakhale mutakhala kuti mulibe ndalama, mukhoza kugwiritsa ntchito zinthu zimene muli nazo pafupi kuti muphunzitse kapena kuonetsera zinthu zina zokhudza chiphunzitsosho. Yesu Khristu analibe chuma chogulira zinthu zothandiza pophunzitsa koma iye amagwiritsa ntchito zinthu zimene zinamuzungulira.

MFUNDO YOPHUNZIRA PANG'ONO PANG'ONO

Yesu anazindikira kuti ophunzira ake kuti sakanatha kuphunzira zinthu zambiri pakamodzi. Chifukwa cha ichi, Iye amaphunzitsa malinga ndi zimene iwo anakakwanitsa kumva:

**Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, 1 monga anakhoza kumva;
(Mark4:33)**

**Ndiri nazo zambirinso zakunena kwa inu, koma simungathe kuzisenza tsopano lino.
(Yohane 16:12)**

Ophunzira wina aliyense amakhala ndi mlingo wake omvetsetsa zinthu. Kuthekera kwa ophunzira kuti aphuzire zinthu kumakhudzidwa ndi zinthu zambiri. Muphunzira zambiri zokhudza izi mu Chaputala 8 chimene chikukamba za kusanthula anthu ophunzitsidwa.

KUIKA OPHUNZIRA M'MA GULU

Yesu amakonza chiphunzitso chake malinga ndi gulu la ophunzira limene akufuna kuphuzitsa.

GULU LA ANTHU LAMBIRI:

Pamene Yesu amaphuzitsa chigulu cha anthu, Iye samapereka mwai kuti alankhule kapena kufunsa mafunso pamapeto pa phunziro. Izi zimagwira ntchito bwino pamene mukuphunzitsa gulu la anthu ambiri. Nthawi zambiri pamene mukulalikira mumatsata ndondomeko imeneyi. Mwachitsanzo werengani Mateyu 5-7.

GULU LALING'ONO

Nthawi zambiri pamene Yesu amaphunzitsa gulu la anthu ochepa iye amalora anthu kuti atenge mbali. Mwachitsanzo, werengani Mark8:10-12: 14-21:27-30.

KUPHUNZITSA MUNTHU:

Yesu nthawi zambiri amagwiritsa ntchito njira yokambirani ndi anthu pofuna kuphunzitsa. Iye amafunsa mafunso pamene amalankhula ndi anthu. Njira imeneyi sikusiyana ndi kukambirana pakati pa anthu. Mwachitsanzo, werengani Yohane 3 ndi 4.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

Fotokozerani zinthu zimene mwaphunzira zokhudza mmene Yesu anagwiritsira njira zimenezi pophunzitsa.

2. Zozizwa

3. Ulamuliro

4. Chikondi ndi kukhudzika

5. kuchita ubwenzi ndi kutengera chitsanzo chabwino

6. Mayankho a anthu:

7. Kutuma:

8. Zinthu zomuzungulira:

9. Zinthu zooneka ndi maso.

10. Mfundo yophunzira pang'onopang'ono.

11. Kuika ophunzira magulu

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pitirizani kuphunzira zozizwa za Yesu zimene zinakumana ndi chosowa cha munthu.

ZOZIZWA ZOUKITSA AKUFA

Mwana yekhayo wa mzimayi wamasiye amane ananyamulidwa kupita kumanda Luka7:11-16

-mwana wa Yairo amene anali olamulira wa Sunagogi: Marko5:22-24, 35-43; Mateyu 9:18-26; Luka8:41,42,49-56

- Lazaro, anaukitsidwa patadutsa masiku anayi: Yohane 11:32-44

-Thupi lake lomwe linaukitsidw patadutsa masiku atatu: Luka 24:1-7; Yohane 19:42-20:14; Marko16:9-11

ZOZIZWA ZOTHAMANGITSA SATANA KAPENA ZIWANDA

-Munthu wa Mzimu onyansa: Marko1:23-26; Luka4:33-37

-wagwidwa ndi ziwanda osayankhula komanso wakhungu: 12:22-23; Marko3:19-30; Luka11:14-23

-Athu awiri ogwidwa ndi gulu la ziwanda: Mateyu 8:28-34; fananizani Luka8:26-39 and Marko5:1-20

Mzibambo osayankhula: Mateyu 9:32-35

-Kabuthu ka mzimayi waku Surofonika: Marko7:24-30; Mateyu 15:22-28

-Mnyamata odwala matenda okugwa amene ophunzira analephera: Mateyu 17:14-21; Mark9:14-39;

Luka 9:37-43

Ogwidwa ndi ziwanda osalankhula: Marko 9:14-26

ZOZIZWA ZA MACHIRITSO

-Mwana wa mdindo ogwidwa ndi manjenje: Yohane 4:46-54

-Mpongozi wa Petro: Marko1:29-31; Mateyu 8:14-17; Luka4:38-39

-Munthu wakhate: Marko1:40-45; Mateyu 8:2-4; Luka5:12-16

-Munthu obadwa ozerezeke: Marko 2:3-12; Mateyu 9:1-8; Luka5:17-26

-munthu olumala amene anakhala kwa zaka makumi awiri: Yohane 5:1-16

-Munthu wa dzanja lapuwara: Marko 3:1-5; Luka6:6-10; compare Mateyu 12:9-13

-Mzimayi amene anali kutaya mwazi kwa zaka zambiri: Marko5:25-34; Luka8:43-48; Mateyu 9:20-22

- akhungu ayamba kupenyanso: Mateyu 9:27-31

-munthu osamva ndi osalankhula achiritsidwa: Marko7:32-37

- Munthu osapenya ayambaso kuwona: Marko 8:22-26
- Mzimayi amene anali ozuzidwa kwa dzaka khumu ndi ndi zitatu: Luka13:11-17
- anthu khumi akugwa khunyu: Luka 17:11-19
- Munthu opempha apenyanso: Luka18:35-43; werenganinso Mateyu 20:29-34
- Batumeyo apenyanso: Marko 10:46-52; compare Mateyu 20:29-34

CHOZIZWA CHOTHANDIZA NTHAWI YOSOWA

- Madzi asandulika kukhala vinyo: Yohane 2:1-11
- Petro agwira nsomba zambiri: Luka5:1-11
- Yesu adyetsa anthu okwana 5000: Mateyu 14:15-21; Marko 6:35-44; Luka9:12-17; Yohane 6:5-14
- Yesu adyetsa anthu okwana 4000: Mateyu 15:32-39; Marko8:1-10
- Apeza ndalama munsomba: Mateyu 17:27
- Akola zomba zambiri: Yohane 21:6-14

ZOZIZWA ZA CHIWERUZO

- Nkhumba zithawira mmadzi: Mateyu 8:30-32
- Mtengo wamkhuyu uwuma: Mateyu 21:18-21; Marko11:12-14,20-24

ZOZIZWA ZOMASURIDWA

- Anadzilanditsa Yekha kwa adani ake: Luka 4:30
- Nyanja ndi mphepo zimamvera iye: Marko 4:37-41; Mateyu 8:23-27; Luka8:22-25
- Yesu apulumutsa Petro panyanja Mateyu 14:28-31; Marko 6:45-52

ZOZIZWA ZIMENE ANTHU ENA ANACHITA POCHIRIRA UMBONI ZA UMULUNGU WA YESU

- Anzeru akummawa atsogozedwa ndi nyenyezi: Mateyu 2:1-9
- Chizindikiro cha ubatizo: Mateyu 3:16-17; Marko1:9-12; Luka3:21-23
- Chizindikira pa nthawi yakusandulika kwake: Mateyu 17:1-14; Luka9:28-37; Marko 9:1-14
- Mayankho a mapemphero ake: Yohane 12:28-30
- zizindikiro za imfa yake: Mateyu 27:45-53
- zizindikiro za chiukitso chake: Mateyu 28:2; Marko16:4
- zizindikiro za kukwera kumwamba kwake: Marko16:19; Luka24:50-51; Machitidwe 1:6-12

2. Ngati mwamaliza ntchito imene yaperekedwa pamwambayi ndiye kuti mwaphunziira zozizwa zonse zimene Yesu anachita pamene anali kuphuzitsa. Tsono werengani Mabuku a Uthenga Wabwino wa Yohane, Marko, Luka ndi Mateyu ndipo werenganinso mfundo zimene Yesu amagwiritsa ntchito pophunzitsa. Lembani zimene mwapeza pa tchati chimene chili pansichi.

Ulamuliro: Chitsanzo mu...

Mateyu Marko Luka Yohane

Chokondi ndi chifundo: Chitsanzo mu...

Mateyu Marko Luka Yohane

Kukhala pamodzi ndi kutengera pa...

Mateyu Marko Luka Yohane

Kuchitapo kanthu: chitsanzo mu.

Mateyu Marko Luka Yohane

Kutuma anthu ena: Chitsanzo mu...

Mateyu Marko Luka Yohane

Kugwiritsa ntchito zinthu zooneka ndi maso: chitsanzo mu

Mateyu Marko Luka Yohane

Mfundo ya kuphunzira pang'onopang'ono: chitsanzo mu...

Mateyu Marko Luka Yohane

Kuika ophunzira mmagulu: Chitsanzo mu....

Mateyu Marko Luka Yohane

Munthu payenkhapayenkha:

Gulu la anthu ochepa

Gulu la anthu ambiri

CHAPUTALA 6

MPHUZITSI AMACHOKERA KUMWAMBA: NJIRA- GAWO II

ZOLINGA:

Pamapeto pa chaputala ichi mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokozerwa mwachidule mmene Yesu anagwiritsira ntchito njira izi pophunzitsa.
- Kuchoka pa zinthu zodziwika kufika pa zinthu zosadziwika.
- Kuchokera ku mfundo yaing'ono kufikira mfundo yaikulu.
- Chionetsero.
- Mafunso ndi mayankho
- Mafanizo
- Mbiri yapadera.
- Kugwiritsa ntchito malemba
- Kusiyanyitsa zinthu.
- Mavuto.
- Nyengo

VEZI YOTSOGOLERA

Ndipo pofika ku dziko la kwao, anaphunzitsa iwo m'sunagoge mwao, kotero kuti anazizwa, nanena, Uyu adazitengakuti nzeru zimenezi ndi zamphamvu izi? (Mateyu13:54)

MAU OYAMBA

Nthawi zambiri Yesu amaphunzitsa kugwiritsa ntchito mau. Pali nthawi imodzi yokha imene Yesu analemba uthenga wake. (Yohane 8:6) chaputala ichi chikhazikika pa njira yophunzitsa ndi mau imene Yesu amagwiritsa ntchito.

KUCHOKA PA ZINTHU ZODZIWIKA KUFIKA PA ZINTHU ZOSADZIWIKA.

Yesu amagwiritsa ntchito zinthu zodziwika kuti aphunzitse zinthu zimene anthu samadziwa. Amagwiritsa ntchito zinthu zakale kuti kuti aphunzitse zinthu zatsopano. Iye amayamba ndi zinthu zimene anthu amazidziwa kale ndi kuonjezera kuti aphunzitse mfundo zimene anthu samadziwa.

Mwachitsanzo, Yesu nthawi zambiri amafotokozerwa mfundo yochokera ku Chilamuro cha Chipangano Chakale kuti awonetsera mfundo yatsopano (Werengani Mateyu 5:17-48)

Cholinga chophunzitsa ndi chakuti anthu amvetse. Mukuyenera kuonetsera choonadi kuchokera ku zimene ophunzira akudziwa kale. Ndi zofunika kuti anthu akuyenera kumvetsa uthenga paokha ndi maganizo awo chifukwa.

Pakuti monga asinkha m'kati mwace, ali wotere; Ati kwa iwe, Idya numwe; Koma mtima wace suli pa iwe. (Miyambo 23:7)

KUCHOKA PA MFUNDO YAING'ONO KUPITA PA MFUNDO YAIKULU.

Chidziwitso cha Mulungu ndi mavumbulutso amakhala akukulabe. Mulungu amayamba ndi mfundo yaing'ono ndikupita ku mfundo yaikulu. Mwachitsanzo, mfundo yaing'ono ya ulosi wa kubwera kwa mpulumutsi inaperekedwa Genesis 3:15. Koma pakudutsa pa nthawi, Mulungu kudzera mwa aneneri analosera zambiri zokhudza kubweranso kwa mneneri.

Pa Yohane 6:35 Yesu anaonetsera mfundo yaing'ono kuti Iye ndi mkate wa moyo. Pamene pa Yohane 6:51-58, Yesu onaonjezera zambiri zokhudza mfundo imeneyi. Iye anafotozera zambiri za thupi lake ngati mkate wamoyo umene uyenera kudyedwa kuti anthu akhale ndi moyo.

CHIONETSERO

Yesu amagwiritsa ntchito zinthu wamba komanso zizindikiro zimene anthu amazidziwa ndi cholinga chofuna kuphunzitsa choonadi cha Baibulo. Iye anagwiritsa ntchito chitsanzo cha maluwa komanso mbalame pofuna kuphunzitsa za chisamaliro cha Mulungu (Mateyu 6:26-30). Iye anagwiritsa ntchito kusodza ndi kukolora ndi cholinga chofuna kuphunzitsa kufunika kwa antchito kuti akafikire anthu osapululumutsidwa. (Yohane 4:35) ndi Mateyu 4:19)

Yesu anagwiritsa ntchito mkate onyemedwa ngati chizindikiro cha thupi lake komanso vinyo ngati chizindikiro cha mwazi wake. (Luka 22:19-20). Anagwiritsa ntchito kuchapa mapazi a ophunzira ake ndi cholinga chofuna kuonetsera kutumikirana wina ndi mzake komanso kudzichepetsa (Yohane 13:1-17) Yesu anaitana mwana wang'ono pofuna kuonetsera kudzichipetsa komansochikhulupiliro choyenera kuti munthu alowe Ufumu wa Mulungu. (Marko 10:13-36). Iye anagwiritsa ntchito zizindikiro zambiri pofuna kuonetsera Ufumu wa Mulungu. Zina mwa zitsanzo zimene ndi fanizo la njera/mbeu, tirigu, chotupitsa ndi zina zambiri.

Pamene tagwiritsa ntchito chifaniziro, ndi zofunika kwambiri kuti tigwiritse ntchito chifaniziro chimene ophunzira akuchidziwa bwino lomwe.

MAFUNSO NDI MAYANKHO

Yesu amagwiritsa ntchito mafunso ndi mayankho pophunzitsa. Nthawi zambiri Yesu amafunsa mafunso ndi cholinga choti ophunzira ake aganize. Nthawi zina akafunsa fuso amafuna kuti ayankidwe. (Mateyu 16:13-16) Pamene nthawi zina Yesu amafunsa mafunso amene amakhala opanda mayankho. Mafunso amenewa cholinga chake chinali chongowapangitsa kuti aganize komanso kuti anthuwo apange maganizo awo. (Luka 10:25-37; Marko 10:17-18).

Nthawi zina mafunso amene amafunso amakhala kuti ndi vuto loti anthu aliganizire (Mateyu 21:25-27). Nthawi zina amatha kufunsa mafunso ndi cholinga chakuti awapangitse anthu akuti ayambapo kuganiza (Mateyu 5:13) Koma nthawi zina iye akacheza ndi anthu amakhala kuti akungofunsa mafunso okhaokha (Mateyu 16:9-12). Nthawi zambiri Yesu amayankha mafunso amene afunsidwa pofunsaso funso linzake (Mateyu 9:14-15; 12:10-11; 15:1-3; 21:23-25).

Yesu anagwiritsa ntchito mafunso mosiyanasiyana. Mukhoza kugwiritsa ntchito mafunso mu njira zili munsimuzi.

-Kupereka chiyambi chaphunziro: Mateyu 21:28

-kupitiriza phunziro: Mateyu 21:40

-pofuna kubwereza zimene anthu amadziwa kale: Marko 2:25-26

-pofuna kukhudza mkati mwaophunzira: Mateyu 23:17

-pofuna kubweretsa chikhulupiriro: Marko 8:29

-Pofuna kuonetsera chinachake: Marko 10:3

-Pofuna kudzudzula: Marko 2:25-26

-Pofuna kukopa anthu kuti aganize kwambiri: Mateyu 6:25-31

-Pofuna kuunikira maganizo osiyasiyana: Mateyu 9:5

-Pofuna kuwamvetsa ophunzira: Mateyu 16:15

Mphuzitsi akhoza:

- Kufunsa mafunso kwa ophunzira onse
- Kufunsa funso kwa ophunzira mmodzi
- Kufunsa funso limodzi pakamodzi. Mukafusa mafunso ambiri pakamodzi zimakhala zosokoneza.
- Pamene mwafunsa funso mukuyenera kukhala chete. Mudikire kuti mwanayo ayankhe kaye funsolo.
- Funsani funso laling'ono kenako funsani funso lalikulu.
- Mukuyenera kuyankha mafunso ochokera kwa ophunzira. Mukuyenera kukhambirana mayankho amene aparekedwa. Simukuyenera kunyoza ophunzira amene sanyanke moyenera.
- Simukuyeners kufunsa mafunso amene ophunzira okhoza kungoyanka kuti eya kapena ayi. Mafunso amenewa samalimbikitsa ophunzira kuti awerenge. Chitsanzo cha mafunso ongoyankha kuti eya kapena ayi ndi awa.

“Kodi Yesu anafera pamtanda”

Koma funso limeneli likufuna kufotokozerwa osati kungoti eya kapena ayi. Kufunsa ophunzira kuti afotokozerwa zimathandiza kuti iwo aganizire kufunika kwa imfa ya Yesu. Ndipo iwo akhoza kuyankha ndi mayankho ambiri. Ena Mwa mayankho amenewa ndi awa:

- Chifukwa chinali cholinga chimene Mulungu anamutumizira.
- Chifukwa chachikondi chake pa dziko lapansi.
- Kuti apulumutse dziko lapansi kumachimo.
- Ndi cholinga chakuti tikachilitsidwe komanso kupulumutsidwa.
- Chifukwa cha machimo anga

Yankho lina lilironse limene laperekedwa likhoza kubweretsa zokambirana zambiri zokhudza imfa Ya Yesu pamtanda paja.

Mu gawo la zoonjezera pophunzira liri ndi mafunso okhudza Yesu Khristu komanso mmene mungagwiritsire ntchito mafunso amenewa mmoyo wanu.

MAFANIZO

Fanizo ndi nkhani imene imagwiritsa ntchito chitsanzo chakuthupi pofuna kuonetsera choonadi chazimu. Tanthauzo lenileni la fanizo ndi kufananitsa. Mu mafanizo a Yesu, iye amagwiritsa ntchito nkhani ya dziko lapansi imene imakhala ndi tanthauzo lakumwamba.

Nthawi zambiri Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo pamene amaphunzitsa:

Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, 1 monga anakhoza kumva; (Marko 4:33)

Fanizo likuyenera kufotokozeredwa kuti limvetsetseke:

ndipo sanalankhula nao wopanda fanizo: koma m'tseri anatanthauzira zonse kwa ophunzira ace. (Marko 4:34)

Nthawi ina ophunzira a Yesu anafunso chifukwa chimene iye amaphunzitsira mu mafanizo ndipo iye anayankha.

Ndipo iye anati, Kwapatsidwa kwa inu kuzindikira zinsinsi za Ufumu wa Mulungu; koma kwa ena otsala ndinena nao mwa mafanizo; kuti pakuona sangaone, ndi pakumva sangadziwitse, (Luka 8:10)

Anthu amene ali ndi maganizo auzimu amatha kumvetsa mafanizo auzimu. Ndipo anthu amaganizo akuthupi sangathe kumvetsa mafanizo.

Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (I Akorinto 2:14)

Munthu amene ali ndi maganizo auzimu ndi amene anabadwa mwatsopano. Werengani Yohane 3 kuti mupeze tanthauzo la kubadwa mwatsopano.

Mafanizo a Yesu amakhala pa zinthu zimene anthu amazidziwa. Pamene mukuphunzitsa, mukhoza kugwiritsa ntchito mafanizo a Yesu komanso mukhoza kugwiritsa ntchito mafanizo amakono kwa ophunzira anu.

Chifukwa chakuti chikhalidwe chimasiyana, mafanizo amene anthu aku America angamvetsetse si mafanizo amene anthu ena akhoza kumvetsa. Anthu alionse ayenera kukhala ndi mafanizo amene amagwirizana ndi chikhalidwe chao. Kuti muphunzire zambiri, werengani gawo la zoonjezera pophunzira.

NKHANI

Ngati mafanizo, nkhani za Baibulo zimaonetsera choondani cha Baibulo koma nkhani za Baibulo zimakhala nkhani zenizeni zimene zinachitika. Mwachitsanzo, nkhani ya Lazaro ndi nkhani imene inachitikadi mu mbiri. Lazaro ndi mwini chuma analidi anthu enieni.

Mukhoza kugwiritsa ntchito nkhani pofuna kuphunzitsa. Werengani gawo la zoonjezera pophunzira kuti muone nkhani zimene Yesu anagwiritsa ntchito pophunzitsa. Mukhoza kugwiritsanso ntchito nkhani zamakono. Gwiritsani ntchito nkhani za atsogoleri a masiku ano kuti muonetsere choodi cha Mulungu.

KUGWIRITSA NTC MHTO MALEMBA

Mu nthawi imene Yesu anatumikira pa dziko lapansi, panali Chipangano Chakale chokha kotere kuti malemba amene Yesu amagwiritsa ntchito mu utumiki wake anali chipangano Chakale. Chigawo cha zoonjezera pophunzira muona malemba amene Yesu anagwiritsa kuchokera mu Chipangano Chakale.

Ndi zofunika kuti mugwiritse ntchito mau a Mulungu pamene mukhuphunzitsa chifukwa ndi mau a Mulungu amane amakwaniritsa cholinga chazimu.

momwemo adzakhala mau anga amene aturuka m'kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira. (Yesaya 55:11)

KUSIYANITSA

Nthawi zambiri Yesu amagwiritsa ntchito kusiyantsa pamene amaphunzitsa. Kusiyantsa kumakhalapo pamene pali chinthu zosiyana ndi chimzake. Mwachitsanzo, Yesu amasiyantsa kuwala ndi ndi mdima, chabwino ndi choipa, komanso osauka ndi olemera ndi cholinga chofuna kuonetsera choonadi.

Kusiyantsa kukhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kuphunzitsa kusiyana kwa zinthu pazimu. Mukhoza kugwiritsa ntchito kusiyantsa kumene Yesu anagwiritsa ntchito kapena mukhoza kupeza zitsanzo zina zosiyantsa.

MAVUTO

Yesu amagwiritsa ntchito mavuto a tsiku ndi tsiku pofuna kuphunzitsa. Nthawi zambiri kuganiza kwenikweni kumabwera pamene pali mavuto. Mwachitsanzo alembi amadabwa amene anali ndi mphamvu zokhululukira machimo (Marko 2:7).

Yesua amagwiritsa ntchito mavuto ngati amenewa.

NYENGO

Yesu amagwiritsa ntchito nyengo za moyo pofuna kuphunzitsa phunziro linalake. Iye anagwiritsa ntchito nyengo yake imene anakumana ndi mzimayi pa chitsime cha madzi kuti aphunzitse phunziro la mmadzi amoyo. (Yohane 4). Pamene Yesu anadzuzuridwa chifukwa chakudya ndi Afarisi, iye anagwiritsa ntchito chidzuzuro chimenechi pofuna kuphunzitsa fanizo la angongole awiri. (Luka 7:36-50)

Werengani zambiri mu gawo la zoonjezera pophunzira kuti muone zina mwa nyengo zimene Yesu anagwiritsa ntchito pofuna kuphunzitsa.

MAYESA ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

Fotokozerani mwachidule njira izi zophunzitsira.

2. Kuchoka mfundo yodziwika kupita ku mfundo yosadziwika

3. Mfundo yaing'ono kupita ku mfundo yaikulu

4. Chionetsero

5. Mafunso ndi mayankho

6. Mafanizo

7. Nkhani

8. Kugwiritsa ntchito malemba

9. Kusiyanitsa

10. Mavuto

10. Nyengo

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Zinthu zili munsimuzi zikuthandizani kuti mupitirize kuphunzire zinthu zimene takambirana

KUCHOKERA YODZIWIKA KUPITA MFUNDO YOSADZIWIKA

Werengani ndime zili munsimuzi zimene Yesu anagwiritsa ntchito njira imeneyi:

Mateyu: 5:17-48; 12:3-8,38-42; 16:5-12

Marko: 2:23-28; 7:9-13; 8:17-21; 10:17-20

Luka: 4:16-21; 6:3-5; 11:29-32; 13:1-5,15-16; 24:44-48

Yohane: 3:14-15; 5:33-36,46-47; 6:32-33; 7:21-24; 8:39-59; 10:34-38

KUCHOKERA MFUNDO YAING'ONO KUPITA MFUNDO YAIKULU

Chitsanzo chimodzi cha njira imeneyi chikupezeka pa Yohane 6:35. Yesu anafotokozera za mfundo yaikulu ya imfa yake pamtanda. Koma iye akufotokozera mfundo zina zokhudza imfa yomweyi pa Yohane 6:35-58. Mu buku la Mateyu Yesu akufotokozera pang'ono chabe za imfa yake (Mateyu: 18:31-34 koma iwo sanamvetsetse. Koma iye anafotokozera zambiri pa Mateyu 18:31-34 ndipo pamene anawafotokozera izi anamvetsetsa (Mateyu 22:15-23)

Kodi mukhoza kupeza chitsanzo cha mmene Yesu anagwiritsira ntchito njira imeneyi yophunzitsirayi?

CHIONETSERO

Gwiritsani ntchito ndime zili munsimuzi zimene Yesu anagwiritsa ntchito chionetsero kapena chizindikiro pofuna kuphunzitsa choonadi chazimu. Pangani tchatu kuti muonetsero chooodi chazimu chimene chikuphunzitsidwa

Mateyu: kuwedza 4:19; mchere 5:13; kuunika 5:14-16; mbalame 6:26; maluwa 6:28-33;

7:1-5; chipata 7:13-14; nkhoa ndi nkhandwe 7:15; chipatso 7:16-20; nyumba ziwiri 7:24-27;

8:20; zovala ndi vinyo 9:16-17; kholora 9:37-38; nkhoa ndi nkhadwe 10:16; mpheta 10:29-31; gori 11:28-30; njere ndi mafuta 13:1-43; chuma 13:44,52; ukonde 13:47-50; mbeu

15:10-14; nyengi 16:1-4; child 18:1-6; khoswe 18:12-14; ngamira ndi singano 19:23-26; mtengo wamkuyu 21:18-22; mwala 21:42-44; mkate ndi vinyo 26:26-29 Marko: nsomba 1:16-18; njere ndi nthaka 4; mkate ndi agalu 8:25-30; mtchere 9:50; children 10:13-16; ngamira ndi singano 10:23-27; penny 12:13-17;

Yohane: mphepo 3:8; madzi 4:13-14, 7:37-38; Kukolora 4:35; kuwala 8:12, 9:5, 12:46; shepherd 10; chimanga ndi tirigu 12:23-24; fines and branches 15; mzimayi akubereka 16:19-21; nkhoa zikudya 21:15-17; kutsuka mapazi 13:1-17

MAFUNSO NDI MAYANKHO

Werengani ndime zili munsimuzi zimene zikuonetsera pamene Yesu anagwiritsa ntchito mafunso ndi mayankho pofuna kuphunzitsa:

Mateyu: 5:13,46,47; 6:25-31; 7:3,4,9-11,16,22; 8:26; 9:4,5,15,28; 10:25,29; 11:7-9,16;

12:4,5,11,12,26,27,29,34,48; 13:27,28,51; 14:31; 15:13,16,17,34; 16:3,8-11,13,15,26; 17:17,25;
 18:12,33; 19:5,17; 20:6,13,15,21,22,32; 21:16,25,28,31,40,42; 22:12,18,22,
 31,32,42-45; 23:17,19,33; 24:2,45; 25:37-39,44; 26:10,40,50,53-55; 27:46
Marko: 2:8,9,19,25,26; 3:4,23,33; 4:13,21,30,40; 5:30,39; 6:38; 7:18,19; 8:5,12,17-
 21,27,29,36,37; 9:16,19,21,33,50; 10:3,18,36,38,51; 11:3,17,30; 12:9-11,15,16,24,26,35,37;
 13:2; 14:6,14,37,48; 15:34
Luka: 2:49; 5:22,23; 6:4,9,32-34,39,41,42,46; 7:24-26,31,42,44; 8:25,30,44; 9:18,20,25,41;
 10:26,36; 11:5,6,11-13,18,19,40; 12:6,14,17,20,24-26,28,42,49,51,56,57; 13:2,4,7,15,16,18,20;
 14:3,5,28,31,34;15:4,8;16:2,3,5,7,11,12;17:7-9,17;8:7,8,19,41;19:31;
 20:3,4,13,15,17,23,24,41,44; 22:11,27,35,46,48,52; 23:31; 24:17,19,26,38,41
Yohane: 1:38,50; 2:4; 3:10,12; 5:6,44,47; 6:5,61,62,67,70; 7:19,23; 8:10,43,46; 9:35;
 10:32,34,36; 11:9,26,34,40; 12:27; 13:12,38; 14:9,10; 16:5,19,31; 18:4,7,11,23,34; 20:15;
 21:5,15-17,22,23

MAFANIZO

| Mutu | ndime |
|--------------------------------|---|
| Nyumba ziwiri | Mateyu7:24-27; Luka 6:47-49 |
| Ana pa msika | Mateyu11:16; Luka 7:32 |
| Angongore awiri | Luka 7:41 |
| Mzimu onyansa | Mateyu12:43-45; Luka 11:24-26 |
| Malingaliro a Munthu olemelera | Luka 12:16 |
| Mtengo wamkuyu osabara | Luka 13:6-9 |
| Ofesa mbeu | Mateyu13:3-8; Marko 4:3-8; Luka 8:5-8 |
| Nansongore | Mateyu13:24-30 |
| Mbeu | Marko 4:26 |
| Mbeu ya Mpiru | Mateyu13:31,32; Mark. 4:31,32; Luka 13:19 |
| Chotupitsa | Mateyu13:33; Luka 13:21 |
| Nyali | Mateyu5:15; Marko 4:21; Luka 8:16; 11:33 |
| Ukonde | Mateyu13:47,48 |
| Chuma chibisika | Mateyu13:44 |
| Ngare ya mtengo wapatali | Mateyu13:45,46 |
| Mwini nyumba | Mateyu13:52 |
| Ukwati | Mateyu9:15; Marko 2:19,20; Luka 5:34,35 |
| Chovala cha zigamba | Mateyu9:16; Marko 2:21; Luka 5:36 |

| | | |
|--------------------------|-------|-----------------------------------|
| Mabotolo a vinyo | | Mateyu9:17; Marko 2:22; Luka 5:37 |
| Kholora | | Mateyu9:37; Luka 10:2 |
| Adani | | Mateyu5:25; Luka 12:58 |
| Angongore awiri | | Mateyu18:23-35 |
| Msamariya wachifundo | | Luka 10:30-37 |
| Mikate itatu | | Luka 11:5-8 |
| M'busa wabwino | | Yohane 10:1-16 |
| Chipata choongoka | | Mateyu7:14; Luka 13:24 |
| Mlendo | | Luka 14:7-11 |
| Mphwando la ukwati | | Mateyu22:2-9; Luka 14:16-23 |
| Chovala cha kuukwati | | Mateyu22:10-14 |
| Nsanja | | Luka 14:28-30 |
| Mfumu ikupita kunkhondo | | Luka 14:31 |
| Mutu | ndime | |
| Nkhosa yotaika | | Mateyu 18:12,13; Luka 15:4-7 |
| Ndalama yotaika | | Luka 15:8,9 |
| Mwana olowelera | | Luka 15:11-32 |
| Wantchito osakhulupirika | | Luka 16:1-9 |
| Mzimayi wamasiye | | Luka 18:2-5 |
| Wansonkho ndi mfarisi | | Luka 18:10-14 |
| Antchito mmunda | | Mateyu 20:1-16 |
| Ma talenti | | Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27 |
| Ana amuna awiri | | Mateyu 21:28 |
| Mtengo wamkuyu | | Mateyu 24:32; Marko 13:28; |
| Munthu wapaulendo | | Marko 13:34 |
| Khalidwe la anthu awiri | | Mateyu 24:45-51; Luka 12:42-46 |
| Anamwari nkhumu | | Mateyu 25:1-12 |
| Mpesa ndi mitengo yake | | Yohane 15:1-6 |

Pangani mafanizo amakono:

1. Sankhani choonadi cha Baibulo chimene mukufuna kuphuzitsa.
2. Ganizirani za nyengo kapena chitsanzo chimene ophunzira atha kumvetsetsa.
3. Pogwiritsa chitsanzo chimene mwapeza, pangani fanizo limene lionetsera choonadi chimene mukufuna kuphuzitsa.

NKHANI ZA M'BAIBULO

NKHANI

Yohane M'batizi
Lazaro ndi mwini chuma

NDIME

Mateyu 11:7-19; Luka 7:24-25
Luka 16:19-31

Tsopano mukhoza kupeka nkhani zanu ndi cholinga chofuna kuonetsera choonadi cha Baibulo. Mwachitsanzo ngati mukudziwa munthu amene anamulandira yesu atatsala pang'ono kufa kapena pangozi mukhoza kugwiritsa ntchito chitsanzo cha munthu ameneyu kuti mupeke nkhani.

Kodi ndi zinthu ziti zimene mwadutsamo zimene zikuonetsera choonadi cha Baibulo. Mukhoza kufotokoza umboni wamoyo wanu kapena nkhani ya atsogoleri amphamvu am'bado uno pofuna kufotokozerana nkhani ya choonadi cha Mulungu.

KUGWIRITSA NTCHITO MALEMBA

Werengani malemba onse mmene Yesu anagwiritsa ntchito mu chiphunzitsi chake.

Chipangano Chakale

Mateyu4:4:
Mateyu4:7:
Mateyu4:10:
Mateyu5:21:
Mateyu5:27:
Mateyu5:31:
Mateyu5:33:
Mateyu5:38:
Mateyu5:43:
Mateyu9:13, 12:7:
Mateyu11:10:
Mateyu13:14,15:
Mateyu15:4:
Mateyu15:4:
Mateyu15:8,9:
Mateyu19:4:
Mateyu19:5:
Mateyu19:18,19:
Mateyu21:16:
Mateyu21:42:
Mateyu21:13:
Mateyu22:32:
Mateyu22:37:
Mateyu22:39:
Mateyu22:44:
Mateyu26:31:
Mateyu27:46:
Luka 22:37:

Chipangano Chakale
Nyengo Imene Zinagwiritsidwa Ntchito
Deteronome 8:3
Deteronome 6:16
Deteronome 6:13
Eksodo 20:13; Deteronome 5:17
Eksodo 20:14; Deteronome 5:18
Deteronome 24:1,3
Levitiko 19:12; Numbers 30:2, Deteronome 23:21
Eksodo 21:24; Leviticus 24:20; Deteronome 19:21
Leviticus 19:18
Hoseya 6:6
Malachi 3:1
Yesaya 6:9,10
Eksodo 20:12; Deteronome 5:16
Eksodo 21:17; Leviticus 20:9
Yesaya 29:13
Genesis 1:27, 5:2
Genesis 2:24
Eksodo 20:12-16; Deteronome 5:16-20
Masalimo 8:2
Masalimo 118:22
Yesaya 56:7; Jeremiah 7:11
Eksodo 3:6
Deteronome 6:5
Leviticus 19:18
Masalimo 110:1
Zekariya 13:7
Masalimo 22:1
Yesaya 53:12

| | |
|---------------|----------------------|
| Luka 23:46: | Masalimo 31:5 |
| Luka 4:18: | Yesaya 61:1,2 |
| Yohane 10:34: | Masalimo 82:6 |
| Yohane 13:18: | Masalimo 41:9 |
| Yohane 15:25: | Masalimo 35:19, 69:4 |

KUSIYANITSA

Werengani ndime zili munsimuzi zimene Yesu Khristu anagwiritsa ntchito kusiyanita zinthu pophunzitsa.

Mateyu:

Chaputala 5- 7 Chiphuzitso chapaphiri.

| | |
|-------------|---|
| 9:12 | waphumphu ndi odwala |
| 9:13 | wangwiro ndi ochimwa |
| 9:16 | chovala chakale ndi chatsopano |
| 9:17 | Vinyo wakale ndi watsopano |
| 10:26 | Zobisika ndi zoululika. |
| 10:27 | Mdimba ndi kuwala |
| 10:28 | Thupi ndi Mzimu |
| 10:32-33 | kuvomereza ndi kukana |
| 10:34 | mtendere ndi lupanga |
| 12:33 | Mtengo wabwino/ Mtengo oipa |
| 12:35 | Munthu wabwino/Munthu oipa |
| 12:37 | Mau oweruza/ Mau alungamitsa |
| 13:12 | amene alinazo ndi amene alibe |
| 13:13 | akupenanya ndi iwo osapenya |
| 13:30 | Tirigu ndi Nansongore |
| 13:47-50 | Chabwino ndi choipa |
| 15:25 k | utaya moyo ndi kupulumutsa Moyo |
| 18:23-35 | onse okhulukiridwa ndi osakhulukiridwa |
| 16:19-18:18 | Kumanga ndi kumasula |
| 19:30 | Oyamba ndi otsiriza |
| 20:16 | Oitanidwa ndi osankhidwa |
| 20:25-28 | Mtumiki ndi Kapolo |
| 21:28-30 | Mwana ogwira ntchito ndi mwana osagwira ntchito |
| 21:42 | Mwala okanidwa ndi mwala wapangodya |
| 23:11 | Wamkulu ndi otumikira |
| 23:12 | Okwezedwa ndi otsitsidwa |
| 24:40-41 | Otengedwa ndi Osiyidwa |
| 25:1-4 | Anamwari opusa ndi anamwari ochenjera |
| 25:29 | anapereka ndi osapereka |

Marko:

| | |
|---------|-----------------------------------|
| 2:17 | Ochimwa ndi wangwiro |
| 2:19-20 | Iwo amene amasala ndi iwo osasala |

2:21 Chovala chakale ndi chatsopano
 2:22 Vinyo wakale ndi watsopano
 2:27 Sabata kupangidwira munthu munthu kupangiridwa Sabata
 3:4 Kupanga chabwino kapena choipa pa Sabata
 2:4 Nthaka yabwino ndi nthaka yoipa.
 4:12 Kuona ndi kumva /kusaona komanso kusamva
 4:22 Zinthu zibisika ndi zinthu zovumbuluka
 4:25 Watenga/ wapereka
 4:31-32 Mbeu yachabe ndi mbeu yabwino
 4:40 Mantha/ chikhulupiriro
 7:6-13 chikhalide/ chiphunzitso cha Baibulo
 7:14-15 Mkati/ Kunja
 8:33 Zinthu za Mulungu/ zinthu za anthu
 8:35 kupulumutsa moyo/ kutaya moyo
 9:40 Otsutsana nafe/ ali ndi ife
 9:50 Mtchere wabwino ndi Mchere Oipa.
 10:43-44 Wamkulu ndi wang'ono
 11:27-33 Ubatizo wa Yohane / Ubatizo wa anthu
 12:17 Kaisala kapena Mulungu.
 12:27 Mulungu wa anthu akufa ndi amoyo
 12:44 Giving from abundance/giving from want
 14:38 Mzimu/ Thupi
Luke:
 5:31 waphumphu/ odwala
 5:32 wangi/ ochimwa
 5:36 Chovala chatsopano/ Chovala chakale
 5:37-38 Chovala chakale/ Chovala chatsopano
 Kusiyanitsa kwambiri kukupezeka pa chaputala
 7:20-21 Yohane M'batizi/ Yesu Khristu
 7:47 Kukonda kwambiri/ kukonda pang'ono
 9:24 Kukhala ndi Moyo/kutaya Moyo
 9:48 Ochepe/ Wamkulu
 9:56 Kuononga/ Kupulumutsa
 Mmene mungachitire mumizinda imene mwalandiridw ndi kumene zimunalandiridwe.
 11:23 Ndi iye/ kutsutsana naye
 11:34 diso limodzi/ diso loipa
 11:35 kuwala ndi mdima
 11:39 kuyera kunja/ kuda mkati
 12:2-3 zobisa/ zoululika
 12:8-9 kuvomereza/ kukana
 12:47-48 mawanga ochepe/ mawanga ambiri
 12:51 Mtendere/ kugawikana
 13:9 Chipatso chabwino/ chipatsi choipa
 13:30 oyamba ndi otsiriza
 14:8-11 okwezedwa ndi otsitsidwa
 14:12-14 olemera ndi osauka

14:30 kuyamba koma osamaliza zinthu
 14:34-35 Mchere/ mchere koma osakoma
 15:4-10 otaika/ opezeka
 15:11-32 Mwana wabwino/ mwana oipa
 16:10-12 okhulupirika pang'ono ndi okhulupirika kwambiri
 16:13 olamulira awiri
 16:19-20 munthu wachuma/ opanda chuma
 17:33 kufuna moyo ndi kutaya moyo
 17:34-36 otengedwa komanso otsala
 18:10-14 kusiyanita anthu awiri akupemphera
 19:12-27 kusiyanita mmene anthu amagwiritsira ntchito luso lawo.
 19:46 Nyumba ya mapemphero ndi nyumba ya akuba.
 20:17-18 mwala wapangodya/ mwala okanidwa.
 20:38 Mulungu wa anthu amoyo/ Mulungu wa anthu akufa
 21:1-4 Mphatso za achuma, mphatso za osauka
 22:25-30 wamkulu/ wang'ono
 23:31 Mtengo wamoyo/ mtengo okufa

Yohane:

3:6 obadwa mwathupi/ Obadwa mwa mzimu
 3:12 Zinthu zapadziko/ zakumwamba
 3:17 kudzapulumutsa osati kuweruza
 3:19-21 Kuwala/ mdi
 4:13-14 madzi amoyo/madzi athupi
 5:24 Imfa ndi moyo
 5:29 chabwino/ chiukitso
 6:32-33 Mkate wa Mose/ Mkate wa Mulungu
 6:63 Mzimu/ Thupi
 7:18 Ulemelero wathu/ Ulemelero wa Mulungu
 7:24 Chiweruzo chiwiri
 8:12 Kuwala/ Mdimba
 8:23 Wadziko lapansi/ okhala wadziko lapansi
 8:35 Otumikira/ Mwana wa Munthu
 8:47 wakumva/ osamva
 9:39 Khungu/ kupenya
 10:1-18 M'busa wabwino/ mbala
 10:25-29 Nkhosa zanga/ nkhosa zina
 12:24-35 Kupulumutsa moyo/ kutaya moyo
 12:35-36,46 kuwala/ mdima
 12:47 chiweruzo/ chipurumutso
 13:16 Mtumiki / Mbuye
 14:12 Ntchito/ Ntchito zazikulu
 14:23-24 Kusunga/ kusasunga
 14:27 Mtendere wa Mulungu/ Mtendere wa dziko lapansi
 15:2 kubala zipatso/ kusabala zipatso
 15:15 Otumikira/ Abale
 15:19 Wadzika lapansi/ osakhala wadziko lapansi

16:20-22 Chisono kusandulika chimwemwe
 20:27 Opanda chikhulupiriro/ achikhulupiliro
 20:29 iwo amene amaona ndi kukhulupirira/ iwo amene amaona koma osakhulupirira
 21:18 Kusi yana pakati pa Petro pamene ali wachichepere ndi pamene anali atakula.

MAVUTO

Werengani ndime zili munsimu zimene Yesu anagwiritsaa ntchito mavuto mu chiphunzitso chake.

Munthu

mavuto

| | |
|--|---|
| Alembi(Marko2:7) | Kodi oyenera kukhululira tchimo ndi ndani? |
| Alembi ndi Afarisi (Marko 2:18) Iwo” (Marko 2:18) | Ubwenzi wa Yesu ndi amisonkho ndi ochimwa Pamene ophunzira sanasale chakudya |
| Afarisi (Marko 2:24) | Kusunga Sabata |
| Alembi (Marko 3:22) | mmene Yesu amachotsera Yesu ziwanda |
| Anthu a kwao komwe (Marko 6:2,3) | Gwero la mphamvu zake |
| Afarisi (Marko 8:11) | Imafuna chizindikiro |
| Petro, Yakobo ndi Yohane (Marko 9:11) | Kubwera kwa Eliya |
| Ophunzira (Marko 9:34) | Kodi wamkulu mndani? |

Munthu

Mavuto awo

| | |
|--|-----------------------------------|
| Yohane ndi anthu ena (Marko 9: 38) | kulorena ndi anthu ena |
| Afarisi (Marko10:2) | Chilekanitso |
| Mwini chuma wachichepere (Marko10:17) | kulowa mu ufumu wa Mulungu |
| Yakobo ndi Yohane (Marko 10: 37) | kukhala pa dzanja lamanja la Yesu |
| Wansembe wamkulu, alembi, ndi akulu (Marko 12:14) | Ulamuliro wa Yesu Khristu |
| Asaduki (Marko 12:23) | Chiukitso |
| Yakobo, Petro, ndi Andrey (Marko 13:4) | “Kodi zidzakhala liti” |

NYENGO

Werengani nyengo zimene Yesu anagwiritsa ntchito pofuna kuphuzitsa

| Nyengo | Kugwiritsa ntchito kwakwake | Ndime |
|--|---|--|
| Amalonda mu kachitsi | Kuyeretsa kachitsi | Mateyu 21:12-13; Marko11:15-17 |
| Nikodemo abwera kwa Yesu | Chiphuzitso cha kubadwa mwatsopano | Yohane 3:1-21 |
| Kukumana ndi mzimayi waku Samaria | Kusintho moyo wa munthu | Yohane 4:1-42 |
| Akhate abwera kwa Yesu | Kuyeretsa Thupi | Mateyu 8:1-4; Marko1:40-45; Luka 5:12-14 |
| Abweretsa munthu opuwala | Machiritso akuthupi ndi auzimu | Mateyu 8:5-13; Luka 7:1- |
| Mzibambo pa thamanda la Betasaida | Machiritso kuthupi | Yohane 5:1-9 |
| Afaris awiringula ndi kutola tirigu kwa ophunzira pa tsiku la Sabata | Chiphuzitso chenicheni cha ubale wa munthu ndi Sabata | Mateyu 12:1-8; Marko2:23-28; Luka 6:1-5 |
| Chikhamu cha anthu | Chiphuzitso chapaphiri | Mateyu 5 to 7 |
| Kubwera kwa amayi ake ndi abale ake | Chiphuzitso cha | Mateyu 12:46-50 Marko3:31-35; Luka 8:19-21 |
| Kudya ndi simoni amene anali wamisonkho | Angongore awiri | Luka 7:41 |
| Ophunzira afunsa chifukwa chimene alankhulira mu mafanizo | Chiphuzitso chokhudza chisinsi cha Ufumu wa Mulungu | Mateyu 13:10-17 |
| Ophuzira afusa tanthauzo la fanizo la tirigu ndi nansongore | Chiphuzitso chokhudza ana a oipa | Mateyu 13:36-43 |
| Chifukwa chimene amadyera ndi amisonko | Chiphuzitso chokhudza odwala komanso agwiro | Mateyu 13:36-43 |

CHAPUTALA 7

ZOTHANDIZIRA POPHUNZITSA

ZOLINGA

Pamapeto pa izi mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokoza tanthauzo la zothandizira pophonzira.
- Kufotokoza tanthauzo la zothandizira zomvera ndi zooneka.
- Kufotokoza kufunika kwa zothandizira zooneka ndi zomvera pophonzitsa.
- Kukonza zothandizira zomvera ndi zooneka.
- Kuunikira zinthu zothandiza pophonzitsa.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo anatenga kamwana, nakaika pakati pao, nakayangata, nanena nao, Munthu ali yense adzalandira kamodzi ka tiana totere cifukwa ca dzina langa, alandira ine; ndipo yense amene akalandira Ine, salandira Ine, koma Iye amene anandituma Ine. (Marko 9:36-37)

MAU OYAMBA

Mu chaputala ichi, muphonzira kagwiritsidwe ntchito ka njira zosiyanasiyana zophonzitsira. Mwina simungathe kukhala ndi mwai ogwiritsa ntchito njira zonsezi chifukwa cha malo amene muli kapena chifukwa cha ndalama. Chifukwa chakuti maphunziro a Harvestime International amaperekedwa madera ambiri, chaputala chimenechi chifotokozerabe njira zimene sizimagwira ntchito madera ena. Pali maganizo ena othandiza amene aperekedwa opezera njira zothandiza pophonzira zimene sizimafuna ndalama.

ZINTHU ZOTHANDIZA POPHUNZITSA

Zothandiza pophonzira ndi zinthu zimene zimathandiza munthu kuti aphunzitse. Ichi ndi chifukwa chake zimatchedwa zothandizira. Zothandizira zikhoza kukhala zochitika pophonzira kapena ntchito imene ophonzira amapatsidwa kuti achite ndi cholinga choti anonetsere choonadi cha Baibulo. Zothandizira pophonzitsa chikhoza kukhala chinthu chimene chikhoza kuoneka ndi maso, kugwiridwa kapena kuchimva kumene. Zinthu zimene zimatchedwa “Audio Visual”.

Mau oti audio amatanthauza kuti kumva. Pamene mau oti visual amatanthauza zithu zimene zimaoneka. Pemene mau oti audi- visual amatanthauza kapena kuimira chinthu chimene mungathe kumva ndi kuchiona.

Koma nthawi zina zothandizira pophonzira zimatha kukhala zongomvera zokha. Zina mwa zinthu ngati zimenezi ndi ma kaseti. Palinso zinthu zina zimene zimangokhala zongoona zokha zimene zikhoza kukhala zinthu ngati zithuzi.

KUFUNIKA KWA ZOTHANDIZA POPHUNZIRA

Zothandizira pophonzira ndi zofunika chifukwa chakuti kuona ndi kumva ndi njira zodalirika pophonzira. Kafukufuku wapadera anaonetsa kuti timakumbukira:

- Zinthu 10 pa 100 zimene timamva
- Zinthu 50 pa 100 zimene taona.
- Zinthu 70 pa 100 pa zimene tapanga.
- Zinthu 90 pa 100 zimene taona, kumva ndi kuchita.

Chifukwa cha ichi ndi zofunika kuti tiphatikize njira zophunzitsira.

MITUNDU YA ZOTHANDIZIRA POPHUNZITSIRA

Zina mwa zinthu zothandiza kuphonzitsa ndi izi:

ZINTHU ZOPEZEKA KWAMBIRI

Mukhoza kugwiritsa ntchito zinthu zopezeka pafupi kapena kwambiri malo amene akuzungulirani. Yesu anagwiritsa ntchito zinthu ngati maluwa, mbalame, nsomba ndi ana ndi cholinga chofuna kuonetsera kapena kutsindika chiphonzitso chake.

ZOWONEKA:

Zina mwa zinthu zimenezi ndi zithunzi, nyuzipepa, mabuku ndi zina zaambiri.

Zithuzi zakanema:

Zina mwa zinthu zinthu zimenezi ndi ma kaseti a Vidiyo kapena kuti DVD.

ZOMVERA

Zina mwa zinthu zimene mungathe kugwiritsa ntchito pophonzitsa ndi zomvera ndi makaseti, ma CD, ndi zinthu zina zomvera

ZIDA ZOTHANDIZ KUPANGA KAFUKUFUKU WA BAIBULO

Mukuyenera kulimbikitsa ophonzira anu kuti agwiritse ntchito zinthu zothandiza kuchita kafukufuku wa Baibulo. Zina mwa zinthu zimenezi ndi monga nthanthauzira mau ndi ma buku ena. Muphonzira zambiri zokhudza phunziro limene mukuphonzitsa ngati mungatsate njira zochitira kafukufuku wa Baibulo.

KUGWIRITSA NTCHITO MAKINA A COMPUTA

Pali zinthu zambiri zimene mukhoza kuziika pa makina a computa amene mukhoza kupezamo mapu komanso nyimbo.

NTCHITO

Perekani ntchito kwa ophonzira anu kuti zimene aphonzira zikhazikike. Mukhoza kuwauza kuti ajambule mapu kapena chifaniziro cha chinthu chinachake cha Chipangano Chakale. mukhoza

kuwauza kuti achite ntchito ya utumiki monga kutumikira anthu amene samudziwa Mulungu, Kuyendera odwala, kudyetsa anjala. Ntchito imathandiza ophunzira kuti achite mau osati kungokhala akumva okha.

MAPU

Mapu amathandiza ophunzira kuti amvetse malo amene nkhani za m'baibulo zinachitikira. Mukhoza kuwauza ophunzira kuti awone mapu kapena kuti ajambule mapu ogwirizana ndi phunziro limene mukuphunzitsa.

ULENDO OKAPHUNZIRA

Kupanga ulendo okaphunzira ndi njira yabwino yophunzilira. Ophunziro akhoza kupanga ulendo okayendera nyumba yosunga mbiri mbiri, kundende ndi cholinga choti aphunzire.

MA TCHATI NDI MA GALAFU.

Pangani ma galafu ndi matchati ndi cholinga choti awonetsere mphunziro limene aphunzira. Ma galafu akhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kusiyanyisa zinthu.

SEWERO:

Ophunzira okhoza kuchita sewero ngati njira imodzi yofuna kuonetsera zimene aphunzira. Kuti izi zichitike, ophunzira amaonetsera za anthu osiyanyisana amene akupezeka mu nkhani.

ZIDOLE:

Mukhoza kugwiritsa ntchito zidole kuti muonetsere nkhani za Baibulo. Zidole ndi ndi tianthu ting'onoting'ono timene timagwiritsidwa ntchito pofuna kuchita sewero.

BOLODI:

Bolodi ndi malo amene amapakidwa utoto wakuda ndipo amagwiritsidwa ntchito polemba mkalasi komanso ndi kufufuta. Aphunzitsi akhoza kugwiritsa ntchito bolodi kuti alembepo mfundo zokhudza phunziro. Komanso bolodi ikhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kujambula zithunzi zophunzitsira. Chimodzimodzinso ophunzira okhoza kugwiritsa ntchito bolodi ngati kuti aphunzire.

MAKAKA:

Makaka ndi pepala limene limalembedwa ndikugwiridwa mmanja. Mwachitsanzo aphunzitsi akhoza kugwiritsa ntchito makaka kuti alembepo vesi komanso ndime imene vesi ikupezeka.

NYIMBO:

Nyimbo zikhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kuphunzitsa. Mukhoza kugwiritsa ntchito nyimbo

- Imene ikugwirizana ndi phunziro limene mwaphunzitsa.
- Nyimbo imene ukuitanira anthu kuti alandire uthenga Wabwino pamene mwaphunzitsa Uthenga Wabwino.

- Imene ikugwirizana ndi mzimu wa phunziro limene mwaphunzitsa. mukhoza kuimba nyimbo yachimwemwe, yachisoni kapena yopembedzera.

MAUMBONI:

Maumboni ochokera kwa ophunzira kapena kwa mlendo okhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kuonetsera phunziro limene mwaphunzitsa. Mwachitsanzo ngati mukuphuzinitsa zokhudza mamasuridwe, mukhoza kuitana munthu kuti achitire umboni zokhudza mamasuridwe.

KULOWEZA ZINTHU PAMTIMA:

Mukhoza kuloweza zinthu ngati ma vesi, nkhani. Izi zimathandiza kuti ophunzira kuti akumbukire zimene aphunzira zokhudza Baibulo.

MAYESO:

Ophunzira akhoza kuyesedwa ndi mayeso ndipo izi zimathandiza kuti zimene aphunzira zikhazikike. Mayeso amenewa akhoza kukhala olemba kapena apakamwa. Ndipo pamene mayeso alembedwa, mukuyenera kukonzetsa mafunso amene ophunzira sanachite bwino.

KUKAMBA NKHANI

Pamene mukuphunzitsa ana, awuzeni anawo kuti afotokoze nkhani imene mwawaphunzitsa malingana ndi mmene iwo ayimvera. Ndipo mukhoza kuuza ophunzira akulu kuti afotokozere mwachidule zimene aphunzira.

MAPEZEDWE A ZOTHANDIZIRA POPHUNZITSA

Mukhoza kupanga nokha zambiri zothandizira pophunzitsira. Pamene zina mwa zinthu zimenezi mukhoza kugula. Koma ngati mulibe ndalama, mukhoza kupanga zina mwa zinthu zimenezi pogwiritsa ntchito zinthu zimene zakuzungulirani. Mukhoza kubwerekanso zothandizira pophunzira zimene ndi zomvera monga ma kaseti kapena ma DVD.

KUUNIKIRA ZOTHANDIZA POPHUNZIRA.

Gwiritsani ntchito ndondomeko zimene zalembedwa pansipa kuti muunikire zothandizira pophunzira:

1. Kodi zothandizira pophunzirazo zikugwirizana bwanji ndi phunzirolo? Kodi zikuthandiza kuti phunziro limveke bwino?
2. Kodi zikugwirizana ndi nsinkhu wa anthu amene mukuwaphunzitsa?
3. Kodi mtengo wa zothandizira pophunzirazo ndi woyenera?
4. Kodi zikuthandiza bwanji pokwaniritsa zolinga zaphunziro lanu?
5. Kodi ndi zosavuta kumvetsa?

Kumbukirani kuti zothandizira pophunzira ndi zongothandizira basi. Paizo zokha sizingagwire ntchito. Tikuyenera kudalira mau a Mulungu amene amabwera kudzera mwa Mzimu Woyera kuti agwire ntchito ya Mulungu.

Mlimi wabwino amagwiritsa ntchito zipangizo zabwino kuti adzale mbeu. Komabe iye amadziwa kuti ndi mbeu imene wadzala osati zida zimene amagwiritsa ntchito zimene zimabweleretsa kholora labwino.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi zothandiza pophonzira ndi chiani?

3. Kodi zothandiza pophonzira za Audio-Visual ndi chiani?

4. Kodi kufunika kwa Audio- Visula Aid ndi chiani?

5. Kodi ndi mtundu wanji wa Visual imene Yesu amagwiritsa ntchito?

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pangani zothandizira pophunzira za Audio- Visual kuti muphunzitsire
2. Unikirani zothandizira pophunzira zimene mwapanga.
 1. Kodi chothandizira pophunzirazo zikugwirizana bwanji ndi phunzirolo? Kodi zikuthandiza kuti phunziro limveke bwino?
 2. Kodi zikugwirizana ndi nsinkhu wa anthu amene mukuwaphunzitsa?
 3. Kodi mtengo wa zothandizira pophunzirazo ndi woyenera?
 4. Kodi zikuthandiza bwanji pokwaniritsa zolinga zaphunziro lanu?
 5. Kodi ndi zosavuta kumvetsa?

CHAPUTALA 8

KUUNIKIRA OPHUZIRA ANU

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokoza tanthauzo la kuunikira ophunzira.
- Kufotokoza kufunika kounikira ophunzira.
- Fotokoza mwachidule ndondomeko za kusanthula ophunzira.
- Kufotokoza makhalidwe a magulu anthu osiyanasiyana?

VESI YOTSOGOLERA

Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa iye anadziwa anthu onse, ndipo sanasowa wina acite umboni za munthu; pakuti anadziwa iye yekha cimene cinali mwa munthu. (Yohane 2:24-25)

MAU OYAMBA

Musanayambe kuphunzitsa ndi zofunika kuti muunikire anthu amene mukufuna kuphunzitsa. Mukuyenera kukhazikitsa zolinga ndi dongosolo limene mutsate pophunzitsa. Cholinga cha phunziro limeneli ndi kufuna kufotokoza mmene mungaunikire ophunzira anu. Pamene machaputala awiri apatsogolo cholinga chao ndi kufotokoza mmene mungakhazikitsire zolinga za phunziro komanso dondosolo la phunziro lanu.

KUUNIKIRA OPHUNZIRA

Ophunzira ndi gulu la anthu amene mumaphunzitsa. Pamene kuunikira ndi kusanthula kanthu mwatsatanetsatane. Pamene tikakamba za kuunikira ophunzira timathanthauza kusanthula makhalidwe a gulu limene mukukonzekera kuti muphunzitse.

KUFUNIKA KOUNIKIRA OPHUNZIRA

Kuunikira ophunzira ndi kofunika kwambiri chifukwa kuphunzira kumakhudzika ndi zinthu zambiri. Zina mwa zinthu zimenezi ndi chilankhulo, maphunzira a anthu, chikhalidwe, kuthekera kwa kuthupi komanso kukhwima muuzimu.

Ngati simuunikira anthu amene mukuwaphunzitsa ndi zikhoza kutheka kuti mukhoza kuwaphunzitsa zinthu zimene ndi zoposa nsinkhu wawo kapena zochepera maphunziro ame ali nao ngakhale zochepera kapena kudutsa kukhwima kwa moyo wao wauzimu. Ndi zosatheka kugwiritsa ntchito chilankhulo chimene iwo samamvetsetsa. Kapena zikhoza kukhala zovuta kuti kuphunziro kuchitike ngati maphunziro siogwirizana ndi mlingo umene anthu ali ku magawo a chuma ndi madera ena ambiri.

Ndi zosatheka kudziwa chinachilichonse chokhudza anthu amene mukuwaphunzitsa. Koma mukhoza kuganizira zimene ophunzira anu ambiri ali. Komanso pemphani Mzimu Woyera akuthandizeni kuti mukumane ndi zosowa za anthuwo.

Yesu amavetsetsa anthu amene amawaphunzitsa. Iye amadziwa chikhalidwe ndi miyambo ya anthu chifukwa anali mbali imodzi ya anthu amene amawaphunzitsa. Koma Yesu analinso ndi chidziwitso chauzimu cha zosowa za anthu.

Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa iye anadziwa anthu onse, ndipo sanasowa wina acite umboni za munthu; pakuti anadziwa iye yekha cimene cinali mwa munthu. (Yohane 2:24-25)

Mulungu akhoza kukuonetserani za anthu amene mukufuna kuwaophunzitsa, koma mukhoza kupeza njira zina zowadziwira anthu. Mtumwi Paulo anachitapo izi.

Koma pozindikira Paulo kuti ena ndi Asaduki, ndi ena Afarisi, anapfuula m'bwalomo, Amuna, abale, ine ndine Mfarisi, mwana wa Afarisi: andinenera mlandu wa ciyembekezo ndi kuuka kwa akufa. (Machitidwe 23:6)

Pamene Paulo amatumikira kwa Ayuda, Iye amatsindika kwambiri za mbiri yake ngati Muyuda. Pamene akakhala kuti akulankula ndi anthu ena monga a Chiroma, iye amasintha kachitidwe kake ka zinthu. Paulo amadziwa kufunika kosanthula anthu amene amawaphunzitsa ndipo iye amachita izi polankhula mu chilankhulo chimene iwo amadziwa komanso amagwiritsa ntchito njira zimene anthuwo amatha kuzizindikira mosavuta.

Ndipo m'mene anafuna kumupha iye, wina anamuuzza kapita wamkuru wa gululo kuti m'Yerusalemumonse muli pinngu-piringu, (Machitidwe 21:39 ndi 22:2)

Zina mwa ndondomeko zimene mungatsate kuti muunikire ophunzira anu ndi izi”

1. Pempherani kwa Mulungu kuti akuwululireni zosowa zakuthupi ndi zauzimu za anthu amene mukufuna muwatumikire.

Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye, (Yakobo 1:5)

2. Timauzidwa kuti tikuyenera kusilira mphatso zabwino zauzimu (I Akorinto 12:31) ndipo pemphani Mulungu kuti akupatsane mphatso yauzimu ya mau a luntha kapena kuti mphatso ya mzeru ndi chidziwitso. Mphatso zimene zimathandiza kuti mukhale ndi chidziwitsa cha anthu makamaka mavuto awo. Mphatso ya kuzindikira mizimu ndi yothandizanso. Kutu mudziwe zinthu zambira zokhudza mphatso zauzimu, werengani phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera”
3. Khalirani limodzi ndi ophunzira komanso yang'anitsitsani zimene iwo amachita. Mukhoza kuphunzira zambiri powona zimene iwo amachita komanso pokhala nawo limodzi ophunzira anu. Werengani mauthenga abwino ndipo onani mmene yesu

anawonenelera khalidwe la ophunzira ake ndipo santhulani mmene izi zimakhudzira kaphunzitsikdwe kake ka ophunzira.

4. Ngati mukutumikira mu dziko limene ndi losiyana ndi dziko lakwanu, phunzirani zinthu zambiri zokhudza anthuwo zimene mungakwanitse pofusa mafunso, kuwerenga mabuku okhudza chikhalidwe cha anthuwo komanso poyang'ana zimene anthuwo amachita.
5. Ngati mukutumikira ana, ndi kofunika kuti mudziwe makolo awo. Funsani makolo zosowa za ana awo ndipo gwirani nawo ntchito limodzi makolo anawo kuti mukwaniritse zosowa za anawo.
6. Ngati zili zotheke yenderani makomo a ophunzira anu chifukwa muphunzira zambiri pakuona malo amene amakhala.
7. Gwiritsani ndondomeko zothandiza kuunikira ophunzira zimene zaperedwa mu phunziro ili.

NDONDOMEKO ZOTHANDIZA KUUNIKIRA OPHUNZIRA

Gwiritsani ntchito ndondomeko zili musimuzi kuti musanthule ophunzira anu:

CHILANKHULO:

Ophunzira akuyenera kumvetsa chilankhulo chimene chikugwiritsidwa ntchito pophunzira. Kupanda kutero zimafuna kukhala ndi munthu omasulira.

KUUNIKIRA OPHUNZIRA ANU:

- Kodi amalankhula chilankulo chimene mulankhula
- Kodi mugulu la ophunziralo muli anthu ena amene samalankhula chilankhulo chimene chikugwiritsaidwa ntchito? Ngati zili choncho ndiye kuti mukufunika kuti mupeze omasulira.

MAPHUNZIRO

Mlingo wa maphunziro umene akuperekedwa ukuyenera kufanana ndi maphunziro a anthu amene mukuwaphunzitsa. Ophunzira ena amakhala kuti anaphunzira sukulu ya primary ndi sekondala yonse pemene ena amakhala kuti sanaphunzire kufikira mlingo umeneu. Pamene ophunzira ena amakhala achangu kumva ndipo sizimawatengera nthawi kuti amvetsetse.

KUUNIKIRA OPHUNZIRA ANU:

Kodi ndi mlingo uti umene ophunzira anu ambiri anasiyira? Kodi amadziwa kulemba ndi kuwerenga? Nanga anafika ku secondary, primary kapena ku college?

CHIKHALIDWE

Chikhalidwe chimakhudza mmene munthu amaphunzilira. Mphuzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zitsanzo zimene ndi zodziwika bwino muchikhalidwe cha anthu. Chikhalidwe

chimakhuza mmene timaonera ndi kumvera zinthu. Nthawi zambiri anthu amaphunzira bwino ngati phunziro limene akuphunziralaro likugwirizana ndi zinthu zimene zawazungulira.

Mwachitsanzo, muzikhalidwe zina ndi zinthu zosayenera kuti mamuna aphunzitse mkazi kapena mkazi aphunzitse mamuna. Pamene zikhalidwe zina zimafuna kuti mphunzitse aloredwe kuphunzitsa ndi akulu amudzi asanayambe kuphunzitsa. Ndi zofuna kusintha makhalidwe komanso mmene timavalira ndi cholinga choti anthu ena atilandire.

KUUNIKIRA OPHUNZIRA ANU:

- Kodi ndi zikhalidwe zANJI zimene zikupezeka pakati pa anthuwo?
- Kodi chikhalidwe chao chikhudza bwanji njira zakaphunzitsidwe kanga?
- Kodi chikhalidwe chikhudza bwanji kagwiritsidwe ntchito ka zimene anthu aphunzira?
- Kodi chikhalidwe chikhudza bwanji mmene ophunzira angaulandilire Uthenga Wabwino?
- Kodi ndi zofunika kusintha makhalidwe ngati mavalidwe ndi cholinga choti anthu atilandire?

KUTHEKERA KWAKUTHUPI:

Kuthekerera kwa kuthupi kumakhudza maphunziridwe. Mwachitsanzo, mphuzitsi amene ali ndi ophunzira amene ali ndi mavuto akumva ndiye kuti akuyenera kupeza njira zina zoti zithandize.

Kuunikira ophunzira anu:

- Ikani kutsogolo amene ali ndi mavuto a maso kapena akumva kuti akhale kutsogolo.
- Onetsetsani kuti zothandiza pophunzitsa ndi zazikulu kwambiri kuti zithe kuonedwa mosavuta.
- Gwiritsani ntchito munthu omasulira ngati muli munthu amene samva.
- Konzani njira zapadera kwa anthu amene ali ndi ulumari.
- Atumikireni anthu amenewa ndi cholinga choti Mulungu awakhudza anthu amenewa.

KUKHWIMA MOYO WAUZIMU:

Ophunzira anu akhoza kukhala anthu amene ndi obadwa mwatsopano kapena ayi kapena okhulupilira okhwina moyo wauzimu kapena ayi. Paulo akuchenjeza kuti anthu ena amakhala osakonzeka kuti alandire mnofu wa Mau a Mulungu (choodani chozama cha mau a Mulungu). Koma anthu akuyenera kumwetsedwa mkaka asanayambe kudyetsedwa zozama za choonadi cha Mulungu.

Kuunikira ophunzira anu:

- Kodi ophunzira anu ambiri akhoza kukhala osakhulupilira? Izi zikhoza kukhala zoonadi ngati mukulalikira malo a Mtaunu. Chifukwa cha ichi ndizofunika kuti mulalikire Uthenga Wabwino kwa anthu amenewa.
- Kodi ophunzira anu ambiri ndi anthu amene angobadwa kumene? Koma ngati izi zili chonchi ndi zofunika kwambiri kuti muwaphunzitse anthu amenewa nsanamira zachikhristu.
- Kodi ophunzira anu ambiri akhala okhulupilira? Izi zikhoza kukhala choncho ngati mkumano wanu ukuchitika pakati pa anthu amene ndi amumpingo okhaokha. Koma musamaone ngati kuti wina aliyense ndi okhulupilira pa mkumano ngati umeneu. Mukuyenera kupereka mwai kwa anthu kuti alandire Yesu.

KODI ANTHUWO NDI AKAZI KAPENA NDI AMUNA

Ngati gulu la ophunzira lanu ndi amayi kapena abambo, izi zimakhudza mmene mungaphunzitsire. Mwachitsanzo, phunziro lokamba za udindo wa abambo kuti akonde akazi awo ndi lofunika kuti liperekedwe kwa ophunzira amene ndi abambo kusiyana ndi kulipereka kwa amayi.

Kuunikira ophunzira anu:

Kodi ndi akazi kapena ndi amuna?

Kodi ndi amuna okhaokha?

Kodi ndi amuna ndi akazi?

OKHALA PABANJA KAPENA AYI

Anthu okwatira ali ndi mavuto awo amene ndi osiyana ndi mavuto a anthu amene ndi osakwatira, osiyidwa kapena amene ndi amasiye. Anthu amene ali ndi ana amakumana ndi mavuto osiyana ndi anthu amene alibe ana.

Kuunikira ophunzira anu:

Unikirani ophunzira anu ndi cholinga choti muone kuti alipo angati:

- Osakwatira
- Okwatira komanso ali ndi ana
- Okwatira komanso amene ali ndi ana
- Amasiye komanso okhala ndi ana
- Amasiye koma opanda ana
- Osiyidwa amene sanakwatirensa ndipo akulera ana okha ana.
- Osiyidwa amene sanakwatirebe komanso alibe ana.
- Osiyidwa koma anakwatira ndipo ali ndi ana

MLINGO WACHUMA CHA ANTHU

Mukuyenera kuphunzitsa malingana ndi mlingo wachuma wa amene mukuwaphunzitsa. Yesu anatumikira mosiyana kwa mzimayi pachitsime paja (Yohane 4) kusiyana ndi mmene anamuphunzitsira Nikodemasi. Mzimayi pachitsime paja anali ochepekedwa mumapezedwa ake pamene Nikodomasi anali munthu waudindo wake.

Paulo akufotokoza kuti iye anali okonzeka kupereka uthenga wake malinga ndi mmene anthu aliri:

(I Akorinto 9:22) (werenganinso 19-21).

Kuunikira ophunzira anu:

- Kodi anthu mapezedwa awo a ndalama ndi otani? Kodi ndi achumwa kwambiri kapena kuti ndi osauka? kodi ali ndi zosowa zambira za chuma?
- Kodi amagwira ntchito yanji kapena kuti amatani? Kodi ndi ophunzira, akuchita utumiki, anapuma pa ntchito, kapena samagwira ntchito?
- Kodi amakhala kuti? Kumudzi, ku tauni, dera la anthu osauka kapena olemera, kodi alibe malo okhala?

ZOFUNIKA PA MOYO WA MUNTHU:

Ndi zofunika kuti mudziwe zinthu zimene anthu amafuna mmagawo awa, kuthupi, maganizidwe awo. Izi ndi zofunika kuti muthe kugwiritsa ntchito nyengo za ophunzira anu pemene mukuwaphunzitsa.

Kuunikira ophunzira anu:

Zina mwa zosowa za munthu ndi izi:

- Zosowa zauzimu:
- Chipulumutso
- Chitsimikizo cha chipulumutso
- Chiyero/ kuyeretsa.
- Ubatizo wa mmadzi
- Ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Kumasuridwa ndi machiritso
- Kukula moyo wauzimu. Zina mwa zinthu zimene zikuyenera kuonekera ndi mphantho zauzimu, chipatso chauzimu, kuzindikira chifuniro cha Mulungu, kuthana ndi mavuto a moyo ndi zina zambiri zokhudza moyo.
- Zosowa za munthu zokhudza maganizo a Munthu:
- Mantha

- Kusungulumwa
- Nkhawa
- Mkwiyoy
- Kusadzikhululukira
- Mmene timadzionera
- Kuukira
- Msanje

Zosowa zachuma:

- Ndalama zosakwana kuti munthu apeze zosowa zakuthupi
- Kufunika kokhala pa ntchito

Zosowa zakuthupi:

- Kudwala
- Kukula kwa thupi
- Maonekedwe athu

Mavuto apadera:

- Kutha kwa banja
- Chisawawa
- Kutaya mimba
- Mankhwala ozunguza bongo
- Mowa
- Nyanga
- Kukondera
- Kugwidwa ndi ziwanda
- Kulira anthu otisiya
- Miseche, kudandaula, kutembelera ndi kutukwana
- Zipembedzo zabolza
- Makhalidwe abodza
- Kuphunzitsa ana

NSINKHU:

Maphunziro akuyenera kuperekedw malingana ndi nsinkhu wa anthu. Kamvetsetsedwe ka zinthu kamasintha malingana ndi nsinkhu wa munthu. Anthu amene anaphunzira mmene munthu amakulira ndi kuthupi, maganizidwe ngakhale moyo wauzimu anapeza makhalidwe a magulu a anthu osiyanasiyana. Makhalidwe amenewa amakhala osiyana malinga ndi chikhalidwe cha anthu.

Nsinkhu 2-3:

A. Kuthupi:

1. Amakonda kutengera komanso kuthandiza
2. Amakonda kuyendayenda, amafuna zothamangathamanga komanso nthawi yopuma.
3. Samapilira komanso amakhala wa mantha.
4. Amakonda kugwira zinthu, amakhala ndi chidwi chachikulu
5. Amakonda nyimbo
6. Minyeneyewa yao imakhala kuti sinagwirane

B. Maganizidwe

1. Amakhala ndi maganizo ambiri
2. Amamvetsera kwa mpindi zitatu kapena zinayi
3. Amakonda zinthu zimene akuzidziwa komanso kubwerezabwereza
4. Amakhala ndi mau ochepa amene amawadziwa komanso amakonda nkhani zosovuta.
5. Amaphunzira kudzera kuyang'ana zimene anthu ena akuchita komanso zimene anthu ena amakamba.
6. Amasunga kwambiri zithu
7. Amakhala kuti akukhazikitsa makhalidwe awo amene akhodza kudziwika nawo.
8. Amakonda kulowelera nkhani pamene zikukambidwa.
9. Amakhulupilira zimene amauzidwa.
10. Amasunga zinthu zambiri zimene amamva.
11. Amkhudzika ndi zinthu zimene zimawachitikira anthu ena.

C. makhalidwe ndi anthu ena.

1. Amakhala amantha ndipo amaopa chigulu cha anthu.
2. Amakhala ndi mantha opanda pake.
3. Amafuna kuti chidwi cha anthu onse chikhale pa iye

4. Amakhala odzikonda yekha. Akuyenera kuphunzira kugawana ndi anthu ena.
5. Amakonda kutengera zimene awona.
6. Amafuna adzitchulidwa nthawi zambiri
7. Amatopa nsanga ndipo sachedwa kukhumudwa
8. Amakhumba atakondweretsa makolo komanso aphunzitsi.
9. Amafunika chikondi, kuwamvetsa ndi chitetezo.

D. Moyo wauzimu

1. Amadziwa mmene angamukondweretsa Mulungu komanso amatha kudziwa mmene angamuthokozere Mulungu: amadziwa kuti Baibulo ndi buku la Mulungu komanso kuti tchalitchi ndi nyumba ya Mulungu.
2. Amatha kuzindikira Mulungu ngati munthu okonda.
3. Amadziwa za Mulungu kudzera muchilengedwe komanso mu china chilichonse chimene Mulungu akutchulidwa.
4. Amafuna kudziwa kuti Mulungu ndi aphunzitsi awo amawakonda.
5. Ngati angaphunzitsidwe bwino, amatha kudalira Mulungu.
6. Amatha kusewera ngati alimbikitsidwa.
7. Amatha kupemphera ngati alimbikitsidwa kuti atero.
8. Amaphunzira kupereka chifukwa chakuti amakonda Mulungu

Dzaka 4-5:

A. Kuthekera kwakuthupi:

1. Amatha kudzisamalira kuthupi.
2. Amatha kuvala okha
3. Amokonda kuthamangathamanga
4. Amalankhula kwambiri
5. Samachedwa kupsya mtima
6. Minyewa imakhala kuti ikukulabe
7. Amatha kupilira pang'ono kuthupi

B. Maganizidwe

1. Amatha kupanga zinthu zimene ndi zosavuta kwambiri.
2. Amatha kumvetsera zinthu kwa mphindi zokwana khumi

3. Amatha kuganizira zinthu paokha.
4. Amvetsa zinthu zochepa zokhudza nthawi ndi malo
5. Samachedwa kukonda komanso kukhala ndi chifundo
6. Kaganizidwe kao kamakhala kakukula
7. Amayamba kuona zinthu moyenera
8. Amatha kuloweza ma vesi afupi

C. Makhalidwe awo ndi anthu:

- Amatha kuchita zinthu zosiyanasiya
- Amayamba kukwanitsa kucheza ndi anthu ena
- Akonda kuchita masewera opanga ndi anthu ena
- Amakhala ndi mwambo
- Amakhala odzikonda, amayenera kuphunzira kupereka kwa anthu ena
- Amayamba kukula mu utsogoleri
- Amakonda kwambiri ndipo amakonda kusangalatsa anthu kwambiri
- Amakonda kukamba nkhani ndi kuzionetsera

D. Moyo wauzimu

- Amatha kukwanitsa kupembedza Mulungu komanso amatha kuyamika Mulungu kudzera mu chilengedwe chake.
- Amayamba kukamba za Mulungu ngati akumudziwa
- Amazindikira kuti Mulungu amawakonda ndi kusamala za iwo
- Amazindikira kuti kuchita zinthu mwa chifuniro chao ndi tchimo
- Amatha kuphunzira za kupezeka kwa Mulungu, chithandizo chake ndi mzeru yake.
- Nthawi zambiri amakhulupilira zinthu koma akuyenera kuphunzira kukhupilira Mulungu

Msinkhu wa 6-8:

A. Kuthupi

- Makulidwe awo amakhala pang'onopang'ono
- Amakhala ndi mphamvu zambiri
- Amatopa msanga
- Amafuna zochitika zambiri
- Amafuna kuphunzira kuti amalize zimene akuchita

- Amakonda kugwira zinthu

B. Maganizidwe

- Amatha kusangalatsidwa kwambiri komanso amamva chisoni
- Amafuna kukonedwa kwapadera komanso chitsogozo
- Amaganiza zinthu zambiri komanso kulingalira
- Amakonda nkhani za Baibulo zimene zimaonetsera mphamvu ya Mulungu.
- Amaphunzira kudzera zimene akumva komanso ndi kuona
- Amaphunzira kupanga zisankho
- Amatha kuloweza mau kusiyana ndi mfundo
- Amayamba kukonda zinthu zokhudza mbiri

C. Makhalidwe ndi anthu

- Amakula ngati akuyamikiridwa
- Amayenera kuphunzitsidwa kuchita chifundo, kusadzikonda komanso kuganizira anthu ena.
- Amakonda kuchita zinthu zimene akulu akuchita ndipo amafuna kuyamikiridwa
- Amakonda nkhani zokhudza ana ansinkhu wake.
- Nthawi zina amachita kusaweruzika
- Samakonda zinthu zampikisano
- Amayamba kusankha anthu ocheza nawo ndipo amakhala ndi anzawo amamtima

D. Moyo wauzimu

- Amapindura kuchokera kwa anthu amene ndi okwima muuzimu
- Amazindikira chikondi cha Mulungu komanso chikhulukiro cha Mulungu
- Amuphunzira kulemekeza anthu ena
- Amakhala okonzeka kulandira khristu ngati mpulumutsi
- Akhoza kuphunzira kupemphera
- Akhoza kukonza mavuto kugwiritsa ntchito Baibulo
- Akuyenera kuphunzitsidwa zakulapa machimo
- Amakhala ndi chidwi kufuna kudziwa za imfa
- Amakonda nkhani zokhudza kumenyana

Msinkhu wa 9-11.

A. Makulidwe kuthupi

1. Amakhala athanzi kwambiri
2. Amakhala othamangathamanga
3. Amayamba kupanga zinthu paokha
4. Samakhala aukhondo
5. Amakonda kusewera kunja kwa nyumba
6. Amayamba kusalika pong'onopang'ono.

B. Maganizidwe

1. Amatha kugwiritsa ntchito Baibulo kuti apeze ma vesi komanso mayankho amafunso.
2. Amakhala ndi kuthekera kwakulu koloweza zinthu
3. Amayamba kuzindikira za nthawi komanso malo amene akukhala
4. Amakhala ndi chidwi chokonza zinthu zolakwika
5. Amakhala ndi chidwi chachikulu kuti adziwe zinthu
6. Amakhala ndi chidwi chopanga zinthu zambiri monga kulemba ndakaturu komanso nkhani zimene
7. Amakhala ndi luso ngati angapatsidwe mwai ndi nthawi kuti apange zinthu
8. Amakonda kuwona mmene akuchitira
9. Amakhala ndi chidwi ndi chilengedwe komanso anthu olimba mtima
10. Amakhala ndi kuthekera koika chidwi pa zinthu kwa nthawi yaitali

C. Ubale ndi anthu ena

1. Akhoza kulimbikitsidwa kuti akhale ndi makhalidwe abwino
2. Amakhala ndi chidwi ndi zinthu zimene ndi zoyenera /zokomera anthu onse
3. Amakonda kutenga mbali mkalasi.
4. Amakonda kucheza ndi anzake achitsikana kapena achinyamata ngati ali mnyamata.
5. Amakhala odzipereka kwa anzake
6. Amasilira atsogoleri
7. Akuyenera kuphunzira kulemekeza ulamuliro
8. Amakhala opanda manyazi kusiyana ndi mmene anali mwana

D. Moyo wauzimu.

1. Amakhala okonzeka kupulumutsidwa
2. Amamva zimene akuphunzitsidwa zokhudza Khristu Yesu

3. Akhoza kumvetsetsa chiphunzitso chachikhristu
4. Amafunika kulimbikitsidwa kuti adzipemphelera moyo wao watsiku ndi tsiku.
5. Akhoza kukhala ndi chidwi chopulumutsa anthu apabanja pawo komanso anthu a dera limene amakhala

Nsinkhu wa 12-14:

A. Kuthupi

1. Amakula nsanga
2. Atsikana amakula nsanga kusiyana ndi anyamata
3. Amachita manyazi ndi makulidwe awo.
4. Amakhala ndi mphamvu zambiri komanso sachedwa kutopa
5. Iyi ndi thawi yovutitsitsa ya moyo wawo

B. Maganizidwe

1. Amakhala ndi mtima ofuna kudziwitsitsa zinthu
2. Amakhala okonda kucheza
3. Amakhala ndi maloto opanda pake
4. Samachedwa kukhumudwa
5. Amafuna kupanga ziganizo pawokha
6. Amakhala ndi mtima ofuna kuukira kapena kudelera ulamuliro

C. Makhalidwe ndi anthu

1. Amayamba kumvera anzawo kapena aphunzitsi kusiyana ndi makolo.
2. Amatsata zimene anthu akupanga.
3. Samasamala za anthu ena
4. Samakonda kitchedwa kuti achibwana
5. Amayamba kukhala ndi chidwi ndi anthu akazi ngati ali mamuna kapena amuna ngati ali akazi.
6. Amafuna kukhala ofunika komanso kukhala ndi anzawo ambiri.

D. Moyo wauzimu

1. Amayang'ana kwa anthu akulu kuti awatsogolere
2. Amakhala ndi mafunso ambiri
3. Akuyenera kuzindikira kuti akufunika mpulumutsi

4. Amafunika chitsogozo

Msinkhu wa 15-18

A. Kuthupi

1. Amakula kwambiri
2. Ayamba kukhala ndi zizolowezi zokhazika
3. Amasamala mmene akuwonokera
4. Amakhala ndi chidwi ndi mmene akuonekera.

B. Maganizidwe

1. Amakhala ndi kuthekera koganiza kwambiri.
2. Amakumbukira mfundo zambiri kusiyana ndi mau
3. Amakhala ndi mfundo zambiri
4. Amabweza maganizidwe

C. Makhalidwe ndi anthu ena

1. Amafuna maudindo ndi utsogoleri
2. Amafuna kukhala pa gulu la abwenzi
3. Amafuna kutamidwa ndi anthu ena makamaka anzawo.
4. Amakhala ndi chidwi pa tsogolo lawo
5. Amakhala ndi chidwi chambiri kuti athandize anthu ena.
6. Amavutika kuti adziletse makhalidwe awo
7. Amafuna zinthu zosangalatsa
8. Sachedwa kukhumudwa
9. Amatsutsana ndi ulamuliro kapena utsogoleri
10. Amafuna chitezo

D. Moyo wauzimu

1. Nthawi zambiri amakhala ndi chikaiko pa zinthu zauzimu
2. Atengeka nsanga
3. Amafuna kukhala chikhristu choti iwo atenge mbali

Anthu akulu akulu

A. Kuthupi

Nthawi zambiri anthu akulu amatha kukwanitsa kukhala panso nthawi yaitali komanso amakhala ndi mavuto athanzi kusiyana ndi anthu achichepere. Anthu akuluakulu amalimbana ndi mmene akuonekera komanso ndi mmene akuchitira zinthu zao makamaka akakhala kuti sakufikira zimene anthu amayembekeza malingana ndi chikhalidwe.

B. Maganizidwe

Nthawi zambiri anthu akuluakulu amakhala kuti akhazikika mu zochita zowo kotere kuti kumakhala kovuta kuti munthu uwasunthe. Nthawi zambiri zimkhala ngati kuti pamene munthu akukula zimakhala zovuta kuti aphunzire zinthu zatsopano. Anthu akulu amatha kumvetsera kwa nthawi yaitali kusiyana ndi ana. Anthu ambiri achikulire amakhala ndi kumvetsetsa kwakukulu kwa chikhalidwe ndi chilankhulo chao.

C. Makhalidwe ndi anthu ena

Anthu ambiri akulu amakhala kuti apeza abwenzi ambiri okhazikika amene amakhala kuti zochitika zawo ndi zofanana. Ambiri amakhala kuti asankha kale munthu amene akufuna kukhala naye ngati bwenzi lawo.

D. Moyo wauzimu

Anthu akuluakulu amafunika uphungu wauzimu mu ziganizo zambiri za moyo wao. Zina mwa ziganizo zimenezi ndi chisankho cha ukwati, maphunziro komanso ntchito imene munthu akufuna kumagwira. Anthu amene ndi okwatira amafunaso uphungu wapadera.

Okhulupilira amafunika ophungu wapadera ndi cholinga choti akule moyo wauzimu ndi kuyamba kutenga pa utumiki ku mpingo. Amayenera kuzindikira mphatso zawo ndi kuyamba kuzigwiritsa ntchito. Akakhala osakhulupilira akuyenera kuti amve uthenga Wabwino ndi kutembenuka mtima.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi mau oti kuunikira ophunzira amathauza chiani?

3. Kodi ndi zofunika bwanji kuti muunikire anthu amene mukuwaphunzitsa?

4. Fotokozerani mwachidule njira zimene zikuyenera kutsatidwa pamene mukuunikira ophunzira

5. Sankhani gulu la anthu limene mukufuna kuphunzitsa kapena limene mumaphunzitsa kale ndipo unikirani makhalidwe a gulu limeneli. Lembani mwachidule makhalidwe a gulu limeneli.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJZERA POPHUNZIRA

1. Yesu anali ndi gulu la ophunzira khumu ndi awiri. Gwiritsani ntchito ukadaulo umene mwaphunzira mu chaputala ichi kuti muunikire anthu ophunzira a Yesu. Mupeza zinthu zokhudza ophunzira a Yesu mu mabuku a Mateyu, Marko, Luka ndi Machitidwe Atumwi.
2. Unikirani gulu la ophunzira limene mukufuna kukaphunzitsa.
3. Werengani phunzira limene Yesu anaphunzitsa kwa Nikodemo pa Yohane 3 komanso kwa Mzimayi pa Chitsime mu buku la Yohane.

CHAPUTALA 9

KUFOTOKOZERA ZOLINGA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokozera tanthauzo la mau oti zolinga
- Kufotokozera kufunika kokhala ndi zolinga pophunzitsa
- Lembani zolinga zophunzitsira.
- Unikirani zolinga zanu.
- Fotokozerani kusiyana pakati pa zolinga zazikulu ndi zazing'no
- Kupeza cholinga chenicheni cha kuphunzitsa Baibulo.

VESI YOTSOGOLERA:

Amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, 8 kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu (Akolose 1:28)

MAU OYAMBA

Taphunzira kuti kukula moyo wauzimu sikumatengera zimene ophunzira wamva koma zimene ophunzirayo akukwanitsa kuchita pa zimene waphunzira. Chaputala ichi chikuthandizani kufotokozera zolinga zaphunziro zimene zikuthandizeni kuti muthe kudziwa ngati ophunzira amvetsetsa zimene amayenera kuchita komanso kugwiritsa ntchito zinthu zimene aphanzira.

ZOLINGA

Cholinga ndi chinthu chimene chikuyenera kukwaniritsidwa. Ndi chinthu chimene chimayembekezedwa kuti chichitike kumapeto kwa zinthu. Pamene mphunzitsi wafotokoza zolinga za phunziro, iye amalemba zimene ophunzira akuyenera kukwaniritsa. Kapena kuti izi zimakhala zinthu zimene ophunzira akuyembekezedwa kuti akwanitse pamapeto paphunziro. Phunziro limene mukuphunzirali liri ndi cholinga kapena zolinga. Bwelerani kumapeto kwa phunziro limeneli ndipo onaninso zolinga zaphunziroli.

KUFUNIKA KWA ZOLINGA

Zolinga ndi zofunika chifukwa cha zinthu izi:

1. Zimatsogolera aphanzitsi, mapemphero, dongosolo ndi zinthu zonse kuti zifikire zolinga zimene zakhazikitsikidwa. Munthu amadziwa chimene chikuyenera kuchitika mu phunziro kotere kuti mumakonzekera moyenelera.
2. Zimathandiza kuti muthe kuona ngati kuphunzira kukuyenda bwino. Mumatha kuona ngati ophunzira akwaniritsa zimene amayenera kuphunzira.

3. Zimathandiza kuti kuphunzira kuyende bwino. Chifukwa chakuti mumatha kuona ngati kuphunzira kwa chitika, mumatha kuoana pamene mwachita bwino komanso pamene mukuyenera kuchita bwino. Mukhoza kuphunzira kuchokera zolephelera zanu ngakhale zimene mwachita bwino kuti mupitilire kuchitabe bwino
4. Zimathandiza ophunzira kuti akhale akuchita mau osati ongomva mau chabe. Ngati mwakhazikitsa zolinga ndipo mwazifotokozerera kwa ophunzira anu zimathandiza ophunzira anu kuti azindikire zimene mukuyembekezera kwa iwo.

KALEMBEDWE KA ZOLINGA

LEMBANI ZOLINGA MALINGANA NDI ZIMENE OPHUNZIRA AKUYENERA KUKWANITSA

Lembani mwachindunji zimene mukufuna kuti akwanitse. Chitsanzo cha izi ndi ichi:

“pamapeto pa chaputala ichi ophunzira akuyenera kukwanitsa kufotokoza Yohane 3:16”

Chitsanzo cha cholinga chimene sichinalembedwe bwino ndi ichi:

“Ndiphunzitsa Yohane 3:16”

Cholinga choyamba chija chafotokozeredwa bwino chifukwa chakuti chikusonyeza zimene ophunzira akuyenera kukwaniritsa pamapeto pa phunziro. Mukhoza kuona ngati ophunzira akwanitsa zimene amayenera kuchita.

Cholinga chachiwiri ndi chosaynera chifukwa chakuti chikutchula zimene mphunzitsi akuyenera kukwaniritsa osati zimene ophunzira akuyenera kukwaniritsa. Kodi mudziwa bwanji kuti mwaphunzitsa moyenera. Cholingachi sichikuthandiza kuti muthe kuzindikira ngati kuphunzira kwachitika.

YAMBANI CHOLINGA CHILICHONSE NDI M’NENI

M’neni ndi mau amene amasonyeza ntchito kapena zimene zikuyenera kutsatira. Mukuyenera kugwiritsa ntchito mau ngati awa.

“pamapeto pa phunziro ili ophunzira akuyenera kukwanitsa:”

Kenako tchulani zolinga zonse poyamba ndi mnene. Mu gawo la zophunzira zoonjezera za chaputala ichi muli aneni amene angakuthandizeni kutchula zolinga zanu.

CHOLINGA CHILICHONSE CHIKUYENERA KUTCHULIDWA PACHOKHA

Mukuyenera kutchula cholinga chimodzi pakamodzi. Chitsanzo cha izi ndi ichi:

“ pamapeto pa phunziro ili ophunzira akuyenera:

Cholondora: Kuloweza Yohane 3:16

Cholakwika: kuloweza ndi ndi kufotokozerera Yohane 3:16.

Ngati mukufuna kuti afotokozerenso ndiye kuti kufotokozerako kukhale padera ngati cholinga chapadera.

“pamapeto paphunziro limeneli mukuyenera:”

Kuloweza Yohane 3:16

Kufotokoza Yohane 3:16

TCHULANI ZOLINGA ZOFANANA MOTSOGOZANA:

Cholinga chinachilichonse chikuyenera kugwirizana ndi chinzake. Mwachitsanzo “kuloweza Yohane 3:16 ndi cholinga chabwino kuti chiyambe kenako mukhoza kuuza ophunzira kuti afotokoza Yohane 3:16. Ophunzira akuyenera kudziwa chinthu asanayambe kuchifotokoza.

FOTOKOZERA CHOLINGA CHILICHONSE NGATI KHALIDWE LIMENE MUKHOZA KULIONA

Chitsanzo cha izi ndi ichi:

“pamapeto pa chaputala ichi ophunzira akuyenera:”

cholondora: Kufotokoza Yohane 3:16

Cholakwika: kumvetsetsa Yohane 3:16.

Ngati ophunzira angafokotokoze Yohane 3:16 mukhoza kudziwa kuti akumvetsa. Koma ngati cholinga chanu ndi kuti ophunzira amvetse ndi zovuta kuti muthu kuzindikira ngati akumvetsa. Cholinga chimenechi chisikufotokoza chimene ophunzira akuyenera kukwanitsa kuti muthe kuona ngati aphunzira akwaniritsa

CHOLINGA CHILICHONSE CHIKUYENERA KUKHALA CHOTHEKA

Ngati mungakhazikitse zolinga zimene ndi zovuta, ophunzira amataya mtima

MNDANDANDA OTHANDIZA KULEMBA ZOLINGA

Gwiritsani ntchito mndandanda wa mafunso awa kuti mulembe zolinga pa ophunzira anu.

1. Kodi zalembedwa malinga ndi zimene mukufuna kuti ophunzira athe kukwanitsa? Kodi zikufotokoza zimene mukuyembekezera kuti ophunzira akwanitse osati zimene mukufuna kukwanitsa?
2. Kodi mukhoza kuona zimene mukufuna kuti ophunzira akwanitse. Kodi mwalembe zolinga zanu ngati makhalidwe amene mukhoza kuwaona.
3. Kodi ndi zachindunji? Kodi zikufotokoza zimene mukuyembekezera kwa ophunzira anu?
4. Kodi zikukhudza ophunzira wina aliyense payekha? Kodi pali mutu umodzi pa phunziro lina lilironse.
5. Kodi ndi zolumikizana? kodi zolingazo ndi zolumikizana.
6. Kodi ndi zotheka? Onetsetsani kuti sizovuta kwambiri ndi cholinga choti ophunzira athe kukwanitsa.

7. Kodi ndi zogwirizana ndi Baibulo.

ZOLINGA ZAZIKULU NDI ZAZING'ONO

Mukuyenera kukhazikitsa cholinga chachikulu komanso chaching'ono:

ZOLINGA ZIKULUZIKULU

Zolinga zikuluzikulu ndi mfundo zimene ophunzira akuyera kukwanitsa pa phunziro lonsero. Zina mwa zolinga zikuluzikulu ndi izi:

Ngati zotsatira za phunziro limeneli, ophunzira akuyenera:

Ophunzira akuyenera kukwanitsa kuvomeleza uthenga Wabwino:

Cholinga chimene ndi chinthu choti mutha kuchiona. kodi ophunzirawo alapa ndi kusiya machimo awo?

Kulandira Ubatizo wa Mzimu Woyera:

Aphunzitsi akuyenera kuthandiza ophunzira kuti akwaniritse zolinga zimenezi. Kulankhula malirime ndi chizindikiro chimene chikhoza kuoneka ngati umboni wa ubatizo komanso mphamvu yoti alalike uthenga Wabwino kukhoza kuoneka ngati cholinga chimene chakwaniritsidwa.

Kubatizidwa ubatizo wamadzi

Ophunzira amene abadwa mwatsopano akuyenera kulimbikitsidwa kutsata chitsanzo cha Yesu chobatizidwa m' mandzi ngati kuchitira umboni poyera za chipulumutso chao.

Kuonetsera chipatso cha Mzimu Woyera

Cholinga chachikulu chophunzitsa ndi chakuti ophunzira akhale ndi khalidwe la ngati la Khristu Yesu. Gawo limodzi la izi ndi zipatso za Mzimu woyera zimene zatchulidwa pa Agalatiya 5:22. Chinthu china chofunikanso ndi kukuza chikhalidwe cha ufumu wa Mulungu malinga ndi mfundo zimene Yesu Khristu anaphunzitsa komanso zimene zikufotokozeredwa mu makalata a Chipangano Chatsopano.

Kuzindikira mpatso zauzimu

Baibulo limafotokoza kuti okhulupilira wina aliyense ali ndi mpatso yauzimu. Ndi udindo wa mphuzitsi wina aliyense kuti athandize ophunzira ake kuzindikira mpatso yao yauzimu.

Kugwiritsa ntchito mpatso yauzimu.

sizokwanira kungozindikira mpatso yanu. Ophunzira akuyenera kulimbikitsidwa kugwiritsa ntchito mpatso zao zauzimu pa utumiki.

Kubala kuuzimu

Kaphunzitsa kumakhala kosakwana ngati ophunzira saphunzitsa ophunzira ena. Werengani II Timoteo 2:2.

Kusanthula Baibulo mwainu nokha

Kusanthula Baibulo mwainu nokha ndi kofunika kwambiri. Mmene mumaphunzitsira Baibulo zikuyenera kuthandiza ophunzira kuti nawonso athe kuwerenga Baibulo pa okha. Phunziro la Haverstine International lotchedwa ukadaulo osanthula Baibulo ndi lothandiza kuti muzindikire ndondomeko zosiyanasiyana zosanthulira Baibulo.

Kugwiritsa ntchito njira zopangira kafukufuku wa Baibulo

Ngati muli ndi mwai wa zinthu zothandiza kuchita kafukufuku wa Baibulo monga nthanthauzira mau wa Baibulo, limbikitsani ophunzira kuti agwiritse ntchito zinthu zimenezi.

Kupemphera pafupipafupi

Ophunzira akuyenera kuphunzitsidwa kupemphera pafupipafupi pa gulu komanso pa iwo okha.

Kutenga gawo pa chiyanjano mu mpingo:

Ophunzira akuyenera kutenga nawo mbali mu mpingo

ZOLINGA ZAZING'ONO

Zolinga zazing'ono ndi zolinga zimene zimene mphuzitsi amakonzekera kuphunzitsa phunziro lina lilironse. Izi zimasintha malinga ndi phunziro mukuphunzitsa. Werenganinso zolinga zimene zaperekedwa pachiyambi cha phunziro ili.

CHOLINGA CHENICHENI

Baibulo limafotokoza cholinga chenicheni cha kuphunzitsa Baibulo.

Amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu; (Akolose 1:28)

Cholinga chenicheni chakuphunzitsa ndi kukonzekeretsa ophunzira kuti akhale angwiro pamaso pa Mulungu ndi Khristu Yesu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Fotokozerani tanthauzo la mau oti cholinga

3. Kodi zolinga ndi zofunika bwanji pophunzitsa

4. Kodi kusiyana kwa cholinga chachikulu ndi chaching'ono ndi chiani?

5. Ndi cholinga chiti chimene chalembedwa molondora

Pamapeto pa phunziro lino ophunzira akuyenera?

chitsanzo A: kudziwa Yohane 3:16

Chitsanzo B: kuloweza Yohane 3:16

Chitanzo _____ ndi cholondora

6. Kodi cholinga chenicheni cha kuphunzitsa Baibulo ndi chiani

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Gwiritsani ntchito tchati ichi kuti musankhe mnene amene mukhoza kugwritsa ntchito polemba zolinga

| Ngati cholinga chili | chidziwitso | kumvetsetsa | ukadauro |
|----------------------|-------------------------|----------------------|--------------------|
| | Kagwiritsidwe | Kagwiritsidwe | Kagwiritsidwe |
| | Ntchito ka mnene | Ntchito ka mnene | Ntchito ka mnene |
| | Tchulani | unikirani | kuthandiza |
| | Unikirani | kusiyantsa | kutsogolera |
| | Tchulani mndandanda | kufananitsa pakati | kuphunzitsa |
| | Fotokozani | kuika zinthu mmagulu | kukonza ndondomeko |
| | Werengani | sankhani | funsani |
| | Lakatulani | lekanitsani | gwiritsani ntchito |
| | Kumbukirani | zindikirani | kuloweza pamtima |
| | Lembani | fananitsani | kufotokozera |
| | Pezani | masulirani | kulongosola |
| | Lwezani | santhulani | kuthandiza |
| | Fukulani | kambiranani | kuchita kafukufuku |
| | Zindikirani | | kuonetsera |
| | Dziwani za | | kukonza |
| | Perekani tanthauzo | | |
| | Fotokozerani | | |
| | Fotokozerani mwachidule | | |

2. Lembani zolinga za phunziro limene mukufa kuphunzitsa. Gwiritsani ntchito mndanda waperekedwa ndi cholinga choti muunikire zolinga zimene mwalembe.
3. Gwiritsani ntchito mndanda uli munsimuwu kuti muone zolinga zimene Mulungu anakhazikitsa pa mphatso zautimiki.

AEFESO 4:11-16

Ndipo mphatso zimenezi ndi zakuti ena:

- A. Pali mautumiki osiyanasiyana: ena ndi atumwi, aneneri, aphunzitsi ndi alaliki
- B. Cholinga chake: Ndikuti zikakonzekeretse anthu oyera mtima ku ntchito ya Utumiki komanso ndi cholinga choti zikamange thupi la Khristu Yesu.

1. Zotsatira zoyembekezekereka: kufikira anthu onse afikira mlingo wa umodzi pa chikhulupiliro ndi chidziwitso cha Mwana wa Mulungu. Komanso kuti akakhale mu ugwiro onse wa Khristu Yesu.
2. Makhalidwe oyenera: Kuti tisakhalenso ngati ana.
 - a. Zinthu zosayenera: kusunthika ndi mphepo ya chiphunzitso chinachilichonse chachinyengo chophunzitsidwa ndi anthu achinyengo
 - b. Zoyenera: kuyankhula choonadi mwa chikondi. Komanso tikuyenera kukula mwa Yesu Khristu amene ndi mutu wa thupi.

CHAPUTALA 10

KUKONZA PHUNZIRO

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kupeza zinthu zimene zimapezeka mu phunziro linalilironse.
- Kuzindikira ma gawo a kukonzekera pophunzitsa.
- Kufokozerera njira zoyenera kutsatidwa pokonza phunziro.
- Kukonza phunziro

VESI YOTSOGOLERA:

Lilime la anzeru linena bwino zomwe adziwa; Koma m'kamwa mwa opusa mutsanulira utsiru. (Miyambo 15:2)

MAU OYAMBA

Pakadali pano mwaphunzira zinthu zimene Yesu anaphunzitsa. Zina zimene mwaphunzira ndi kagwiritsidwe ntchito ka zinthu zothandiza pophunzira, kuunikira ophunzira komanso kalembedwe ka zolinga pophunzira.

KUPHUNZITSA MALINGA NDI NYENGO

Pamene mukuphunzitsa dziwani kuti phunziro lina lilironse limakhala ndi zinthu izi.

MPHAMVU YA MULUNGU

Mulungu Tate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi amene amapereka mphamvu pophunzitsa Baibulo. Mzimu ndi amene amathandiza mphuzitsi kuti aphunzitse anthu ndi kumva komanso kumvetsetsa. (Werenganinso chaputala 2)

MPHUZITSI

Mphuzitsi ndi amene amadziwa choonadi chimene chikuyenera kuphunzitsidwa:

Ndipo anaturuka Iye, naona khamu lalikuru la anthu, nagwidwa cifundo ndi iwo, cifukwa anali ngati nkhosa zopanda mbusa; ndipo anayamba kuwaphunzitsa zinthu zambiri. (Marko 6:34)

(werenganinso chaputala 1 ndi 2 “mphuzitsi amachokera kwa Mulungu”)

OPHUNZIRA

Ophunzira ndi munthu wina aliyense amene amapezeka mu phunziro ndi chidwi chonse. Ophunzira amaphunzira pamene akumva, kuona ndi kumvetsetsa zimene zikuphunzitsidwa.

Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, 1 monga anakhoza kumva; (Marko 4:33)

CHILANKHULO

Chilankhulo chimene mukuyenera kugwiritsa ntchito chikuyenera kukhala chimene ophunzira anu amamva. Koma ngati sizili choncho ndiye kuti mukuyenera kupeza otanthauzira.

MYENGO YA OPHUNZIRA

Zimene akuphunzira zikuyenera kukhala zogwirizana ndi nyengo zimene amakumana nazo. Uthenga umene akuphunzira ukuyenera kukumana ndi nyengo zimene akudutsamo.

PHUNZIRO

Phunziro limene mukuyenera kuphunzira likuyenera kukhazikika pa mau a Mulungu. Baibulo ndi buku limene mukuyenera kuphunzitsa. Mabuku ena akhoza kugwiritsidwa ntchito koma mau a Mulungu ndi amene ali ndi ulamuliro.

ZOLINGA

Phunziro lina lilironse likuyenera kukhala ndi cholinga chimene ndi chogwirizana ndi zolinga za phunziro

NJIRA:

Phunziro lilironse limaphunzitsidwa pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana.

CHITSANZO

Chitsanzo cha zinthu zimene zimapezeka mu phunziro lina lilironse ndi ichi:

Mphamvu ya Mulungu: Yesu amayankhula uthenga ochokera kwa Mulungu mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Ophunzitsa: Yesu.

Ophunzira: mzimayi pachitsime

Chilankhulo: Yesu analankhula naye mzimayiyu mu chilankhulo chimene amachidziwa.

Malo: Nkhaniyi inachitika pa chitsime cha Yakobo ndipo Yesu anagwiritsa ntchito malo amewa kuti aphunzitse.

Phunziro: Mulungu ndi mzimu kotero kuti onse akuyenera kulambira mu mzimu ndi choonadi. Ndipo Yesu ndi gwero la madzi a moyo.

Zolinga: kuti amutsogolere mzimayi kuti azindikire choonadi chake chenicheni.

Njira: Yesu anagwiritsa ntchito chinthu chodziwika ngati njira yofuna kuphunzitsa. Yesu anagwiritsa ntchito nyengo yokatunga madzi. Yesu anagwiritsa ntchito kusiyana kwa madzi amoyo ndi madzi akuthupi. Iye anagwiritsa ntchito chipangano chakale pofuna kuonetsa chosowa cha mzimayiyu.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

Pakadali pano ndinu okonzeka kuti mukhoza kukonzekera kuphunzitsa potsata njira zili munsimuzi:

STEPE 1- kukonzekera kuuzimu:

Mukuyenera kukonza mtima wanu:

Malongoledwe a mtima nga munthu; Koma mayankhidwe a lilime acokera kwa Yehova. (Miyambo 16:1)

Mukuyenera kukonzekeretsa maganizo anu:

Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye, (Yakobo 1:5)

Mukuyenera kupemphelera kuti Mulungu akonze mitima ya ophunzira anu kuti athe kulandira mau a Mulungu. Komanso mudzipemphelere nokha kuti Mulungu akudzodzeni kuti muthe kuphunzitsa mau a Mulungu.

STEPE –konzekerani phunziro:

werengani ndime imene mukufuna kuphunzitsa. Ndipo werenganinso ndime zimene zikugwirizana ndi phunziro lanu kuti muthe kudziwa zambiri. Lingalirani ndime imene mukufuna kuphunzitsa. Werengani china chilichonse chimene Baibulo limafotokoza chokhudza zimene mukufuna kuphunzitsa. Ndipo ngati muli ndi zinthu zothandiza kuti kuchita kafukufuku wa Baibulo, gwiritsani ntchito zinthu zimenezi.

Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wanchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi. (II Timoteo 2:15)

Pamene mukuwerenga zimene mukufuna kuphunzitsa, lembani mavumbulutso apadera amene mwalandira kuchokera kwa Mzimu Woyera. Ndipo mukhoza kugwiritsa ntchito zimene mwalembazo kuti mulembe dongosolo la zimene mukufuna kuphunzitsa.

STEPE 3- unikirani anthu amene mukufuna kuphunzitsa:

Gwiritsani ntchito ukadauro umene mwaphunzira mu chaputala 8 kuti muunikire ophunzira anu.

STEPE 4- khazikitsani zolinga:

Pogwiritsa ntchito zinthu zimene mwapeza powerenga, komanso poganizira anthu amene mukawaphunzitse, khazikitsani zolinga zimene mukufuna kuti phunziro lanu likwanitse. (Kuti mudziwe zambiri, werenganinso chaputala 9)

STEP 5- Lembani mndandanda waphunziro lanu:

Phunziro linalilironse limakhala ndi magawo anayi ndipo ena mwa magawo amenewa ndi awa: chiyambi cha phunziro, zinthu zimene zikuyenera kuphunzitsidwa, kagwiritsidwe ntchito ka zimene zaphunzitsidwa ndi mathero aphunziro. Mndandanda umakhala ndi mfundo zikuluzikulu

zimene mukufa kufotokozerana mu phunziro limene mukufuna kuphunzitsa. Kulemba ndandanda kumathandiza chifukwa munthu sumaphunzitsa zimene sunakonzeke kuti uphunzitse komanso zimathandiza kuti ukumbukire mfundo zofunika zimene munthu umayenera kuphunzitsa. Gwiritsani ntchito zinthu zimene mwapeza powerenga kuti mulembe mndandanda ophunzitsira.

Mndandanda okhoza kulembedwa moteremu:

Mutu: Mutu umakuthandizani kuti mukumbukire zimene mukuphunzitsa komanso zimathandiza kuti mphuzitsi akhale olakhula mwachindunji phunziro lake. Mukuyenera kusankha mutu umene ukuonetsera choonadi chachikulu chaphunziro lanu. Mukuyenera kudzifunsa za chimene mukuphunzitsa muphunziro lanu komanso mukuyenera kulemba mutu wanu pachiyambi pa phunziro lanu.

Chiyambi: chiyambi ndi mau oyamba a phunziro lanu. Ndi zofunikwa kwambiri kuti mau oyamba akuyenera kukhala osangalatsa kapena opereka chikoka kwa ophunzira kupanda kutero zimakhala zovuta kuti ophunzira amvetsera mwachidwi.

Yesu nthawi zambiri samagwiritsa ntchito chiyambi chimene tonse timadziwa. Iye amatha kungoyamba ndi mau oti “ndinena ndinena” Pamene Yesu amanena mau amenewa zinali chimodzimodzi kunena kuti mvetserani mosamala chifukwa ndi zofunika.

Yesu amakopa anthu kuti amvetsera mwachidwi poyamba ndi mau opereka chikoka kwa munthu amene akulankula naye. Mwachitsanzo, iye anayamba ndi kulankhula ndi mzimayi pachitsime paja pomupempha madzi kumwa.

Kunali ngati ora lacisanu ndi cimodzi. Kunadza mkazi woturuka m'Samariya kudzatunga madzi. Yesu ananena naye, Undipatse Ine ndimwe. (Yohane 4:7)

Mzimayi anali atabwera kuti adzatunge mmdazi kotere kuti Yesu anayamba kulankhula pa zinthu zimene zinali zomkomera mzimayiyu. Chiyambi chimene Yesu anapereka chinapangitsa kuti ayambe kukambirana za phunziro la madzi amoyo.

Ngati anthu amene akufuna kuwaphunzitsa chidwi chao chili pa chilamulo cha mose nde kuti Yesu anamagwiritsa ntchito mutu umenewu ngati chiyambi chake. Koma ngati iwo amakhudzika kwambiri ndi ufumu wa Israeli, ndiye kuti Yesu ayamba chiyambi chake ndi mutu ogwirizana ndi zimene anthu amakonda. Ngati mungayambe phunziro lanu ndi mutu umene ophunzira anu amakondweretsedwa nao zimapereka chikoka chachikulu kotere kuti mukhoza kugawana nao anthu amenewa Uthenga Wabwino.

Yesu amagwiritsanso ntchito zinthu ngati mafunso ndi mayankho, mafanizo, kusiyantsa zinthu komanso malemba ndi cholinga choti akope anthu kuti amvetsera. Iye amagwiritsanso ntchito nyengo zimene zinali gawo limodzi la anthu kapena kuti zinthu zimene anthu amadutsamo. Iye amagwiritsa ntchito zinthu zimene amazidziwa kuti aphunzitse zimene samadziwa. Komanso amawatenga anthu kuchokera pa mfundo yodziwika ndi wina aliyense kupita pa mfundo zikuluzikulu.

Chiyambi chikuyenera kukhala:
chachifupi: ngati chili chachitali anthu amasiya kumvetsera.

Chachikoka: chikuyenera kupereka chikoka kwa omvera: chikuyenera kukhazikika pa zimene omvera amakonda.

Chokumbukirika: chikuyenera kukhala chokumbukirika.

Choyenera: chiyambi chikuyenera kugwirizana ndi choonadi chimene mukufuna kuphunzitsa. Mukuyenera kugwiritsa ntchito chiyambi pofuna kudziwitsa omvera mfundo zimene muphunzitse

Mukuyenera kukonza chiyambi chimene chikonzekeeretsa ophunzira anu kuti akhale ndi chidwi ndi zimene mukufuna kuphunzitsa. Pa zokonzekera zanu, lembani mwandanda wachidule okhudza mfundo zimene mukufuna kuti muphunzitse

Zophunzitsa/thunthu: Thunthu ndi zinthu zimene mukufuna kuti muphunzitse. Mu phunziro limene Yesu anaphunzitsa mzimayi pachitsime, thunthu la uthenga wake linakhazikika pamadzi amayo. Linaonetsera gwero la madzi amayo komanso kusiyana kwa madzi amayo ndi madzi akuthupi. Yesu anaphunzitsanso zinthu zoyenera kuti munthu alandire madzi amoyo komanso zotsatira zomwa madzi amenewa.

Gwero la madzi amoyo:

Yesu anayankha nati kwa iye, Ukadadziwa mtulo wa Mulungu, ndi Iye amene alinkunena ndi iwe, Undipatse Ine ndimwe; ukadapempha iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo. (Yohane 4:10)

Kusiyana pakati pa madzi amayo ndi madzi akuthupi:

Yesu anayankha nati kwa iye, Yense wakumwako madzi awa adzamvanso Iudzu; koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha. (Yohane 4:13-14)

Machitidwe oyenera:

koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha. (Yohane 4:14)

Njira yachidule ya dongosolo la chiyambi ndi ili:

- I. Mfundo yoyamba yaikulu
 - A. Mfundo zoonjezera kufotokozera mfundo yoyamba.
 1. Mfundo yofotokozera yaing'ono
 2. Mfundo yofotokozera yaing'ono

B. Mfundo zina zoonjezera ku mfundo yoyamba

1. Mfundo yapadera yoonjezera

C. Mfundo zina zoonjera pa mfundo yoyamba.

II. Mfundo yachiwiri

(lembani mfundozi ngati mmene talembelera pamwambapa)

Onetsani kuti mfundo zanu zalembedwa mwadongosolo malingana ndi ndimene zimene musanthule kuchokera mu Baibulo. Mfundo zazikulu zikuyenera kugwirizana ndi mutu waphunziro komanso mfundo zoonjezera zikuyenera kugwirizana ndi mfundo zikuluzikulu.

Mfundo: mfundo zikuyenera kulumikizana ndi mfundo zi nzake. Koma kuchulukwa kwa mfundo kumasiyana malinga ndi phunziro limene mukufuna kuphunzitsa.

Kugwiritsa ntchito phunziro: kugwiritsa ntchito mau a Mulungu ndi pamene tikugwiritsa ntchito mauwo pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mupagwiritsa ntchito zimene mwaphunzira kunyengo zenizeni za moyo. Pamene choonadi chaphunzitsidwa, chikuyenera kugwiritsidwa ntchito mmoyo wathu komanso pa utumiki. Phunziro likuyenera kuyankha funso lakuti kodi zimenezi zikukhudza bwanji mowa wanga?

mu chitsanzo cha Yesu ndi mzimayi pachitsime, yesu anaphunzitsa za madzi amoyo komanso ndipo anaonetsera kufunika kwa zimenezi. Iye anamuuzza kuti madzi amoyo akhoza kukhala mwa iye komanso ndi kusintha moyo wake. Anamuonetsa mmene angapembedzere Mulungu weniweni mu mzimu ndi choonadi. Kugwiritsa ntchito phunziro limene mwaphunzira zikhoza kuchitika pofunsa ndi kuyankha mafunso pa zimene mwaphunzitsa kapena pa zimene aphunzira. Aloreni ophunzirawo kuti agwiritse ntchito zimene aphunzira paokha.

Kuonetsera kufunikwa kwa phunziro kukuyenera kuchokera pa zimene ophunzira amakumana nazo. Mukhoza kupeza zitsanzo kuchokera ku nkhani za mu Baibulo, anthu otchuka, nyimbo za m' buku komanso pakuwerenga mabuku ena. Anthu amaphunzira bwino ngati akutengapo mbali pakuphunzirapo. Chifukwa cha ichi ophunzira akuyenera kutenga nawo mbali ndi cholinga choti aphunzire moyenera.

Ngati mudziwa izi, odala inu ngati muzicita. (Yohane 13:17)
(Werenganinso Yakobo 5)

Mukhoza kuuza ophunzira anu kuti achite ntchito ndi cholinga choti athe kugwiritsa ntchito zinthu zimene aphunzira. Mu mndanda wanu ophunzitsira lembani zinthu zimene mukufuna kuti ophunzira anu achite.

Mathero: mathero ndi pamene pamathera phunziro lanu. mapeto aphunziro lanu akuyenera kukhala ndi mfundo zikuku zikulu zimene mwaphunzitsa muphunziro. Koma mathero sakuyenera kukhala malo ongobwereza zimene mwaphunzitsa ayi. Mukhoza kugwiritsa ntchito mfundo zimene zaperekedwa mu chaputala 5 ndi 6 kuti mubwerenze phunziro lanu. Kubwerenza

ndi kofunika kwambiri. Nthawi zambiri Yesu amabwereza choonadi chazimu chifukwa izi zimathandiza kuti ophunzira akumbukire zimene aphunzira.

Mathero aphunziro lanua akuyenera kulora ophunzira kuti ayankhulepo. Nthawi zonse Yesu akamaliza phunziro lake, iye amafunsa anthu mafunso kapema maganizo awo. Pa chitsime paja, Yesu anafunsa mzimayi uja kuti akaitane amuna ake. Izi zinapangitsa kuti iye alape. Ndi zosakwanira kuti munthu angomva mau chabe. Ndi zofunika kuti tithe kugwiritsa ntchito zinthu zimene zaphunzitsidwanzo mmoyo wathu.

Ndi pokhapokha pamene choonadi chikugwirizana ndi ife pamene tingathe kuchigwiritsa ntchito choonadicho. Choncho tikuyenera kudziwa mmene choonadicho chikugwilira ntchito kwa ife kuti tichitepo kanthu.

Pamene pagwa vumbulutso, munthu akuyenera kuchitapo kanthu. Ngakhale chidziwitso choti Mulungu wadzionetsera yekha mu chilengedwe zikulira kuti tichitepo kanthu ngati anthu:

Pakuti Mulungu ali mboni yanga, amene ndimtumikira mu mzimu wanga, m'Uthenga Wabwino wa Mwana wace, kuti kosalekeza ndikumbukila inu, ndi kupempha masiku onse m'mapemphero anga, (Aroma 1:19-20)

Chitsanzo cha kuchitapo kanthu titatha kuphunzira ndi kuvomelereza kuti Yesu ndi ambuye, kubwera kuti mulandire pemphero la machiritso, ubatizo wa mzimu Woyera kapena kulapa machimo kumene. Anthu sakuyenera kuchitapo kanthu pa uthenga pamene walalikidwa chifukwa chakungotengeka. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti Yesu ananeneratu kuti kuvomereza Uthenga Wabwino sichinthu chophweka (Marko 8:34-35)

Muyenera kupanga chiganizo ngati zolinga zanu zakwaniritsidwa pa ophunzira anu. Kodi muwapatsa ophunzira anu mayeso kapena ntchito yoti apange? Lembani mwachidule mathero a phunziro lanu. Kumbikirani kuitanira ophunzira kuti achitepo kanthu pazimene aphunzira komanso mmene mukufunira kuti ophunzira anu achitire akaphunzira phunziro lanuro.

STEPE 6- sankhani njira komanso zothandiza pophunzira:

Sankhani njira zimene mugwiritse ntchito pophunzitsa ndipo zina mwa njira zimene mungathe kugwiritsa ntchito ndi izi:

- Kuchokera kumfundo zodziwika kupita ku mfundo yosadziwika
- Kuchoka mfundo yaing'ono kupita ku mfundo yaikulu
- Zophunzitsira zooneka ndi maso
- Mafunso ndi mayankho
- Mafanizo
- Kuonetsera zimene mukuphunzitsa
- Kugwiritsa ntchito malemba

- Kusiyanitsa zinthu
- Kugwiritsa ntchito nyengo za anthu

Onetsetsani kuti njira zimene mwasankha ndi zogwirizana ndi anthu amene mukufuna kuwaphunzitsa. Gwiritsani ntchito njira zimene ophunzira atenganawo gawo pophunzira.

STEPE7- Bweretsani pamodzi zinthu zophunzitsira

Bweretsani pamodzi zinthu zonse zimene mugwiritse ntchito pophunzitsa. Zina mwa zinthu zimenezi ndi zimene mwalemba, zothandizira kuphunzitsa ndi zinthu zonse zimene zingakuthandizeni kuti mukachite zonse zimene mwakonza.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi ndi zithu ziti zimene zimapezeka mu phunziro lilironse?

3. Tchulani magawo anayi okonzekera kuphunzitsa amene takambirani mu phunziro ili?

4. Tchulani ma stepe onse akukonzekera kuphunzitsa:

Stepe 1 _____

Stepe2 _____

Stepe3 _____

Stepe4 _____

Stepe5 _____

Stepe6 _____

Stepe7 _____

5. Gwiritsanzi ntchito mndandanda umene waperekedwa mu gawo la zoonjezera pophunzira kuti mukonzekere kuphunzitsa.

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa phunziro ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Cholinga chimodzi chophunzitsa ndikuthandiza ophunzira kuti alandire kapena kuvomereza Yesu ngati mhulumutsi wao. Cholinga chimenechi ndi chotheka ngakhale pakati pa ana. Izi ndi zotheka ngati mwanayo wafika pa nsinkhu oti okhoza kupanga chiganizo payekha.
 - Chitsanzo cha ana amene anabwera kwa Mulungu ndi Yosefe, Samueli, Yeremiya, Danieli, Yohane ndi Timoteyo.
 - Munthu akhoza kutembenuka mtima akadali wachichipere: Mateyu 18:3.
 - Kudzichepetsa ndi chikhalidwe chimodzi chimene ana ali nacho chimene chimawathandiza kuti akhoza kubwera kwa ambuye kapena kulandira uthenga wabwino: Mateyu 18:4
 - Mwana wang'ono akhoza kukhulupilira: Mateyu 18:6.
 - Mwana ndi wantengo wake pamaso pa Mulungu 18:10
 - Yesu anali akukamba za ana pamene anali akukamba za nkhosa yosochera imene inapezeka: Mateyu 18:12,13
 - Sichifuniro cha atate kuti kuti mwana mmodzi ataike.
2. Pezani zinthu zimene zikupezeka mu chiphunzitso cha Yesu kwa Nikodemo pa Yohane 3

Kupezeka kwa Mulungu:

Mphuzitsi

Ophunzira

Chilankhulo

Phunziro

Njira

3. Unikirani ndondomeko ya ziphunzitso zina zimene Yesu anaphunzitsa mu Baibulo. Ndipo gwiritsani ntchito mafunso awa:

Chiyambi: kodi ndi njira zANJI zimene anagwiritsa ntchito kuti anthu akhale ndi chidwi?
Kodi iye amayamba bwanji phunziro lake?

Thunthu la Uthenga wake: kodi ndi choonadi chiti chimene iye anaphunzitsa? Kodi ndi njira ziti zimene iye anagwiritsa ntchito pofuna kuphunzitsa?

kugwiritsa ntchito: kodi iye anagwiritsa ntchito bwanji choonadi mu moyo wanthu omvera kapena kuti ophunzira.

Mathero: kodi Yesu amamariza bwanji uthenga wake? Ndipo kodi iye amafuna anthu kuti achite chiani akamva uthenga wake?

4. Gwritsani ntchito mdandanda uli munsiu kuti mukonzekere kuphunzitsa phunziro.

MNDANDA WA KUKONZEKERA PHUNZIRO

Mutu waphunziro:

Malemba: _____

Kuunikira ophunzira: Lembani mwachidule zimene mukudziwa zokhudza ophunzira

Zolinga: pamapeto pa phunziro ili ophunzira akuyenera kukwanitsa zinthu izi:

Mndanda waphunziro

Chiyambi: kodi ndiyamba bwanji phunziroli?

Thunthu: (mndanda wa mfundo zikuluzikulu):

Kagwiritsidwe ntchito: Kodi ndigwiritsa ntchito bwanji zinthu zimenezi pa moyo wa ophunzira:

Mathero: konzekerani zinthu izi:

Kufotokozero mwachidule phunziro lanu:

Unikirani phunziro lanu: kodi muunikira bwanji phunziro lanu ngati ophunzira aphunziradi moyenera kapena ngati zolinga za phunziro zakwaniritsidwa.

Kuitanira anthu kuti achitepo kanthu: kodi muwauza ophunzira kuti achite chiyani atamva uthenga wabwino.

Njira zophunzitsira: njira zophunzitsira zimene zigwire ntchito mu phunziro lino ndi izi:

- Zina mwa njira zimene mungagwiritse ntchito ndi izi:
 - Kuchokera kumfundo zodziwika kupita ku mfundo yosadziwika
- Kuchoka mfundo yaing'ono kupita ku mfundo yaikulu
- Zophunzitsira zooneka ndi maso
- Mafunso ndi mayankho
- Mafanizo
- Kuonetsera zimene mukuphunzitsa
- Kugwiritsa ntchito malemba
- Kusiyantsa zinthu
- Kugwiritsa ntchito nyengo za anthu

Zina mwa njira ndi izi:

Zothandizira pophunzira: zothandizira pophunzira zimene tingagwiritse ntchito ndi izi:

Zinthu zofunika kuti zipite mkalasi ndi izi:

Baibulo- zothandiza pophunzitsa ndi zina monga_____

CHAPUTALA 11

KUUNIKIRA PHUNZIRO

ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili mukuyera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokera tanthauzo la kuunikira
- Kufotokoza kufunika kounikira kaphunzitsidwe.
- Tchulani njira zinayi zounikira kaphunzitsidwe.
- Pezani zifukwa zobweretsa mavuto pakati pa ophunzira kapena aphunzitsi.
- Kuona mavuto ngati mwai osati zinthu zolepheretsa kapena zotchinga.

VESI YOTSOGOLERA

kuti mukayese inu zinthu zosiyana; kuti mukakhale a mtima woota ndi wosalakwa, kufikira tsiku la Kristu; (Afilipo 1:10)

MAU OYAMBA

Pakadali pano mwaphunzira mmene mungakhazikitsire zolinga za phunziro, komanso kaphunzitsidwe ka Baibulo pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana. Koma mungadziwe bwanji kuti maphunzitsidwe anu ndi oyenera? Komanso mungadziwe bwanji kuti zolinga zauzimu zimene mwakhazikitsa zikukwaniritsidwa. Mayankho amafunso onsewa amayankhidwa kudzera mukuunikira phunziro lanu.

KUUNIKIRA

Kuunikira ndi ndondomeko yosanthula mosamalitsa chinthu chinachake. Pamene mukuunikira maphunzitsidwe mumakhala kuti mukuunikira ngati utumiki wanu ndi opinduritsa. Ndi zofunika kuti muunikire maphunzitsidwe anu ngati mukufuna kuti muchite bwino pa mphatso imene Mulungu anakupatsani. Paulo analankhula kuti:

kuti mukayese inu zinthu zosiyana; kuti mukakhale a mtima woota ndi wosalakwa, kufikira tsiku la Kristu; (Afilipo 1:10)

NSANAMIRA ZA KUUNIKIRA KUPHUNZIRA

Kuunikira kuphunzitsa kumakhazikika pa zinthu izi:

ZOLINGA:

mukhoza kuunikira kuphunzitsa poyang'anira zolinga. Kodi zolinga zophunzitsa zinanakwaritsidwa ndi ophunzira? Mukuyenera kukhazikitsa zolinga zimene mukhoza kukwaniritsa ndi cholinga choti pamapeto pake mukhoza kuona ngati zakwaniritsidwa kapena ayi.

Yesu amakhazikitsa zolinga pa ophunzira ake ndipo pamapeto pake iye amaunikira ngati zolingazo zakwaniritsidwa.

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; (Marko 6:7,30) (weranganinso Luka 9)

MAYESO

Mayeso amagwiritsidwa ntchito pofuna kuyesa kapena kuona ngati ophunzira waphunziradi zimene anaphunzitsidwa. Mulungu amaphunzitsa komanso kutipatsa mayeso kudzera mu nyengo zamoyo wathu. Yesu amaunikira ophunzira ake kudzera mu mayeso.

Pamenepo Yesu, pokweza maso ace, ndi kuona kuti khamu lalikuru lirinkudza kwa iye, ananena kwa Filipino, Tidzagula kuti mikate kuti adye awa? Koma ananena ici kuti amuyese; pakuti anadziwa yekha cimene adzacita. (Yohane 6:5-6)

Mwachitsanzo phunziro ili liri ndi gawo la mayeso odziyesa nokha. Koma mukhoza kuunikira ophunzira pogwiritsa ntchito mafunso ongoyankha pakamwa. Koma nthawi zina anthu amayesedwa kudzera munyengo zimene akudutsamo osati kungolembe mayeso kapena kufunsiidwa mafunso chabe.

MACHITIDWE A OPHUNZIRA:

Kuphunzira kumaunikiridwa malinga ndi zimene ophunzira akuyankha.

1. Kodi ophunzira amamvetsera zimene amaphunzira?
2. Kodi amayankha zinthu zimene amafunsiidwa kuti achite ndi aphunzitsi awo? Mwachitsanzo ngati chiphunzitsi chinali chokhudza chipulumutso kodi anthu amene ndi osamulumutsidwa anachitapo kanthu? Kodi ngati tinaitana anthu kuti abatizidwa kapena kulandira ubatizo wa Mzimu woyera, kodi iwo anachita bwanji? Ngati cholinga chaphunziro chinali choti ophunzira akule moyo wao wauzimu, kumbukirani kuti kukula moyo wauzimu sikumayesedwa malingana ndi zimene ophunzira amva koma zimene akukwnitsa kuchita pazimene amva.

KACHITIDWE KA APHUNZITSI

Mphuzitsi naye akuyenera kuunikira mmene wachitira. Gwiritsani ntchito mdandanda umene waperekedwa mu gawo la zoonjezera pophunzira kuti muunikire zimene mwaphunzitsa.

KUUNIKIRA ZOLEPHERETSA

Simukuyenera kukhumudwa ngati mwakumana ndi mavuto pakaphunzitsidwe kanu. Mavuto amene tawazindikira amatithandiza kuti tikonze mavuti amenewa. Ngakhale Yesu naye amakumana ndi mavuto pophunzitsa makamaka pa ubale wake ndi ophunzira ake. Ganizirani zinthu izi:

3. Werengani Luka 9:54-56. Pamene Yohane ndi Yakobo ataona kuti Yesu wakanidwa, iwo amafuna kut aitane moto kumwamba kuti uwonge anthuwo. Iwo sanamvetse uthenga Wa Yesu Khristu.

(Luka 9:56)

4. Pamene Yesu anayamba kuphunzitsa kuti anadza kuti afere machimo a anthu, Petro anadzudzula Yesu. Koma yesu anamukonza maganizidwe ake (Marko 8:31-33)
5. Ngakhale kuti Yesu anapereka ulamuliro kwa ophunzira ake kuti akhodza kuchotsa ziwanda, koma iwo analephera kutumikira kwa munthu ogwidwa ndi ziwanda (Marko 9:13-33)
6. Werengani Marko 10:35-45. Yokobo ndi Yohane anapempha ngati angaloredwe kukhala pambali pa Yesu mu ufumu wa Mulungu. Koma ophunzira ena anakhumudwa atamva izi. Koma nkhani ndi yakuti ophunzira onse a Yesu anali atasemphana ndi chiphunzitso cha Yesu Khristu.

Koma mwa inu sikutero ai; kama amene ali yense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la kwa anthu ambiri. (Marko 10:43-45)

7. Ophunzira anagona kwa ola limodzi pa nthawi imene Yesu amafuna kuti akhale naye mu pemphero (Marko 14:32-42)
8. Ophunzira mmodzi anamukana Yesu pamene wina anamupereka Yesu ndipo ophunzira otsala onse anamuthawa Yesu iye atamangidwa (14:43-72)
9. Mwini chuma wachichepere anakana kutsata Yesu (Marko 10:17-22)

Chifukwa chakuti Yesu analibe ntchito, mavuto amene amakuna nawo pakati pa iye ndi ophunzira ake sikuti amayamba chifukwa cha iye. Mavuto amabwera chifukwa cha ophunzira ake. Mulungu salephera chomwechonso mau ake salephera ngakhale Yesu amene salephera. Pamene pali mavuto pakati pa ophunzira ndi mphunzitsi, pali magawo awiri amene akuyenera kuunikidwa. Zimakhala kuti vuto liri ndi ophunzira kapena mphunzitsi.

Zina zimabweretsa mavuto pakati pa ophunzira ndi aphunzitsi ndi izi:

APHUNZITSI:

Zolinga sizinakhazikitsidwe ndipo palibe zimene zinakwaniritsidwa.

Sanaunikire bwino ophunzira: aphunzitsi sanakonzekera malinga ndi chikhalidwe, maphunziro kapena uzimu wa ophunzirawo.

Aphunzitsi sanakonzekere: sanakhale ndi nthawi yokwanira kuti akonzekera kuphunzitsa.

Sanapemphere: analibe nthawi yokwanira yopemphelera phunziro komanso ophunzira.

Njira zosayenera: Njira zimene zinagwiritsidwa ntchito ndi zosagwirizana ndi ophunzira. Mwina aphunzitsi sanaganizire za nsinkhu komanso chikhalidwe cha ophunzira.

Kukhazikitsa mwambo: panalibe mwambo ndipo chifukwa cha ichi zinali zovuta kuti ophunzira akhale ndi chidwi pophunzira.

Kuphunzitsa kusayenera: aphunzitsi amalankhula mwansanga kapena pang'onopang'ono, mwina amakuwa kwambiri kotere kuti zinali zovuta kuti athe kumvedwa.

OPHUNZIRA

Kusakhulupirira: Yesu sanakwanitse kutumikira kwa anthu amu mzinda wake chifukwa cha kusakhulupirira kwa anthuwo (Mateyu 13:58)

Mbeu ya Mau a Mulungu sinagwere pa nthaka yabwino. Werenga fanizo la munthu ofesa pa Mateyu 13:1-9,18-23. Satana analanda mau, mau amafota pamene munthu ayamba kusamala za mavuto amoyo uno.

Kusamvetsera: Ophunzira samvetsera chifukwa cha zinthu zolepheleretsa kapena kusowa kwa bata mkalasi. Anamulora Satana kuti alande mau a Mulungu mkati mwao (Mateyu 13:19)

Kukana kuchitapo kanthu: ophunzira anasankha kuti asachite kanthu pa mau a Mulungu. Anamva mau a Mulungu ndipo sanawakane koma anasankha kusawagwiritsa ntchito mauwao m'moyo wao (werengani Yakobo 1:22-25). Ili linali vuto la mwini chuma wachichepere amene anakana kutsata Mulungu chifukwa cha chuma chake (Marko 10:17-22)

Kukana uthenga: nthawi zina ophunzira amakana Uthenga. Izi ndi zimene zimachitika ndi ophunzira a Yesu pamene ena mwa iwo anamutembenukira iye (Yohane 6:53-66)

KUGWIRITSA NTCHITO MAVUTO

Simukuyenera kukhumudwa ndi mavuto pamene mukuphunzitsa. Muwagwiritse ntchito ngati chida choti muphunzire komanso kukonza zinthu zimene simukuchita bwino. Mavutowa akhoza kusintha pogwiritsa ntchito pemphero komanso kusintha machitidwe athu a zinthu. Aphunzitsi ndi ophunzira akhoza kukonza ndi kusintha mavuto ena.

Yesu sanawagwere ulesi ophunzira ake. Iye sanakhumudwe ndi zolakwitsa zawo komanso kulephera kwao. Iye amaona chimene iwo amayenera kukhala atamulora Mzimu Woyera kuti agwire ntchito mkati mwao. Ndipo pamapeto pake iwo anakhaladi anthu odalirika. Mu buku la Machitidwe tikuona anthu amantha komanso okaika akusandurika kukhala atumiki amphamvu a Mulungu.

Mukhoza kuona mavuto ngati mwai kapena ngati zinthu zolepheretsa. Koma ngati mungaone mavuto ngati chinthu chotchinga ndiye kuti mugwa mphayi kenako ndikulephera kapena kusiya kumene. Koma ngati mungaone mavuto ngati mwai, mukula moyo wanu wauzimu komanso mu ukadaulo wanu wakaphunzitsidwe ka Baibulo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Fotokozani tanthauzo la kuunikira

3. Kodi kuunikira kaphunzitsidwe kanu ndi kofunika bwanji?

4. Tchulani njira zinayi zounikira kaphunzitsidwe ka Baibulo

5. Fotokozera mwachidule zifukwa zobweretsa mavuto pakati pa ophunzira ndi aphunzitsi pakuphunzira

6. Kodi mungagwiritse ntchito bwanji mavuto moyenera?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

KUUDZIUNIKIRA NOKHA NGATI MPHUNZITSI

Mukuyenera kudziunikira nokha ngati mphunzitsi. Werengani mafunso ali pansipa ndipo zunguliza yankho limene mukuona kuti ndi loyenera. Onkhetserani mayankho amene mwapeza. Ngati mwapeza marikisi okwana 85 kupitsa mtsogolo ndiye kuti mwachita bwino ndipo ngati mwapeza 40 ndiye kuti simunachite bwino. Marikisi apakati pa 41 kufikira 60 akusonyeza kuti mwachita bwinbo pang'ono. 61 kufikira 84 akusonyeza kuti mwachitako bwino

KUKONZEKERA:

| | |
|--|------------|
| Ndimayamba kukonzekera phunzira langa kwa sabata imodzi isanafike nthawi yophunzitsa. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimagwiritsa ntchito kwambiri Baibulo pamene ndikukonzekera. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimakhala ndi dongosolo latsatanetsatane la phunziro langa. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimaganizira zosowa za ophunzira anga pamene ndikuophunzitsa. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimalemba zolinga za phunziro lina lilironse. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimalemba mnene phunziro likayendere. | 5 4 3 2 1 |
| Ndimapemphera pa zimene ndikufuna kuchita. | 5 4 3 2 1 |
| Nthawi zonse ndimafuna kuchita bwino kaphunzitsidwe kanga pakuwerenga ndi kuchita maphunzirammo ena. | 5 4 3 2 1. |

KAPHUNZITSIDWE

| | |
|--|-----------|
| Ndimakhala ndi chikoka cha ophunzira pachiyambi | 5 4 3 2 1 |
| Ndimawerenga uthenga wa Baibulo momveka | 5 4 3 2 1 |
| Ndimamaliza kuphunzitsa poitanira ophunzira kuti achitepo kanthu | 5 4 3 2 1 |
| Ndimagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana pophunzitsa | 5 4 3 2 1 |
| Ndimatsata mutu waphunziro kufikira kumapeto opanda kupita kwina | 5 4 3 2 1 |
| Ndimatsindika choonadi chachikulu | 5 4 3 2 1 |
| Ndimaonetsera kufunika kwa zimene zikuphunzitsidwa pa utumiki | 5 4 3 2 1 |

KACHITIDWE KA OPHUNZIRA

| | |
|---|-----------|
| Ophunzira anga amakhala ndi chidwi kuti asanthule Baibulo | 5 4 3 2 1 |
| Maphunzitsidwe anga amathandiza kusintha moyo wa anthu. | 5 4 3 2 1 |
| Chiphunzitso changa chimakhudza anthu otaika mwa Khristu | 5 4 3 2 1 |
| Chiphunzitso change chimathandiza kulimbikitsa kukula moyo wauzimu. | |

CHAPUTALA 12

KUPANGA NDI KUSANKHA NDONDOMEKO YA KAPHUNZITSIDWE(Curriculum)

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokoza ndondomeko yamaphunzira a Baibulo.
- Kufotokoza mfundo za ndondomeko za maphunziro a Baibulo.
- Kusankha ndondomeko ya maphunziro yoyenera
- Kukonza ndondomeko yanu yamaphunziro.

MA VESI OTSOGOLERA

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (II Timoteyo 3:16-17)

MAU OTSOGOLERA

Baibulo ndiye nsanamira ya kaphunzitsidwe konse mu mpingo. Koma olemba ena achikhristu alembapo zinthu zambiri zimene zingathandize pophunzitsa. Phunziro ili likhazikika pa kasankhidwe kwa ndondomeko ya maphunziro a Baibulo.

NDONDOMEKO YA MAPHUNZIRO A BAIBULO

Mau akuti karikulamu kapena kuti ndondomeko ya maphunziro amatanthauza zinthu zimene anthu akuyenera kuphunzira. Mau amenewa amaimira maphunziro onse amene anthu akuyenera kuphunzira pa sukulu. Pamene tikakamba za kalikulamu ya Baibulo tikutanthauza maphunziro onse amene anthu akuyenera kuphunzira pa nkhani za Baibulo.

MAZIKO A MAPHUNZIRO A BAIBULO

Ndondomeko ya maphunziro a Babulo ndi nsanamira yofunika kwambiri pa kuphunzitsa maphunziro a chikhristu. kufunika kwa izi ndi uku:

- Zimapereka mwai wa kafukufuku wa Baibulo amene munthu payenkha sangathe kukhala ndi nthawi yokwanira kuchita.
- Zimapereka maphunziro olembedwa komanso zinthu zimene opunzira akuyera kuchita.
- Zimapereka mndanda wa zinthu zimene zikuyenera kuphunzitsidwa.
Zimafotokoza mfundo zimene mungathe kutsata kuti muphunzitse.
- Ndondomeko zina zamphunziro zimafotokoza zolinga za phunziro linalilironse.

- Ndongomeko zambiri zamaphunziro zimakonzedwa malinga ndi nsinkhu wa anthu. Zimalembedwa ndi anthu amene anaphunzitsidwa ukadaulo ogwira ntchito ndi anthu amasinkhu ya anthu ena ake.
- dondosolo la maphunziro limapereka mwai oti anthu aphunzire zinthu zambiri zokhudza Baibulo. Nthawi zambiri aphunzitsi a Baibulo amatsindika kuphunzitsa zinthu zimene iwo amakonda kapena zimene zimakhala zosavuta kuphunzitsa kwa iwowo. Pamene dongosolo lamaphunziro a Baibulo limakhudza magawo ambiri a Baibulo osati magawo okhao okodweretsa kwa aphunzitsi
- Limapereka mwai otha kuyendetsa maphunziro a anthu amagulu osiyanasiya

KASANKHIDWE KA NDONDOMEKO YA MAPHUNZIRO (KALIKULAMU)

Chinthu chofunika kukumbikira ndi chakuti ndondomeko yamaphunziro yolembedwa ndi anthu ilibe ulamuliro omaliza pamoyo wathu. Baibulo ndi bukhu lokhalo limene liri ndi ulamuliro pa aphunzitsi. Chifukwa cha ichi, ndondomeko ya maphunziro a Baibulo ikueyenera kuunikiridwa bwino ngati ikugwirizana ndi zimene Baibulo limaphunzitsa.

Zina mwa ndondomeko zothandiza kusankha ndondomeko ya maphunziro ndi izi:

- Ngati mpingo wanu ndi gawo limodzi la mipingo imene ili ndi chikhulupiliro chimodzi. Mukhoza kugwiritsa ntchito ndondomeko ya maphunziro amene mipingo yanu imagwiritsa ntchito. Komanso mukhoza kugwiritsa ntchito maphunziro a Harvestime International pa maphunziro anu.
- Pamene mukudikira kuti mupeze ndondomeko ya maphunziro anu, lembani zolinga za maphunziro amene mukufuna kuti kupereka kwa gulu la anthu limene mukufuna kuliphunzitsa.
- Pamene mwapeza kapena kulandira zinthu zimene muziphunzitsira, unikirani maphunziro amenewa. Ngati pali anthu ena amene adzakuthandizeni kuphunzitsa anthu amenewa akuthandizeni kuunikira maphunziro amene mudzaphunzitsese.
- Mukuyenera kuphunzitsa anthu ena mmene agwiritsire ntchito ndondomeko ya maphunziroyo.

KAKONZEDWE KA NDONDOMEKO YA MAPHUNZIRO

Ngati mulibe ndalama zoti mukhoza kugula ndondomeko ya maphunziro, mukhoza kupanga ndondomeko yanu panokha ya maphunziro. Mu chaputala 10 mwapunzira mmene mungakonzekera maphunziro a Baibulo. Gwiritsani ntchito zimene mwapunzira mu chaputala chimenechi kuti mukonze maphunziro angapo. Zimenezi ndi zimene mungagwiritse ntchito kuti muphunzitsire maphunziro anu a Baibulo. Phunzitsani pogwiritsa ntchito maphunziro amene mwakonza kuti muone kufooka komanso mphamvu yake.

Zimatenga nthawi kuti mupange ndondomeko yamaphunziro kusiyana ndi kugula. Koma kupanga nokha zili ndi ubwio wake:

- Mumapanga maphunzirowo malingana ndi chikhalidwe cha anthu amene mukufuna kuwaphunzitsa.
- Mutsikimikiza pa zimene mukuphunzitsa ngati zikugwirizana ndi Baibulo.
- Mukhoza kukonza ndondomeko kuti ikumane ndi zosowa zanu zauzimu.

KUUNIKIRA NDONDOMEKO YANU YAMAPHUNZIRO

Gwiritsani ntchito ndondomeko zili munsimuzi kuti muunikire maphunziro anu.

ZINTHU ZOPHUNZITSIRA:

Zolinga:

- Kodi ndi zolinga ziti zimene mwakhazikitsa?
- Kodi zolinga zimene mwakhazikitsa ndi zogwirika kotero kuti mukhoza kuona ngati zakwaniritsidwa kapena ayi.

Zinthu zophunzitsa:

- Kodi zimene mukuyenera kuphunzitsa zikugwirizana ndi Baibulo?
- Kodi ndi zogwirizana ndi chikhalidwe chanu?
- Kodi zikugwirizana ndi msinkhu wa ophuzira anu?
- Kodi kutanthauziridwa kwa Baibuloko ndi kogwirizana ndi nsinkhu wa anthu amene adzagwiritse ntchito maphunzirowo. (maphunzirowo sakuyenera kukhala ophweka kwambiri kwa anthu akulu komanso ovuta kwambiri kwa ophunzira achichepere)
- Kodi zimene zikuphunzitsidwa zikuthandiza ophunzira kuzindikira tanthauzo la kukhala mbali imodzi ya anthu okhulupilira, komanso mbiri ndi zolinga cha mpingo?
- Kodi zimene zikuphunzitsidwa zikuthandizira zimene mpingo wanu umachita.

Moyo watsiku nditsiku:

- Kodi zimene zikuphunzitsidwa zikugwirizana bwanji ndi moyo wathu watsiku ndi tsiku wachikhristu? Kodi zikugwirizana ndi zolinga zimene mwakhazikitsa?
- Kodi zimene mukufuna kuphunzitsazo zikugwirizana ndi moyo wachikhristu wa tsiku ndi tsiku?
- Kodi maphunzirowo akupereka mwai oti anthu akhoza kulingalira mozama za moyo wachikhristu?
kodi maphunzirowo akuthandizira bwanji moyo wachikhristu pa banja, mmudzi ndi komanso padziko lapanse?

Kalembedwa kamaphunziro:

- Kodi mabuku amaphunzirowo alembedwa mopatsa kaso?
- Kodi phunziro lina lilironse mu buku lalembedwa momveka bwino kwa aphunzitsi?

- Kodi pali zinthu zina zimene ndi zothandiza aphunzitsi kuti amvetse zimene ayenera kuphunzitsa?
- Kodi ndondomeko zakaphunzitsidwe zaperekedwa? Ndipo ndi njira ziti zimene ndi zosavuta kugwiritsa ntchito pakati pa aphunzitsi?
- Kodi ndomeko za ntchito zochita pophunzitsa ndi zomveka bwino?
- Kodi pali zinthu zina zophunzitsira zimene zaperekedwa kuti mutha kuwerenga? Ndipo ndi ziti zimene mungazipeze mosavuta komanso zimene zili zoyenera?
- Kodi pali zina zoonjezera zimene zingathandize aphunzitsi kuphunzitsa mozama?

ZOTHANDIZA OPHUNZIRA KUPHUNZIRA

Mabuku owerenga:

- Kodi mabuku ali ndi zojambula ngati ndi olembedwa kupita kwa ana?
- Kodi malembo amabuku ndi osavuta kuwerenga kwa mwana?
- Kodi kalembedwe kabuku ndi kopatsa chikoka kwa mwana kuti akhoza kuwerenga?
- Kodi nkhani zili mmabuku ndi nkhani zoti mwana akhoza kuwerenga?

Buku la ntchito:

- Kodi ntchito imene yaperekedwa ndi yosangalatsa kwa mwana?
- Kodi ntchitoyo ndi yovuta kwa mwana kapena yophwekwa kwambiri?
- Kodi ithandiza kuti amvetse phunzirolo bwino?

Buku lofokozera ntchito:

- Kodi ndi zinthu ziti zimene zingakhale zapafupi kugwiritsidwa ntchito?
- Kodi zinthuzo ndi zabwino bwanji?
- Kodi ana akhoza kusangalatsidwa ndi ntchito zimene apatsidwa kuti achite kapena kuti pakhoza kukhala zina zimene akhoza kupatsidwa kuti achitenso?

MFUNDO ZIKULUZIKULU ZA NDONDOMEKO YA MAPHUNZIRO

- Kodi cholinga chenicheni ndi chiani kwa zaka 6 kufikira zaka 12?
- Tchulani zinthu zimene zikuyenera kuphunzitsidwa kwa zaka 12
- Onani mmene zinthu zophunzitsa zikuyendera?
 - Kodi zinthu zokhuza Baibulo zalembedwa mwadongosolo?
 - Kodi ubwino ndi kuipa kwa ndondomeko imene mwatsata ndi chiani?
 - Kodi pali kubwereza kwa zinthu zophunzitsa?
 - Kodi kubwerenza kumene kwachitika kukuthandiza kuphunzira?

- Kodi mitu yakaphunzitsidwe yaikidwa malinga ndi nyengo ya zinthu?
- Kodi mtengo wa zinthu zophunzitsira ukugwirizana ndi kapezedwe kanu ka ndalama?
- Kodi ndi zotheka kuti pakhoza kukhala kuchotsa zinthu zina koma osasokoneza maphunziro?

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Fotokozani tanthuazo la ndondomeko ya maphunziro a Baibulo(kalikulamamu)

3. Kodi nsanamira za maphunziro a Baibulo ndi chiani?

4. Kodi mukhoza kukhazikitsa ndondomeko yanu ya maphunziro a Baibulo?

(Mayankho amafunso odziyesa nokha ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani ndondomeko ili munsiyi ya mmene ndondomeko ya maphunziro amakono imapangidwira.

NDONDOMEKO YAMPUNZIRO YA MAKONO

Pali mfundo zinayi zimene zimatsatidwa popanga mfundo zamaphunziro zamakono. kuti muunikire ndondomeko zamaphunziro zimenezi, mukuyenera kuunikira ubwino ndi kuipa kwa ndondomeko ina ili yonse malinga ndi zolinga zanu zamaphunziro.

MAPHUNZITSIDWE OFANANA:

Kakonzedwe ka ndondomeko ya maphunziro:

Ndime yomweyo ya Baibulo imaphunzitsidwa kwa anthu amisinkhu yosiyana.

Ubwino wake:

1. Mpingo onse umatha kubwera pamodzi ndi kuchita chipembedzo
2. Anthu abanja limodzo akhoza kukambirana zinthu pamodzi kunyumba.

Kuipa kwake:

1. Nthawi zambiri maphunziro ambwerezedwa mukudutsa kwa nthawi makamaka pakadutsa dzaka 5-7 zimene sizithandiza kuti anthu aphunzire zambiri zokhudza Baibulo?
2. Maphunziro ena amakhala osagwirizana ndi nsinkhu wa anthu ena.

MAPHUNZITSIDWE OFANANDA PA MUTU:

Ndondomeko ya maphunziro:

Zinthu zokhudza Baibulo pa mutu umodzi zimaphunzitsidwa kwa anthu osiyana misinkhu.

Ubwino wake:

1. Anthu osiyana akhoza kukumana ndi phunzira zinthu zofanana.
2. Ngakhale kunyumba anthu akhoza kupitilira kukambirana.

Kuipa kwake:

1. Chifukwa chokambirana mfundo zofanana zimakhala zovuta kuti Baibulo lonse liphuinzitsidwe.
2. Maphunzirowo nthawi zina zamakhudza zosowa za ophunzira:

MAPHUNZIRO OSIYANA AMAPEREKEDWA KWA ANTHU OSIYANA:

Dongosolo la maphunziro amenewa:

Zinthu zosiyana zokhudza Baibulo zimaperkedwa kapana kuphunzitsidwa kwa anthu osiyana.

Ubwino wake:

1. Zonse zimene zimaphunzitsidwa zimakhala zogwirizana ndi gulu la anthu limene likuphunzitsidwa.
2. Phunziro limakonzedwa malingana ndi zofuna za anthu amene akupupunzitsidwa komanso zimene angakwanitse.

Kuipa kwake:

1. Zimakhala zovuta kuti anthu kunyumba apitirire kukambirana onse pamodzi chifukwa wina aliyense amakhala akuphunzira zogwirizana ndi msinkhu wake.

CHAPUTALA 13

KUPHUNZITSA ANTHU OSADZIWA KUWERENGA

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kuzindikira ophunzira osadziwa kuwerenga
- Kufotokozero mwachidule ndondomeko zophunzitsira anthu osadziwa kuwerenga.

VESI YOTSOGOLERA:

**Ciyambi ca nzeru ndico kuopa Yehova; Kudziwa Woyerayo ndiko luntha;
(Miyambo 9:10)**

Aphunzitsi ambiri amakumana ndi mavuto pophunzitsa ophunzira amene sadziwa kuwerenga ndi kulemba. Ngati muli ndi chikonzero choti muphunzitse anthu oterewa mukuyenera kuwerenga chaputala chimenechi koma ngati mulibe chikonzero chimenechi mukhoza kupita chaputala 14.

KODI AKHOZA KUPHUNZITSIDWA?

Sizimatengera kuti munthu achite kudziwa kulemba ndi kuwerenga kuti aphunzire.

Mwachitsanzo, kuphunzira chilankhulo ndi chinthu chovuta koma ana amaphunzira chilankhulo chamakolo awo asanadziwe kulemba ndi kuwerenga. Ndi zotheka anthu osadziwa kulemba ndi kuwerenga kuphunzira choonadi cha mau a Mulungu ngakhale kuti sangathe kuwerenga paokha mau a Mulungu.

Lamuro limodzi limene linaperekedwa linali loti mau aphunzitsidwe kwa anthu ena ndi pakamwa kapena kuti kuchokera pa mtima.

Ndipo mau awa ndikuuzanilero, azikhala pantima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansu m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pouka inu. (Deteronome 6:6-7)

Yesu anaphunzitsa opanda kulemba penapake. Iye sanaperekeko kwa ophunzira ake zinthu zolembedwa kuti awerenge kapena kuuza ophunzira ake kuti awerenga Baibulo.

Tikhoza kuganizira kuti Yesu anaphunzitsa anthu amene anali osauka ndipo chifukwa cha kusauka kwao ambiri mwa iwo analibe mwai wamaphunziro. Anthu amenewa samalemba kapena kuwerenga zimene Yesu amaphunzitsa. Iwo amangodalira zimene amva Yesu akuphunzitsa.

Ngati muli ndi chikonzero choti muphunzitse uthenga wabwino kwa anthu onse, mukuyenera kukhala ndi dongosolo loti mufikire anthu amene sadziwa kulemba ndi kuwerenga. Izi zili chomwechi chifukwa simungafikire munthu wina aliyense ndi uthenga olembedwa ndipo sitinganene kuti anthu adziwe kaye kuwerenga ndi kulemba asalandire mau a Mulungu. kuphunzira mau a Mulungu sizimatengera maphunziro athu, zimatengera mmene mtima wathu uliri.

Ciyambi ca nzeru ndico kuopa Yehova; Kudziwa Woyerayo ndiko luntha; (Miyambo 9:10)

KUPHUNZITSA ANTHU OSADZIWA KULEMBA NDI KUWERENGA

Zina mwa ndondomeko zimene mungatsate kuti muphunzitse anthu amenewa ndi izi:

GWIRANI NTCHITO NDI ATSOGOLERI A M'DERA

Anthu osadziwa kulemba ndi kuwerenga nthawi zambiri amamvera atsogolero awo. Ngati atsogoleri a anthu angalandire Uthenga zimakhala zosavuta kuti muwafikire anthu ena onse. Pamemene atsgolera alandira uthenga, zimakhala zosavuta kwa iwo kuti afotokozere anthu ena chifukwa anazolowera kupereka uthenga popanda kulemba.

UTHENGA WANU IKUYENERA KUKHALA OGWIRIZANA NDI CHIKHALIDWE

Mwaphunzira kale kuti uthenga umene ndi ogwirizana ndi chikhalidwe cha anthu umakhala ndi chikoka kwambiri. Chitani kafukufuku wa chikhalidwe cha anthu amene sadziwa kulemba ndi kuwerenga. Kodi ndi zinthu ziti za moyo wa tsiku ndi tsiku ndi tsiku zimene zimawakhudza kwambiri? Kodi ndi mavuto ati amene awakhudza kwambiri muchikhalidwe chao? Chonco uthenga wanu ukuyenera kukumana ndi zinthu zimene zimawakhudza tsiku ndi tsiku.

GWIRITSANI NJIRA ZOPHUNZITSIRA ZIMENE NDI ZOGWIRIZANA NDI CHIKHALIDWE CHA ANTHU:

Zikhalidwe zambiri zili ndi njira zachikhalidwe zimene amagwiritsa ntchito pofuna kupereka Uthenga. Ena amachita izi kudzera mu nkhani. Ndipo enamapereka mauthenga kudzera mu nyimbo zimene zimapereka uthenga. Chitani kafukufuku wa chikhalidwe chimene mukufuna kutumikira ndipo pezani njira zimene anthuwo amagwiritsa ntchito pofuna kupereka mauthenga.

KUGWIRITSA NTCHITO ZINTHU ZIMENE ZAWAZUNGULIRA ANTHU:

Gwiritsani ntchito zinthu zimene zawazungulira anthu amene samadziwa kulemba ndi kuwerenga. Gwiritsani ntchito zina mwa zinthu zimene zimapezeka pakati pawo ngati zinthu zimene mungagwiritse ntchito pophunzitsa. Kumbikirani kuti Yesu amagwiritsa ntchito zinthu ngati miyala, maluwa, mbeu, nsomba ndi zina zambiri pophunzitsa. Mukhoza kupanga mafanizo anu amakono kuti muonetse choondai. Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo amene amakhudza zinthu ngati kuwedza nsomba chifukwa izi zinali zinthu zimene ophunzira ake amadziwa. Koma mwina ophunzira anu mkovuta kuti amvetse zina mwa zinthu zimenezi. Chitani kafukufuku wa malo emene anthu osadziwa kulemba amakhala ndipo gwiritsani ntchito zinthu zimene zawazungulira.

BWEREZANI MFUNDO ZIMENE SOZOVUTA:

Phunziro lanu likuyenera kukhala losavuta. Gwiritsani ntchito mfundo zosavuta ndipo mubwereze mfundo zimenezi kuti ophunzira anu amvetsetse. Muwafunse ophunzira anu kuti abwereze mfundo zimene mwawaphunzitsa.

FOTOKOZERANI MWACHIDURE

Fotokokozerani mwachidule mfundo zimene mwaphunzitsa potsindika mfundo yaikulu. Mwachitsanzo, ngati mukuphunzitsa mfundo yakubadwa mwatsopano kuchokera pa Yohane 3, mukhoza kutsiriza phunziro lanu ndi mau akuti mukuyenera kubadwa mwatsopano. Mukhoza kufotokozerana kuti munthu amabadwa mwatsopo pakulapa machimo ake ndi kuvomereza Yesu ngati mpulumutsi.

FUNSANI MAFUNSO:

Pamene mwamaliza kuphunzitsa, funsani mafunso kuti muone ngati amvetsetsa mfundo zimene mwaphunzitsa.

FUNSANI KUTI ACHITEPO KANTHU:

Njira imodzi yofuna kudziwa ngati ophunzira amva zimene aphunzira ndikuwafunsa kuti achitepo kanthu pa zimene aphunzira. Mwachitsanzo, ngati mumaphunzitsa zokhudza Yohane 3 mukhoza kufunsa amene ali okonzeka kuti abadwense mwatsopano?

BAIBULO NDILO BUKU LA MULUNGU

Baibulo ndi mau a Mulungu amene amapita kwa anthu. Ndi buku limene muli mau ake a Mulungu kotere kuti cholinga cha Mulungu ndi chakuti anthu anse akathe kuliwerenga. Chifukwa cha ichi, atsogoleri ambiri achikhristu akhala akuphunzitsa anthu kuti adziwe kulemba ndi kuwerenga ndi cholinga chakuti anthu athe kuwerenga mau a Mulungu pa okha.

Ngati muli ndi chidwi ndi izi, werengani zambiri kugawo la zoonjezera pophunzira. Koma kumbukirani kuti sizikutengera kuti munthu amadziwa kulemba ndi kuwerenga kuti alandire uthenga Wabwino.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani ma vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi kusadziwa kulemba ndi chiyani?

3. Fotokozerani mwachidule mfundo zothandiza kuphunzitsa anthu osadziwa kulemba ndi kuwerenga.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pezani munthu amene sadziwa kulemba ndi kuwerenga kuti mugawane naye Uthenga Wabwino?
2. Ngati muli ndi chidwi chofuna kuthandiza anthu amene sadziwa kulemba ndi kuwerenga, lemberani mabungwe amene amathandiza magawo amenewa mu dziko lanu monga “Laubauch Literacy Society”

CHAPUTALA 14

MAPHUNZIRO A APHUNZITSI

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili, mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kupeza zinthu ziwiri zofunika zokhudza maphunziro a aphunzitsi.
- Kufotokoza njira zinayi zokonzekera maphunziro a aphunzitsi.
- Kufotokoza mmene mungapezera ophunzira a maphunziro a aphunzitsi.
- Kufotokoza mwachidule ndondomeko zochitira maphunziro aphunzitsi.
- Kufotokoza mwachidule ndondomeko zakagwiritsidwe ntchito ka aphunzitsi mu mpingo.
- Tchulani njira zounikira aphunzitsi.

VESI YOTSOGOLERA

cifukwa mau amene munandipatsa Ine ndinapatsa iwo; ndipo analandira, nazindikira kooni kuti ndinaturuka kwa Inu, ndipo anakhulupira kuti Inu munandituma Ine. (Yohane17:8)

Yesu anaphunzitsa ophunzira ndipo pamapeto pa zonse anawauaza nati:

cifukwa mau amene munandipatsa Ine ndinapatsa iwo; ndipo analandira, nazindikira kooni kuti ndinaturuka kwa Inu, ndipo anakhulupira kuti Inu munandituma Ine. (Yohane17:8)

Ndondomeko ya Baibulo ya kuchurikitsa ndi kuphunzitsa anthu amene akhoza kuphunzitsa ena (II Timoteo 2:2). Kuti mukwaniritse ichi, nthawi zonse mukuyenera kuphunzitsa aphunzitsi. Cholinga cha chaputala ichi ndifotokoza za kuphunzitsa aphunzitsi.

ZOFUNIKA ZIWIRI POPHUNZITSA

Pali zinthu ziwiri zimene ndi zofunika pophunzitsa anthu mu mpingo. Zinthu zimenezi ndi kuphunzitsa anthu amene sanaphunzitsidwe ndi kuphunzitsa anthu emene aphunzira kale.

KUPUNZITSA ANTHU AMENE SANAPHUNZIRE:

Awa ndi maphunzira amene amaperekedwa kwa okhulupilira asanayambe kutumikira ngati aphunzitsi mu mpingo. Awa ndi maphunziro amene amathandiza munthu kuti athe kuphunzitsa.

KUPHUNZITSA ANTHU OPHUNZIRA KALE:

Awa ndi maphunziro amene amaperekedwa kwa anthu amene ndi aphunzitsi kale mu mpingo ndi cholinga choti akuze mphatso yao yauphunzitsi. Yesu anapereka mitundu iwiri yonse yamaphunziro.

KUKONZEKERO MAPHUNZIRO A APHUNZITSI

Zina mwa ndondomeko zoyenera kutsata pa maphunziro a aphunzitsi ndi izi:

- Bweretsani atsogoleri auzimu ndi ndi abusa onse pamodzi mu mumpingo.
- Funsani anthu amene ndi aphunzitsi kale kuti athandize atsogoleri amene adzakwanitse kuphunzitsa anthu ena.
- Kumananai ndi atsogoleri kuti mupange zinthu izi:
 - Kukhazikitsa zolinga za maphunziro anu.
- Kukhazikitsa malo ndi tsiku limene maphunziro anu adzichitika.
- tsogoleri amene adziphunzitsa maphunziro anu.
- Zomuyenereza munthu kuti achite nawo maphunziro. Kodi ndi ndani amene akuyenera kubwera nawo kumaphunzirowo? Akuyenera kukhala munthu obadwa mwatsopano. Koma mukhoza kukhala ndi zinthu zinu zowayenereza anthu.
- Zomuyenereza munthu kuti amalize nawo maphunziro amenewa. Kuti mudziwe zambiri werengani gawo la zoonjezera pophunzira.
- Mtundu wa malo amene mukufuna kuchitira maphunziro anu. Pezani zambiri ku gawo la zoonjezera pophunzira.
- Ndalama zimene zifunika kuti mupereke maphunziro anu.
- Zinthu zimene mufune kuti muphunzitse. Phunziro limeneli mukhoza kugwiritsa ntchito kuti muphunzitse aphunzitsi koma mukhoza kuonjezera zina zapadera ndi cholinga choti mukwaniritse zolinga za maphunziro anu.
- Konzani kalenda ya mmene mudzikumanilana kwa chaka chonse. Ndipo pa kalenda yanu ya sukulu muonetse masiku, komanso malo amene mudzikumana.
- Konzani ndondomeko ya ntchito zimene aphunzitsi anu mukufuna kuti adzigwira. Mukhoza kupeza zambiri mu gawo la zoonjezera pophunzira.
- Konzani dongolo limene aphunzitsi onse akuyeenera kusaina kuti adzipereka pa ntchito imene apatsidwa kuti agwire.

KAPEZEDWE KA ANTHU KUTI APHUNZITSIDWE NGATI APHUNZITSI

1. Itanani aphunzitsi amene muli nawo kuti aphunzitsidwe.
2. Lengezani mmipingo zokhudza anthu amene ali ndi chidwi choti akhale aphunzitsi.
3. Lankulani ndi anthu amene munaona kuti ali ndikuthekera koti akhoza kukhala aphunzitsi.
4. Unikirani anthu amene awonetse chidwi choti apunzire ngati ali oyeneradi kuti aphunzitsidwe.
5. Adziwitseni anthu onse amene akwaniritse zinthu zowayenereza kuchita maphunzirao za malo ndi tsiku limene maphunziro ayamabe kuperekedwa.

KACHITIDWE KA MAPHUZIRO

Zina mwandondomeko zoyenera kutsata pochita maphunziro a aphunzitsi ndi izi:

6. Yambani phuziro lina lilironse mu nthawi yake.
7. Yambani ndi pemphero kuti Mulungu adzodze ophunzitsi ndi kutsekula mitima ya ophunzira.
8. Lembani maina anthu amene abwera kudzaphunzira. Ophunzira akuyenera kupezeka mu makalasi angapo kuti akwaniritse zowayeneraza kumaliza maphunziro.
9. Onenetsetsani kuti ophunzira wina aliyes ali ndi buku lokhudza zinthu zimene mukuphunzitsa.
10. Onenetsani kuti muli ndi zinthu zonso zoyenera kuti muphunzitse mphunziro lanu. Izi zikhoza kukhala zinthu ngati zothandiza pophunzitsa mabuku ndi zina zambiri. Gwiritsani njira zophunzitsira zimene mwaphunzira mu phunziro lino.
11. Apatsane ophunzira ntchito yoti achite musanakumane mumkumano wina. Zizi zikhoza kukhala zinthu ngati zoti akawerenge kapena kulemba kumene.
12. Sungani nthawi imene mwapatsidwa pokhapokha ngati mzimu woyera akulankhulani kuti muchite mosiyana ndi dongosolo.

KUIKA APHUZITSI MMALO OTI APHUNZITSE

Kuphunzitsa aphuzitsi kumakhala kopanda mpindu ngati anthuwo sangwiritsidwa ntchito yoti aphunzitse. Zina mwa ndondomeko zimene mungatsate kuti mugwiritse ntchito aphunzitsi mu mpingo ndi izi:

FUNSIRANI KWA ABUSA:

Kodi ndi gawo liti likufunika apunzitsi? Kodi ndi pati pamene akuona kuti munthu akhoza kuchita bwino? Abusa ndi munthu amene Mulungu anakhazikitsa mu mpingo kotere kuti iwo ali ndi udindo okonza dongosolo la maphunziro mu mpingo. Mwachitsanzo, mtumwi Paulo anachita bwino pa utimiki chifukwa chakuti Mulugu anamuitanira kuti atumikire gawo limene amachita limene linali kutumikira kwa anthu Amitundu.

ANTHU APATSIDWE NTCHITO MALINGANA NDI CHIDWI CHAWO:

Anthu ena alibe chidwi ndi utumiki wa ana. Pamena anthu ena samaona bwino kuphunzitsa akulu. Anthu amagulu onse akuyenera kuphunzitsidwa koma aphunzitsi ayenera kukhala ndi chidwi ndi gulu la anthu limene akuphunzitsa.

MWAYI UPEREKEDWE KUTI APHUNZITSI AYESELERE KUPHUNZITSA:

Aphunzitsi amene angoyamba kumene apatsidwe mwai oti aphunzitse pamene aphunzitsi akale palibepo. Komanso ongoyamba kumene aphunzitse limodzi ndi nkhalakale imene iyenera kuwonelera mmene akuphunzitsira. Pamapeto pa phunzirolo, mphuzitsi amene amaonelera akuyenera kupereka ndemanga za mmene mphuzitsi watsopano wachitira.

KUUNIKIRA KAPHUNZITSIDWE

Pamene mphuzitsi akuphunzitsa mu mpingo, utumiki wake ukuyenera kuunikiridwa mmene akuchitira pakadutsa kwa nthawi. Yesu anachita zomwezi ndi ophunzira ake pamene anawatuma kuti akatumikire. Iwo anafotokoza zonse zimene anachita (Marko 6:7 ndi 30). Kuunikira kumathandiza kuti ngati pali mavuto akonzedwe. Koma zimathandizaso aphunzitsi atsogoleri ampingo kuti athandize aphunzitsi awo kuti akule mu utumiki komanso mphatso yawo yauphunzitsi.

Zina mwa njira zothandizira kuunikira kaphunzitsidwe mu mpingo ndi izi:

1. Aphunzitsi akuyenera kuunikiridwa pogwiritsa ntchito ukadaulo umene waperekedwa pa chaputala 11. Choyamba aphunzitsi akuyenera kuziunikira okha komanso mapeto ake athandizane ndi wina kuunikira mmene amapuzitsira.
2. Unikirani anthu malinga ndi ntchito imene anapatsidwa kuti adzichita. Kodi anthu akukwaniritsa zimene anapatsidwa kuti adzichita?
3. Kodi akusunga malonjezani awo amene analonjeza kuti adzichita?
4. Yang'anirani kapena kuonelera aphunzitsi akuphunzitsa. Kodi akuphunzitsa mau a Mulungu kwa ophunzira awo? Kodi ndi zinthu ziti zimene akuyenera kusintha kuti achite bwino? Afototozereni zinthu zina zimene angathe kutsata.
5. Unikirani chipatso chawo. Baibulo limafotokoza kuti chipatso cha utumiki chikhoza kuoneka. (Luka 6:43-44)

Kumbukirani kuti kukonza mavuto komanso kuunikira maphunzitsidwe zikueyenra kuchitika mwachikondi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi ndi zinthu ziti ziwiri zofunika pophunzitsa aphunzitsi?

3. Fotokozerani njira zoyenera kutsata popangsa ndondomeko yopunzitsa aphuzitsi.

4. Kodi mungachite bwanji kuti mupeze ophunzira kuti achite maphunziro auphunzitsi?

5. Fotokozerani mwachidule ndondomeko zakachitidwe ka maphunziro a aphunzitsi

6. Fotokozerani mwachidule ndondomeko za kaikidwe kapena kagwiritsidwe ntchito ka aphunzitsi mu mpingo?

7. Tchulani njira zisanu zounikira mpunzitsi?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku lino)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Zinthu zili musimu zikufotokozeraz mwachidule zimene zaphunziridwa mu chaputala chimenechi. Mukhoza kugwiritsa ntchito kuti muphunzitse aphunzitsi.

1. Tchulani zolinga zomaphunziro anu:

2. Khazikitsani malo ndi nthawi imene mudzikumana pachaka (gwiritsani ntchito kalenda yanu kuti muchite zimenezi.
3. Khazikitsani zinthu zowayenereza anthu kuti achite nawo maphunziro a Baibulo: ophunzira ofunsira malo akuyenera kukhala ndi zinthu izi:
8. Obadwa mwatsopano.
9. Amene anabatizidwa mu ubatizo mwa mmadzi.
10. Odzala ndi Mzimu.
11. Akusonkhani ndi abale ena mu mpingo.’
12. Okhala ndi mbiri yabwino pakati pa abale.
13. Okwaniritsa zomuyenereza munthu kukhala mtsogoleri malinganda ndi Baibulo.
14. Zomuyenereza munthu kuti amalize maphunziro. Ndongomeko zina ndi izi:
15. Akuyenera kupezeka mu makalasi onse pokhapokha patakhala kuti pali chifukwa chomveka bwino chimene chaloredwa ndi aphuzitsi.
16. Akuyenera kulemba ntchito zonse zimene anapatsidwa ndi aphuzitsi.
17. Akuyenera kuphunzitsa phunzira limodzi moyang’aniridwa ndi munthu wina.
18. Ganizirani za malo amene mudziphuzitsira anthu. Ndongomeko zina zothandiza ndi izi:
19. Ngati aphunzitsi a pampingo amakumana kale, gwiritsani ntchito mwai umeneu kuti apitirize kukuza ukadaulo wao.
20. Mukhoza kuphunzitsa aphuzitsi nthawi ya Sunday sukulu pamene iwo akhoza kukhala ndi nthawi yao yapadera.
21. Kuphunzira payenkha: perekani buku limeneli kwa aphunzitsi kuti athe kuwerenga paokha ndi kumaliza phunziro.
22. Kakumanidwe: kumanani malinga ndi masiku amene mwakhazikitsa. Mwachitsanzo mukhoza kukumana kwa sabata imodzi imene mwaisankha kuti mukumane.
23. Pezani nthawi yopuma: Pezani nthawi yoti mupume imene mukhoza kuwatengera ophunzira anu malo apadera kumene akhoza kupepuza matupi awo ndi kusangalala.

24. Maphunziro a mipingo yosiyanasiyana. Mipingo yosiyanasiyana ikhoza kubwera pamodzi ndikuchita maphunziro a aphuzitsi mipingo yawo.

23. Sankhani mphuzitsi oti aphuzitse: kodi ndi madera ati amene adzaphunzitse, ndipo adzaphuzitsa nthawi yanji.

24. Kodi adzagwiritsa ntchito chiani pophunzitsa?

Dzina la phunziro _____

Dzina la buku limene adzaphunzitsire _____

25. Dongosolo la zachuma:

26. Kodi zifuna ndalama zingati kuti anthu adziwe za maphuziro? K _____

27. Kodi zinthu zophuzitsira zifuna ndalama zingati? K _____

28. Nanga zina ndi zina zifuna ndalama zingati K _____

29. Konzani ndondomeko yofotokozera maudindo a nthu mu utumiki wanu K _____

CHITSANZO CHA NTCHITO ZIMENE ANTHU AKUYENERA KUMACHITA

Dzina la udindo pa utumiki: mphuzitsi wa akulu.

Ntchito zake: mphuzitsi wa akulu ali ndi maudindo awa:

1. Kukonzekera ndi kuphunzitsa makalasi a pasabata.

Nthawi _____ tsiku _____ Malo _____

2. Kulondoloza anthu amene sanabwere kudzaphunzira, kuchenjeza ophunzira amene akumajomba komanso kubwenzeretsa ophunzira amene anasiya.

3. Kutengera kwa Yesu ophunzira osapulumsidwa kwa Yesu.

4. Kutumikira zosowa zauzimu kwa ophunzira ndi kuwathandiza kuti iwo akule moyo wao wauzimu.

5. Kulimbikitsa ophunzira kuti akhale mbali imodzi ya mpingo umene adzitengapo gawo pakutumikira.

6. Kulemba zinthu zonse zofunika kulembedwa monga anthu amene ambwera pa kudzaphunzira tsiku lina lilironse.

Zowayenereza anthu:

1. Oitanidwa ndi Mulungu kuti utumikire.

2. Okwaniritsa zomuyenereza mtsogolera malinga ndi Baibulo.

3. Amene anamaliza maphunziro a aphunzitsi a mumpingo.

4. Okhala ndi kuthekera kolankhula ndi anthu ena.

5. Ankhale membala wa mpingo amene amatenga gawo.

6. Amene akugwirizana ndi chikhulupiriro cha mpingo.

7. Okhala ndi ubale wabwino ndi mpingo.

Kudzipereka kwao:

1. Akuyenera kukhala ndi nthawi yokonzekera kukaphuzitsa.
2. Kupezeka mkalasi kuti aphunzitse kwa maola awiri.
3. Kupezeka pa mkumano wa pamwezi wa aphuzitsi.
4. Kupezeka pa maphunziro apachaka aphunzitsi.
5. Kukhala ndi nthawi yokumana ndi anthu ena komanso kuwayendera ophunzira.

Lembani zinthu zoti aphunzitsi asaine kuti adzatsata: Chitsanzo cha izi ndi ichi:

Nditalandira Yesu ngati mbuye ndi mpulumutsi, komanso ndi kukhala naye pachiyanjano ndi iye, ndi kuzindikira kuti kutumikira Yesu kwa anthu ena ndi maitanidwe akulu. Poganizira maitanidwe anga ngati mphuzitsi komanso podalira chithandizo chochokera kwa Mzimu Woyera, ndi kulonjeza kuti:

6. Ndikugwirizana ndi chikhulupiriro cha mpingo, ndipo ndikulonjeza kuti sindidzaphunzitsa chilichonse chosemphana ndi izi.
7. Ndidzakhala ndi nthawi tsiku ndi tsiku yowerenga Baibulo.
8. Ndidzipephera modzipereka kuti ophunzira anga atembenuke mtima komanso kuti akule moyo wao wauzimu kwa iwo amene ndi otembenuka kale mtima.
9. Ndidzapereka nthawi yanga kukonzekera phunziro lina lilironse. Komanso ndidzaikonzekeretsa ndekha moyo wauzimu pokhala moyo ogwirizana ndi zimene ndi maphunzitsa.
10. Ndidzakhala okhulupirika pa udindo wanga ophunzitsa mu mpingo.
11. Ndidzaphuzitsa mau a Mulungu mkalasi komanso ndikuwalimbikitsa ophunzira kuti adziwerenga Baibulo ndikutenga gawo mkalasi.
12. Ndidzatenga gawo pa chipembedzo mu mpingo komanso kuthandiza mpingo magawo azachuma.
13. Ndidzatenga gawo pa mkumano wina ulionse ochitika mu mpingo, pokhapokha patakhalazovuta ndikhoza osapezeka pa mkumano umeneu.
14. Ngati pali zifukwa zina zolepheleretsa kukwaniritsa udindo wanga ngati mphunzitsi, ndidzakambirana ndi atsoleri anga kuti munthu wina ayambe kuphunzitsa kalasi yanga ngati chimenechi chingakhale chinthu choyenera.

Dzina _____ Tsiku _____

CHAPUTALA 15

MFUNDO ZA KULALIKA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokozera tanthauzo la ulaliki?
- Kupeza mitu imene ulariki ukuyera kukhazikika.
- Kufotokozera kufunika kwa kuonetsera mphamvu ya Mulungu polalika.
- Kuzindikira machenjezo asanu ndi awiri okhudza kulalika.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? ndipo adzalalikira bwanji, ngati satumidwa? monganso kwalembedwa, Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino. (Aroma 10: 14-15)

MAU OYAMBA

Chaputala ichi chifotokozera za kulalikira Baibulo. Chifotokozera zinthu ngati tanthauzo la kularika, kufunika koonetsera mphamvu polalika ndi zina zambiri zokhudza ulariki.

KUPHUNZITSA NDI KULALIKA

Mwaphunzira za tanthauzo la kuphunzitsa mu chaputala 1 ndipo tinati:

Kuphunzitsa ndi kupereka chidziwitso kwa anthu ena kudzera kuonetsera, kudziwitsa ndi kutsogolera.

Tanthauzo la kulalika:

kulalika ndi mchitidwe ofaritsa uthenga kwa anthu ena ndi cholinga chofuna kuwadziwitsa kapena kuti kuwaphunzitsa. Muona mu chaputala chikubwerachi kuti kukonzekera kulariki ndi chimodzimodzi ndi kukonzekera kuphunzitsa. Pamene kuphunzitsa ndi kulalika kumasiyana nji njira zophunzitsira komanso mmene uthenga umaperekeredwera.

KUPHATIKIZA ULALIKI NDI UPHUNZITSI

Kufaritsa uthenga wabwino kumakhala kopindulitsa ngati mwaphatikiza ulariki ndi chiphunzitso. Yesu amaphunzitsa komanso kularika.

Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)

(Werenganinso Mateyu 4:17,23; 9:35; 11:1,5; Marko 1:14,38-39; 2:2; Luka 4:43-44; 9:6; 20:1; I Petro 3:19; 4:6).

Yesu anafa ndi cholinga choti kulapa ndi chikhulukiro cha machimo chilalikiidwe:

ndipo anati kwa iwo, 8 Koteru kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacinatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhulukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:46-47)

KUTUMIDWA KUKALALIKA

Ophunzira a Yesu anatumidwa ndi Yesu kuti akalalike:

Ndipo anaika khumi ndi awiri, kuti akhale ndi Iye, ndi kuti akawatume kulalikirira, (Marko 3:14)

Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikirira. (Mateyu 10:7) (werenganinso Mateyu 10:27)

Cholinga cha mpingo oyambilira chinali kulalika uthenga Wabwino kwa amene sanaumve:

Cikho ca dalitso cimene tidalitsa, siciri ciyanjano ca mwazi wa Kristu kodi? Mkatu umene tinyema suli ciyanjano ca thupi la Kristu kodi? (I Akorinto 10:16)

Chimodzimodzi ndi kuphunzitsa, kulalikirira sikunangochitika mkati mwa mpingo kapena mu kachisi mokha ayi:

Ndipo masiku onse, m'Kacisi ndi m'nyumba, sanaleka kuphunzitsa ndi kulalikirira Kristu Yesu. (Machitidwe 5:42)

Komanso anthu amene amalalikirira si anthu okhawo amene anaitanidwa kuti akagwire ntchito ngati atumiki a Mulungu. Okhulupirira anabalarika chifukwa cha chidzuzo ndipo:

Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikirira mauwo. (Machitidwe 8:4) (onaninso Machitidwe 11:19-20)

Ngati okhulupiririra, taitanidwa kuti tikalalike Uthenga Wabwino ku mafuko a dziko lapansi onse:

Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)

MUTU WAULALIKA

Kulalika kukuyenera kukhazika pa Mau a Mulungu. Mwachitsanzo, Mau amene Petro analalika pa Machitidwe 2:12-23 amachokera mu Chipangano Chakale.

Kulakira malinga ndi Baibulo kukuyenera kukhazikika pa zinthu ngati izi:

KULAPA NDI CHIKHULULUKO CHA MACHIMO:

Ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhulukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:47)

Ndipo anaturuka nalalikira kuti anthu atembenuke mitima. (Marko 6:12)

UTHENGA WA UFUMU WA MULUNGU:

Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)
(werenganinso Mateyu 9:35; 11:5; Marko 1:14; 16:15; Machitidwe 4:18; Machitidwe 8:12; 14:7,21; 16:10; 20:25; Aroma 1:15; 15:19-20; I Akorinto 15:1; II Akorinto:12; 10:14; 11:7; Akorinto 1:23;

CHIUKITSO CHA AKUFA:

Obvutika mtima cifukwa anaphunzitsa anthuwo, nalalikira mwa Yesu kuuka kwa akufa. (Machitidwe 4:2)

MAU A MULUNGU:

Ndipo ambiri anaunjikana, kotero kuti anasowa malo, ngakhale pakhomo pomwe; ndipo analankhula nao mau. (Marko 2:2)

Koma Mau a Mulungu akhala cikhalire. Ndipo 10 mau olalikiwa kwa Inu ndi jawo. (I Petro 1:25)

MAU ACHIKHULUPIRIRO:

Koma citani? Mau ali pafupi ndiwe, m'kamwa mwako, ndi mumtima mwako; ndiwo mau a cikhulupiriro, amene ife tiwalalikira: (Aroma 10:8) (Werenganinso Agalatiya 1:23)

ZINTHU ZONZE ZOKHUDZA YESU KHRISTU:

ndi kulalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Kristu ndi kulimbika konse, wosamletsa munthu. (Machitidwe 28:31)

Kwa ine wocepa ndi wocepetsa wa onse, oyera mtima anandipatsa cisomo ici, ndilalikire kwa amitundu cuma cosalondoleka ca Kristu; (Aefeso 3:8)

MTENDERE KUDZERA MWA YESU KHRISTU:

Mau amene anatumiza kwa ana a Israyeli, akulalikira Uthenga Wabwino wa mtendere mwa Yesu Kristu (ndiye Ambuye wa onse) (Machitidwe 10:36)

MTANDA:

**Pakuti mau a mtanda ali ndithu cinthu copusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tirikupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu. (I Akorinto 1:18)
(Werenganinso I Akorinto 1:17-22)**

CHIONETSERO CHA MPHAMVU YA MULUNGU

Chionetsero cha mphamvu ya Mau a Mulungu chikuyenera kuyenda limodzi ndi ulaliki:

Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'amasunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)

Paulo anafokotoza kuti:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (I Akorinto 2:4-5) (werenganinso Marko 1:39: Luka 9:6)

Chionetsero cha mphamvu ndi chofunika chifukwa chakuti zimachitira umboni Mau a Mulungu:

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikiraponseponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

MLALIKI

Mbuyomu tinakambapo za makhalidwe kuti akuyenera kuonekera mmoyo mwa mphuzitsi. Makhalidwe amenewa akuyeneranso kuoneka mmoyo wa munthu amene ndi mlaliki. Akolose chaputala cha 1 akuonetsera makhalidwe okwana atatu owonjezera amenea akuyenera kuoneka mwa mlaliki.

AKUYENERA KUTUMIKIRA KHRISTU

Mtumiki okhukupirika amatumikira Khristu Yesu(V7). Yesu akuyenera kulandira ulemeu mu kulalika kwake.

NDI MTUMIKI WA UTHENGA WABWINO:

“Uthenga umene Petro ndi Paulo analilikira (vesi 23)

NDI MTUMIKI WA MPINGO:

Mpingo unali ndi atumiki (24-25)

MACHENJEZO KWA ALALIKI M'BAIBULO

Ena mwamachenzo akhudza kulalika mu Baibulo ndi awa:

ALALIKI AKUYENERA KUKHALA CHIMENE AMALALIKA:

Ndiwe tsono wakuphunzitsa wina; kodi ulibe kudziphunzitsa mwini? iwe wakulalikira kuti munthu asabe, kodi ulikuba mwini wekha? (Aroma 2:21)

koma ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, ndingakhale votayika ndekha. (I Akorinto 9:27)

TINAITANIDWA KULALIKA MAU A MULUNGU SITINGACHIITIRE MWINA:

Kulalika ndi chinthu chimene anthu oitanidwa akuyenera kuchita opanda kukambirana:

Pakuti ngati ndilalikira Uthenga Wabwino ndiribe kanthu kakudzitamandira; pakuti condikakamiza ndigwidwa naco; pakuti tsoka ine ngati sindilalikira Uthenga Wabwino. (I Akorinto 9:16)

KULALIKA KUKUYENERA KUKHAZIKIKA PA MAU A MULUNGU:

Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa.

Monga tinanena kale, ndipo ndinenanso tsopano apa, ngati wina akulalikirani uthenga wabwino wosati umene mudaulandira, akhale wotembereredwa. (Agalitiya 1:8-9) (werenganinso II Akorinto 11: 4)

CHOLINGA CHOLALIKA CHIKUYENERA KUKHALA CHOYENERA:

Paulo akufotokoza cholinga cholalika uthenga pa Afilipo 1:15-18. Werengani ndimeyi. Paulo akufotokoza kuti:

Enatu alalikiranso Kristu cifukwa ca kaduka ndi ndeu; koma enanso cifukwa ca kukoma mtima; (Afilipo 1:15)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozani tanthauzo la ulaliki?

3. Kodi mutu waulaliki ukuyenera kukhala chiani?

4. Tchulani machenjezo akulalika amene anaperekedwa mu chaputala ichi?

5. Ndi chifukwa chiani chionetsera cha mphamvu ya Mulungu ndi chofunika kwambiri polalika?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Werengani ndime za Baibulo izi zokhudza kulalika

CHIPANGANO CHAKALE NDI ULALIKI

Werenganinso Mateyu 9:35; 11:5; Marko 1:14; 16:15; Luka 4:18; Machitidwe 8:12; 14:7,21; 16:10; 20:25; Aroma 1:15; 15:19-20; I Akorinto 15:1; II Akorinto 2:12; 10:14; 11:7; Akolese 1:23; I Atesalonika 2:9).

CHIPANGANO CHATSOPANO NDI ALALIKI

Mateyu 12:41; Luka 11:32; II Peter 2:5

CHIPANGANO CHATSOPANO NDI ALALIKI

Mateyu 3:1, 4:17,23; 9:35; 10:7,27; 11:1,5; 12:41; 24:14,41; 26:13

Marko 1:4,7,14,38-39; 2:2; 3:14; 6:12; 14:9; 16:15,20;

Luka 3:3,18; 4:18-19,43-44

Machitidwe 3:20; 4:2; 5:42; 8:4,5,12,25,35,40; 9:20,27; 10:36-37,42; 11:19-20; 13:5,24,38,42; 14:7,15,21,25; 15:21,35-36; 16:6,10; 17:3,13,18; 19:13; 20:7,9,25

Aroma 1:15; 2:21; 10:8-15; 15:19-20; 16:25

I Akorinto 1:17-18; 2:4; 9:14-16,18,27; 15:1-2,11,12,14

II Akorinto 1:19; 2:12; 4:5; 10:14; 10:16; 11:4,7

Agalatiya 1:8,9,11,16,23; 2:2; 3:8; 4:13; 5:11

Aefeso 2:17; 3:8; Afilipo 1:15-18; Akolose 1:23,28; I Atesalonika 2:9; I Timoteyo

2:7; 3:16; II Timothy 1:11; 4:17; Titus 1:3; Ahebri 4:2,6; I Petro 1:12,25; 3:19; 4:6; II Petro

CHAPUTALA 16

KUKONZEKERA KULALIKA:

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala chimenechi mukwanitsia kuchita zinthu izi:

- Kufotokozero mwachidule ndondomeko za kapangidwe ka ulaliki.
- Kufotokoza kulalika pa mutu.
- Kufotokoza kulalika kosanthula mau.
- Kukonza ulaliki oti mulalike.

VESI YOTSOGOLERA:

lalikira mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace; tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitsa. (II Timoteyo 4:2)

Mu chaputala chimenechi muphunzira mmene mungalalikire uthenga wa Baibulo. Muphunzira mfundo zikuluzikulu za kulalika pakuona ma ulaliki ena amphamvu amene analembedwa mu Baibulo komanso mu mbiri. Muona kuti kulalika ndi kuphunzitsa ndi kofanana mu njira zambiri ngakhale kuti zinamasiyana mu njira zimene zinagwiritsidwidwa ntchito pofuna kutumikira.

KUSIYANA KWA KUPHUNZITSA NDI KULALIKA

Kuphunzitsa ndi kulalika kumasiyana motere:

NJIRA:

Nthawi zambiri kulalika sikumafuna kuti anthu atengepo gawo. Mwachitsanzo, sipamakhala kukambirana kapena kufunsana mafunso nthawi zambiri pamene munthu akulalika. Chifukwa chake ndi chakuti kulalika nthawi zambiri kumachitika ku gulu la anthu ambiri.

KAPEREKEDWE KA UTHENGA:

Nthawi zambiri pamene anthu akuphunzitsidwa amaikidwa mmagulu malinganga ndi misinkhu yawo. Kalasi imakhala ya ana, kapena anthu akulu nthawi zambiri. Pamene ulaliki umaperekedwa ku gulu la anthu amisinkhu yosiyanasiyana ali pamodzi. Mwachitsanzo ku Sunday school anthu amisinkhu imodzi amaphunzitsidwa pamodzi.

Pazifukwa zimene zaperekedwa pamwambapa. Ndi zofunika kwambiri kuti mulalikire pa mlingo umene munthu wina aliyense akhoza kumvetsa. Chifukwa cha ichi, uthenga siukuyenera kukhala ovuta kwambiri oti anthu achichepere sangamve komanso usakhale ophweka kwambiri umene ukhoza kupangitsa anthu akulu akulu kuti asakhale ndi chidwi.

NDONDOMEKO YA MAPHUNZIRO:

Sunday sukulu ndi maphunziro ena ampingo amakhala ndi ndondomeko ya maphunziro imene iyenera kutsatidwa. Pamene kulalika sikumakhala ndi ndondomeko zimene munthu ayenera kugwiritsa ntchito kapena kuti zinthu zokhazikika zimene zikuyenera kulalikidwa. Pamene ulaliki umeperekedwa malinga ndi mmene munthu walankhuliridwa ndi mzimu wa Mulungu.

KAKONZEDW KA ULALIKI

Ndondomeko zimene zikuyenera kutsatidwa pokonza ulaliki zimene sizosiyana ndi njira zimene zimatsatidwa pakukonza ulaliki. Zina mwa zinthu zimene ndi izi:

15. Dzikonzekeretseni nokha kuuzimu.
16. Unikirani anthu omvera.
17. Khazikitsani zolinga.

Ndondomeko zakayalidwe ka ulaliki ndi izi:

18. Mutu.
19. Chiyambi.
20. Thunthu.
21. Kugwiritsa ntchito zimene saphunzitsidwa.
22. Mathero.

(bwerezani chaputala 1, “kakonzedwe ka phunziro)

Chimodzimodzi ndi kuphunzitsa, mukuyenera kuwakopa omvera anu pamene mukulalika. Zimene mukulalikira zikuyenera kugwirizana ndi moyo watsiku ndi tsiku komanso mukuyenera kuwafunsa anthu kuti achitepo kanthu pazimene mwadalilika.

MITUNDU YA ULALIKI

Pali mitundu ingapo ya ulaliki ndipo ina mwa iyo ndi iyi:

KULALIKIRA PA MUTU UMODZI

Ulaliki wa mutu umakhazikika pa mitu yokhazikika. Mwachitsanzo, munthu akhoza kulalika zinthu ngati chipatso chauzimu, nkondo yauzimu komanso mphatso zauzimu ndi zina zambiri.

Kakonzedwe ka ulaliki wa mutu:

1. Pezani mutu wanu waulaliki. Mwachitsanzo mukhoza kusankha pemphero ngati muti wa ulaliki wanu.
2. Sankhani mutu weniweni kuchokera pa mutu wanu waukulu. Mwachitsanzo. Mitu ina imene mungasankhe ndi iyi:
 23. Kufunika kwapemphero
 24. Mphamvu ya pemphero
 25. Nthawi ya pemphero
 26. Cholinga cha pemphero
 27. Njira zakupemphera
 28. Zotsatira zapemphero
 29. Nyengo zapemphero

30. Kupemphera mu mzimu
31. Kupilira mupemphero
32. Pemphero lodzikhuthula
33. Mayankho amapemphero
34. Pemphero lopembedzera
35. Pemphero lapabanja
36. Zolepheleretsa kupemphera
37. Mapemphero a Baibulo
38. kupemphera koyenera
39. makhalidwe oyenera popemphera
40. chikhulupiliro popemphera
41. kukula kwa zinthu zopemphelera

Ndi zofinika kuti mupeze mutu weniweni okhazikika wa pemphero lanu. Ndi zosatheka kuti mukhoza kukamba chilichonse chokhudza mutu wa ulaliki wanu. Ngati mmene taoneramu, pali mitu yambiri imene imachoka pa mutu umodzi. Mwachitsanzo mukhoza kusankha kulalikira pa mutu wa zolepheretsa za pemphero.

3. Santhulani Baibulo kuti mupeze chinachilichonse chimene Baibulo limakamba chokhudza mutu umene mwasankha kuti mulalikire. Mukhoza kuchita izi pogwiritsa ntchito zinthu ngati zotanthauzira za Baibulo komansi ndi mabuku ena.
4. Yalani mdandanda wa ulaliki wanu malingana ndi mmene mwaphunzirira mu buku limeneli.

Chitsanzo cha pa mutu umodzi:

MUTU: ZOLEPHERETSA PEMPHERO

Chiyambi: khazikikani pa mavuto amene anthu ambiri amakumana nawo: mapemphero osayankhidwa komanso chifukwa chimene samayakhidwa. Izi zikhoza kupereka chidwi chifukwa chakuti anthu ambiri akumana nazo zimenezi.

Thunthu: Kambilanani zolepheretsa zapemphero:

42. Zolinga zolakwika zopemphera: Yakobo 4:2-3
43. Tchino linalilironse. Yesaya 59:1-2.
44. Mafano mmitima ya anthu: Ezekieli 14:1-3.
45. Mtima osafun kukhulukira anthu ena: Marko 11:25.
46. Kudzikonda: Miyambo 21:13.
47. Kuzunza mkazi kapena manuna wako I Petro 3:7.
48. Kudziyenereza nokha kukhala angwiro Luka 18:10:14.

49. Kusankhulipilira: Yakobo 1:6-7.

50. Kusakhala mwa Khristu komanso kusachita mau ake.’

- i. Kagwiritsidwe ntchito kazinthu zimene mwalalikira:
Fotokozerani mmne mapemphero osayankhidwa amakhudzira magwo awa:
 - A. Moyo wa pa banja.
 - B. Moyo wathu wauzimu.
 - C. Utimimiki wathu
- ii. Funsani anthu amene akumvera kuti awunguze zimene mwalalikira pa moyo wao.
 - A. Kodi ndi chotchinga chiti chimene chikulepheretsa mapemphero anu.

Mathero:

- I. Fotokozerani mwachidule zotchinga za pemphero zimene zakambidwa mu chaputala chimenechi.
- II. Pemphani anthu kuti alape kumanso ndi kusiya zonse zolepheretsa kupemphera.

ULALIKI OSANTHULA MAU:

Ulaliki osanthula mau pamakhala ndime imodzi imene imasanthulidwa kapena kukhala nsanamira ya ulaliki wanu.

Kayalidwe ka ulaliku osanthula mau:

1. Sankhani ndime.
2. Pezani mutu wa ulaliki wanu.
3. Santhulani ndime yanu mwatsatanetsatane. Komanso santhulani ndime zina zimene ndi zogwirizana ndime imene mwawerenga. Mukhoza kugwiritsa ntchito zinthu zina zothandiza kuchita kafukufuku wa Baibulo.
4. Yalani mndandanda wa ulaliki wanu ngati mmene tafotokozera pa chaputala 10.

Chitsanzo cha ulaliki osanthula mau:

Ulaliki wa Petro pa Machitidwe 2:14-36 ndi chitsanzo chabwino cha ulaliki umeneu.

Chiyambi: Petro anayamba Uthenga wake ndi Vesi yochokera mu Chipangano Chakale:

komatu ici ndi cimene cinanenedwa ndi mneneri Yoeli, Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, Ndidzathira ca Mzimu wansa pa thupi liri lonse, Ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera, Ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, Ndi akulu anu adzalota maloto; Ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m'masiku awa Ndidzathira ca Mzimu wanga; ndipo adzanenera. (Machitidwe 2:16-18)

Chiyambi chimenechi chinali chopereka chikoka chifukwa chakuti anthu anaona kukwaniritsidwa kwa ndimene imene inawerengedwa ndi maso awo.

Thunthu: Zimene Petro analalikira zinakhazikika pa zimene anawerenga.

- I. Iye anapereka mbiri ya ndime imene imakwaniritsidwa pa tsikulo.
- II. Iye anaonetsa mmene ndime imeneyi inakwaniritsidwira mu mbiri ya Israeli komanso mmoyo wa Khristu Yesu.

Kagwiritsidwe ntchito ka ndimeyi:

Pakuti lonjezano 1 liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, 3 onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana. (Machitidwe 2:39)

Mathero; Anafunsa anthu kuti achite kanthu.

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Machitidwe 2:38)

Mnene anthu anachitira:

Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu. (Machitidwe 2:41)

MTUNDU WACHIWIRI: ULALIKI OFOTOKOZEKERA NDIME

Uwu ndi ulaliki umene umafotokozerana ndime poisanthula vesi ina iliyonse payokha.

Kulalika kumeneku kumakhala kwa tsatanetsatane. Ulaliki umatha kukhazikika pa mutu wina wake kapena pa phunziro linalake. Chifukwa chakuti ulaliki umenewu umasanthula zinthu mozana, maulaliki ake amakhala angapo. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti zimakhala zovuta kuti muthe kufotokozerana zinthu zonse zokhudza mutu wanu mu ulaliki umodzi. Kotere kuti ulaliki wina ulionse umayenera kugwirizana ndi maulaliki ena. Pamene mwayamba kulalika mukuyenera kuonetsa kuti zimene mukulalikira zikugwirizana ndi zimene mwalalika kale.

Koma ngakhale kuti ulaliki wina ulionse umayenera kulumikizana ndi unzake, ndi zofunikanso kuti ulaliki wina uli onse ukhale oima paokha. Si anthu onse amene angapezeke mu ulaliki wina ulionse choncho ndi zofunika kuti wina aliyense athe kumvetsa ulaliki wina ulionse paokha.

Kakonzedwe ka ulaliki:

1. Sankhani mutu, ndime, munthu wa m'Baibulo kapeba buku limene mukufuba kulalika.
2. Werengani chinachilichonse chimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza mutu wanu. Mukhoza kugwiritsa ntchito chinachilichonse chimene chingathandize kuti mumvetse zimene mukusanthula.
3. Unguzani ngati mutu wanu ukhoza kulalikidwa pakamodzi kapena ngati mungafune mauthenga angapo.
4. Pezani mutu wa uthenga kapena mauthenga anu.
5. Lembani mndanda wa Uthenga wanu.

Chitsanzo cha Ulaliki osanthula mutu.

Mutu: makhalidwe a aphunzitsi achinyengo:

Ndime: Yuda Chaputala 1

Chiyambi: Yuda 1:3-4.

Thunthu:

- I. Chiyambi cha ndimeneyi.
 - A. Vesi 4.
- II. Mayendedwe awo
 - A. Obwera mwakachetechete. (Vesi4)
 - B. Oyenda malingana ndi zilakolako zathupi lawo (Vesi 16)
 - C. Oyenda malingana ndi zilakolako zao zosalemekeza Mulungu (Vesi 18)
- III. Mayankhulidwe awo
 - A. Amayankhula zinthu zoipa (Vesi 8-10)
 - B. Amalankhulo zinthu zoipa zimene samazidziwa (Vesi 8-10)
 - C. Ong'ungudza nthawi zonse (Vesi 16)
 - D. Odandaulo (Vesi 16)
 - E. Pakamwa pawo pamalankhula zinthu zotukwana (Vesi 16)
 - F. Ndi anthu onyoza (Vesi 18)
- IV. Chiphunzitso chawo
 - A. Ayesa chisomo cha Mulungu ngati ufulu (vesi 4)
 - B. Amakana Yesu ngati mbuye ndi Mulungu(Vesi4)
 - C. Alibe mzimu (Vesi 19)

Makhalidwe awo

- A. Ndi osapembedza (Vesi 4)
- B. Olota zonyasa (Vesi 8)
- C. Ochita zodetsa thupi (Vesi 8)
- D. Odana ndi ulamuliro (8-10)
- E. Osilira anthu chifukwa cha zimene amapindura (Vesi 16)
- F. Odziputala (Vesi 19)
- G. Amakhala moyo wakuthupi (Vesi 19)

Kangwiritsidwe ntchito ka ndime: kodi tichite bwanji malinga ndi ndime imeneyi: Yuda 1:20-23

Mathero: Fotokokozerani mwachidule ndipo uzani anthu achitepo kanthu malinga ndi uthenga umene waperekedwa.

NDONDOMEKO ZOTHANDIZA

Zina mwa zinthu zimene zikuyenera kutsatidwa pamene tikupanga ulaliki ndi izi:

KUSANKHA NDIME:

Ndime ya Baibulo ndi mau amene ulaliko umakhazikika. Mau a Mulungu akuyenera kukhala nsanamira ya ulaliki wanu. Kugwiritsa ntchito mau a Mulungu ngati nsanamira ya ulaliki wathu zimapereka ulamuliro wa uthenga wathu. Izi zimathandiza kuti anthu azindikire kuti zimene zikukambidwa sizongokamba koma ndi mau a Mulungu.

Zina mwa ndondomeko posankha ndime ya Baibulo ndi izi:

- 1) Pemphani chitsogozo chochokera kwa Mulungu.
- 2) Werengani mau a Mulungu kawirikawiri. Ndime zimene mumalikira zimachokera ku mau amene mumawerenga nthawi zonse. Lembani zinthu zimene mwazipeza pamene mukuwerenga Baibulo. Ndipo mfundo zimenezi mokhoza kugwiritsa ntchito pokonza ulaliki.
- 3) Ganizirani zosowa zauzimu za anthu amene mukufuna kuwatumikira. Mwachitsanzo mkumano wa anthu amene ndi atumiki sukufunika uthenga wa Chipulumutso. (Kumbukirani zimene munaphunzira zokhudza kuunikira anthu omvera)
- 4) Musanalalikire onetsetsani kuti ndime imene mukufuna kulalikira mwa imvetsa.
- 5) Ganizirani mau onse a Mulungu osangoti gawo lokhalo limene limakusangalatsani kapena kuti mutu umene umakusangalatsana. Mau onse ndi ochokera kwa Mulungu kotere kuti ndi opindirutsa.

KUMASULIRA MALEMBA:

Pamene mwasankha ndime imene mukufuna kulalikira, santhulani zonse zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza ndime imene mwasankha. Kotere kuti gwiritsani ntchito chinachilichonse chimene chingakuthandizeni kuti mumvetse ndime yanu. Zina mwa zinthu zimenezi ndi ma Baibulo amene amafotokozera tanthauzo la ndime.

Zina mwa ndondomeko zimene zikuyenera kutsatidwa pomasulira Baibulo ndi izi:

Ulamuliro wa Mulungu: Baibulo liri ndi ulamuliro omaliza. Chifukwa cha ichi gawo linalilironse la Baibulo ndi loozulidwa ndi Mulungu.

Kumasulira mmene zikumvekera: Baibulo limathanthauza zimene limakamba. Koma nthawi zina Baibulo limakhala ndi zifanifani ndi mafanizo koma zimene zimagwiritsidwa ntchito pofuna kuonetsera choonadi cha Mulungu.

Lamuro loganizira zimene zimachitika mu ndime: Ndime iliyonse ikuyenera kuonedwa malinga ndi zimene zimachitika mu nthawi imeneyo. Ziphunzitso zambiri zabodza zinabadwa chifukwa chosaganizira mbiri ya ndimeyo kapena zimene zimachitika pamene ndime imalembidwa. Pamene mukuwerenga ndimeyo ganizirani zinthu izi:

- Ndi ndani akulemba kapena kulankhula?

- Kodi chimene chikukambidwa ndi chiani?
- Kodi zimenezi zikukambidwa kwa ndani?
- Kodi zimenezi zikunenedwa chifukwa chiani?
- Kodi zimenezi zinanedwa nthawi yanji?

Lamuluro la kutchulidwa koyamba: Nthawi zambiri pamene mau kapena chinthu chatchulidwa mu Baibulo koyamba zimapereka tanthauzo lake limene limathandiza kuti mumvetse tanthauzo lake mu ndime zina.

Mwachitsanzi pa Genesisi 3 amatchula masamba a mtengo wa mkuyu. Apa ndi pamene Adamu anagwiritsa ntchito masamba pofuna kubisa maliseche ake ndi kuthekera kwake. Masamba a mkuyu akufotokozera za ungwiro odzipatsa nokha, kukana Mulungu ndi kufuna kudziyenereza tokha pamaso pa Mulungu.

Ichi ndi chifukwa chake Yesu anatembelera mtengo wa mkuyu umene unali ndi masamba koma opanda chipatso pa Mateyu 21 ndi pa Marko 11 ndi 13. Kuti timve izi tikuyenera kubwelera ku mfundo ya kutchulidwa kwa mau koyamba pa Genesis 3. Mtengo wa Mkuyu umaimira kudziyenereza kwa Israeli amene anakana komanso anakanika kubala chipatso chakulapa.

Mfundo/Lamuro la kubwereza: pamene chinthu chabwerezedwa mu Baibulo, cholinga chake chimakhala kufuna kutsindika. Izi zimaonetsa kuti choonadicho ndi chofunika kotere kuti ndi chofunika kubwerezedwa.

Mfundo yobweretsa zinthu zonse pamodzi:

Mfundo imeneyi imatanthauza kuti choonadi cha mau a Mulugu pa mutu wina ulionse chikuyenera kuchokera mu Baibulo lonse osati ndime imodzi. Izi zikutanthauza kuti mukuyenera kusanthula Baibulo lonse pa mutu wina ulionse. Simungapange chiphuphunzitsa kuchokera ku vesi imodzi.

Kubweretsa zinthu pamodzi kuti mupange ulaliki:

Pamene mwasankha ndime yoti mulalikire, mukuyenera kubweretsa pamodzi zinthu zonse zimene mwapeza. Kufunsa mafunso awa zikhoza kukuthandizani:

1. Kodi Baibulo limaphunzitsa chani pa za izi? Cholinga chenicheni ndi kuzindikira zimene Mulungu wavumbulutsa mmau ake. Izi ndi zimene zikuyenera kupanga gawo lalikulu la mau ulaliki wanu.
2. Kodi ndi chani chimene chikugwirizana ndi mau amenewa pa utumiki komanso pa moyo. Kodi munaona choonadi chimenechi chikugwira ntchito mmoyo watsiku ndi tsiku. Mukhoza kugwiritsa ntchito zitsanzo pofuna kuonetsera kufunikwa kwa uthenga umene mukulalikira.
3. Kodi ndi chani chimene mwawerenga chokhudza mutu umene mukufuna kuwerenga. Ngati muli ndi zina zowerenga monga ma Baibulo amene amafotokozera mau, gwiritsani ntchito zinthu zimenezi.

4. Kodi ndi ndani amene ndikumudziwa amene ali ndi chidziwitso cha zinthu zimenezi? Alipo amene anakuma ndi zimene ndimeyi ikukamba. Kodi alipo munthu wina amene mukumdziwa kuti anaphunzira mozama zimene mukufuna kulalikira. Ngati alipo mukhoza kuwapeza anthu amenewa pakukonzekera kwanu.

CHOLINGA CHOMARIZA:

Chaputala chimenechi ndi chomaliza mu phunziro la ukadaulo wa kuphuzitsa. Koma zoonza zake ndi zakuti ichi ndi chiyambi chabe chifukwa mukuyenera kuputilira kulalika kufikira cholinga chanu chomaliza chakwaniritsidwa.

amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, 8 kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu; (Akolose 1:28)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozerani ubale wakulalika ndi kuphuzitsa. Kodi zinthu zimenezi zimafanana komanso kusiyana bwanji?

3. Fotokokozerani ndondomeko za kukonzekera kulalikira?

4. Kodi kulalika pa mutu ndi chiani?

5. Kodi kulalika kosanthula malemba ndi chiani?

6. Kodi kulalikira kofotokozerani ndimendi chiani?

7. Fotokozerani mwachidule ndondomeko zothandiza pasankha ndime.

8. Fotokozerani mwachidule ndondomeko zothandiza kumasulira ndime

9. Footokozerani ndomeko zothandiza kubweretsa zinthu pamodzi pokoza ulaliki?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani ma ulaliki akuluakulu opezeka mu Baibulo ali munsimuwa:
 - Ulaliki wa mose otsanzika: Deteteronome 29:33.
 - Ulaliki wa Yoswa otsanzika: Yoswa 24:2-15.
 - Samueli alankhula ndi Israeli: I Samueli 12
 - Uthenga wakulumbitsidwa kwa Solomoni: I Mafumu 8:15-61.
 - Uthenga wa Yereimiya kwa anthu: Yereimiya 7
 - Zitsanzo za Maulaliki a Yesu: Mateteyu: 5-7; 11:7-19; 12:25-37; 13; 15:10-20; 21:28-44; 24-25; Yohane 3:3-21; 6:26-58; 14-16
 - Uthenga wa Petro Machitidwe 2:14-36; 3:12-26
 - Mauthenga a Paulo: 13:16-41; 17:22-31; 20:17-35; 22:1-21; 26:2-23
 - Uthenga omaliza wa Sitefano: Machitidwe: 7:2-53
2. Gwiritsani zimene zalembedwa pa tsamba lachiwiri kuti muunikire uthenga umene munamvapo kapena umene mumve. Komanso gwiritsani ntchito zimenezi kuti muunikire uthenga wanu.

NDONDOMEKO ZOTHANDIZA KUUNIKIRA UTHENGA.

CHIYAMBI:

Kodi uthengawo ukupereka chidwi? _____ kodi uthengawo ukukhudza zosowa zinazake kapena ayi?

Kodi uthengawo ukupereka mfundo zimene simumadziwa? _____

Kodi kutalika kwa uthenga ndi koyenera? _____ kodi uli ndi cholinga chogwirika?

Thunthu:

Kodi kayalidwe kauthenga mkomveka? _____ kodi uthengawo wayalidwa moyenera? ____

Kodi mfundo zauthengazo ndi zolumikizana bwino? _____

Kodi mfundo zikuluzikulu zikugwirizana ndi mutu wauthengawo? _____

Kodi mfundo zing'onozing'ono zikugwirizana ndi mfundo Yaikulu?

Kagwiritsidwe ntchito ka Uthenga.

Kodi mutu wauthenga ndi ofunika? _____ kodi ndi oyenera? _____

Kodi uthenga wakhazikika pa mfundo zolondora za kamasulidwe ka Baibulo? _____

Kodi amene akulalikira akuonetsa pamene ali mu ndime ya Baibulo.

Kodi kusanthula kwa mutu wauthengawo ndi kokwanira?

MATHERO:

Kodi uthenga ukufika pachindeinde? __ kodi mlaliki akufotokozero mfundo zauthenga mwachidule? _____

Kodi mathero authenga akuitanira anthu kuti achitepo kanthu? _____

Kaperekedwe kauthenga?

Kodi mlaliki akugwiritsa malamuro a chiyankhulo moyenera? Kodi iye akatchula mau moyenera?

Kodi akugwiritsa ntchito mau oyenera komanso osiyanasiyana? _____

KAFOTOKOZEREDWE KA UTHENGA:

Kodi mlaliki mukuona ngati cholinga chake ndi chakuti alankhule ndi muthu? _____

Kodi uthenga wake mu njira imene ikuonetsera kuti pali ubale pakati pa inu ndi mlalikiyo? _____

Kodi mau ake ndi osavuta kuwamva? _____

Kodi mau akumasinthatintha? _____

Kodi olankhulayo akumapuma polankhula? _____

Kodi pali makhalidwe ena alionse amene ndi osokoneza? _____

Kodi makhalidwe kapena maimidwe ali bwanji? _____

Kodi mkhope ya munthu ikuoneka bwanji?

LALIKIRANI KUTI MUPEZE ZOTSATIRA

Wolembe Charles Finney

Kodi cholinga chanu cholalika ndi chiani? Ngati cholinga chili chofuna kuti mutchuke nde kuti mauthenga anu cholinga chake adzikhala ongofuna kutchuka osati kubweretsa anthu kwa Yesu.

Kodi mumapewa kulalika mauthenga amene samakomera anthu ena? Kodi mumakhudzika kuti omvera anu akhoza kunena kwa inu zimene ananena kwa Yesu Khristu? Kodi mumaopa kusokoneza chikumbumtima cha omvera anu?

Kodi ndi njira zANJI zimene mumagwiritsa ntchito? Kodi mumagwiritsa zitsanzo zANJI pofuna kufotokozera mfundo zanu. Kodi muli ndi njira zabwino zofuna kubwereza mfundo zanu?

Kodi munagokhazikika pongowakopa mtima anthu chabe osati kuti mufikire chikumbu mtima chao? Kodi mumachitira umboni za Uthenga wabwino kuchokera pa zimene mwakumana nazo osati kudzera mu mphamvu ya Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu?

Kodi mumaopa kukumbutsa anthu zinthu zakale zowawa zimene anakumana nazo powakumbutsa machimo akale. Cholinga cha Satana ndi chakuti mungotchula machimo mongodutsamo osati kutchula mwachundunji zimene anthu akuchita.

Atumiki ofoooka amaopa kuitanira anthu kuti achite choonadi cha Mulungu mwamachawi. Koma kukanika kumvera choonadi cha Mulungu mwachangu ndi kusamvera kumene. Mukuyenera kukhala amphamvu ndithu polamura anthu kuti achite monga mwa chifuniro cha Mulungu komanso ndi kuchitapo kanthu mwachangu pamene Mau a Mulungu alalikidwa. Mukuyenera kukhala ndi chiyembekezo kuti anthu apereka moyo wao kwa Mulungu Pamene mwalalikira Mau a Mulungu. Kodi mumakhala ndi chiyembekezo kuti anthu sakuyenera kubwelera ndi machimo awo ndi chikuchitapo kanthu mu nthawi imene akonzeka iwowo? Kodi iyi ndi njira yabwino yofaritsira Uthenga Wabwino.

Kodi mumauza anthu kuti sangathe kumvera? Kodi akuyenera kudikira Mulungu kuti ndi amene angawasinthe? Kusintha kumabwera pamene anthu apereka moyo wao kwa Yesu Khristu. Athandizeni anthu kuti alandire chipulumutso nthawi imene mwalalikira. Ndi koyenera kulalika kuti chipulumutso ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. Koma mukuyenera kufotokozera kuti ochimwa onse amene akumvera ulaliki wanu ndi oweruzidwa komanso otaika pamaso pa Mulungu. Ndi chifukwa cha ichi adzamvetsa chisomo Mulungu. Lalikirani za Uthenga Wabwino ngati njira yokhayo yochizira matenda a tchimo ndipo simukuyenera kubisa kapena kulekelera matenda a munthu ochimwa amene zotsatira zake ndi imfa ku Gahena.

MAYANKHO AMAFUNSO ODZIYENSE NOKHA:

CHAPUTALA 1

1. Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:18-19)
2. Mau oti kuphuzitsa amanthauza kuonetsera, kudziwitsa ndi kupereka chidziwitso kwa munthu wina. Mphuzitsi ndi munthu amene amaphuzitsa. Pamen kuphuzitsa ndi mtchitidwe ophunzitsa anthu ena.
3. Aphunzitsi ndi ofunika chifukwa amathandiza kufotokozera za choonadi cha Mau a Mulungu kwa anthu osakhulupirira komanso kwa anthu okhulupirira. Popanda aphuzitsi anthu ali ngati khosa zopanda abusa.
4. Udindo wautsogoleri wa mphuzitsi ndi udindo umene umatsogolera anthu mu mpingo kuonjezera kuphunzitsa. Munthu amene ali ndi mphatso yauphuzitsi yolankhula amangophunzitsa sakhala ndi udindo wina ulionse.
5. Chiganizo chimenechi ndi choona.
6. Tikuyenera kuphunzitsa anthu onse okhulupirira amene akhoza kuphuzitsa anthu ena.
7. Zolinga ziwiri zakuphunzitsa andi kupanga ophunzira ndi kufaritsa uthenga Wabwino.
8. Machenjezo atatu okhudza kuphunzitsa ndi awa:
 - Kuphunzitsa kukuyenera kukhazikika pamaso pa Mulungu osati ziphunzitso za anthu.
 - Aphuzitsi akuyenera kukhala zimene amaphuzitsa.
 - Padzakhala aphuzitsi onyenga.

CHAPUTALA 2:

1. Iyeyu anadza kwa Yesu usiku, nati kwa iye, Rabi, tidziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wocokera kwa Mulungu; pakuti palibe munthu akhoza kucita zizindikilo zimene inu mucita, ngati Mulungu sakhala naye, (Yohane 3:2)
2. Fanizirani yankho lanu ndi chaputala 2.
3. Fanizira yankho lanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 2.
4. Fanizirani yankho lanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 2.
5. Yesu Khristu.
6. Fanizira yankho lanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 2.
7. Fanizirani yankho lanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 2.
8. Yesu Khristu.

9. Yohane 20:21.
10. Ngati mene Atate anatumira Yesu Khristu, nafenso tatumidwa kuti tikakwanitse cholinga cha Khristu Yesu.

CHAPUTALA 3:

1. Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)
2. Uthenga wa Yesu unali okhazikika pa za Ufumu wa Mulungu. Zina mwa zimenezi ndi mmene munthu angalowere mu ufumu wa Mulungu, komanso mmene munthu angakhalire mu Ufumu wa Mulungu.
3. I Akorinto 15:1-4.
4. Chiganizo chimenechi ndi cholondora.
5. Mphamvu.
6. Mau a Mulungu.

CHAPUTALA 4:

Palibe mayeso odziyesa nokha a Chaputala chimenechi.

CHAPUTALA 5.

1. Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'amasunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)
2. Fananizani mayankho anu ndi chaputala ichi.

CHAPUTALA 7.

1. Koma Iye, poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi cisoni cifukwa ca iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhusa zopanda mbusa. Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka. (Marko 9:36-37)
2. Zothandizira pophunzita ndi chinthu chimene chimathandiza kuti phunziro lanu liyende bwino. zikhoza kukhala ntchito imene ophunzira auzidwa kuti achite pofuna kuonetsera choonadi cha Baibulo. Komanso chikhoza kukhala chinthu chooneka ndi maso kapena chomveka ndi makuti.
3. Mau oti Audio amatathauza kumva. Pamene mau oti Visul amatanthauza kuti kuona. Izi ndi zinthu zimene zimathandiza ophunzira kuti athe kumva ndi kuona choonadi kudzera muzinthu zooneka ndimaso kapena zomveka ndi makuti awo.

4. Zothandizira pophuzira ndi zofunika kwambiri chifukwa chakuti kumva ndi kuona ndi njira zikuluzikulu zothandiza pophuzira.
5. Amagwiritsa ntchito zinthu zosavuta zopezeka malo amene anamuzungulira.

CHAPUTALA 8:

1. Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa iye anadziwa anthu onse, ndipo sanasowa wina acite umboni za munthu; pakuti anadziwa iye yekha cimene cinali mwa munthu. (Yohane 2:24-25)
2. Anthu omvera ndi gulu la anthu limene mukhale mukhale mukuluphuzitsa. Kuunikira chinachake ndi kuunikira mosamalitsa makhalidwe a chinthucho komanso kuchisanthula chonse. Kuunikira ophuzira kumatanthauza kusanthula makhalidwe a gulu la anthu limene mukufuna kuphuzitsa.
3. Kuunikira ophuzira ndi kufunika chifukwa chakuti kuphuzira kumakhudzidwa ndi zinthu zambiri monga chikhalidwe, maphunziro amene, kukhwima muuzimu komanso ndi kapezedwe kachuma ka anthu ndi zina zambiri. Ngati simungaunikire anthu ophuzira anu, zikhoza kutheka kuwaphuzitsa kuposa kuthekera kwao kapena zinthu zochepa mphamvu malingana ndi kuthekera kwao mmagawo osiyanasiyana. Zikhozanso kutheka kuwaphuzitsa muchilankhulo chimene iwo samvetsa. Izi zikhoza kupangitsa kuti musawafikire madera ena amoyo wao.
4. Fananitsani kuofotokozerana kwanu ndi zimene zakambidwa mu chaputala 8.

CHAPUTALA 9:

1. amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphuzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, 8 kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu; (Akolose 1:28)
2. Cholinga ndi chinthu chimene mukufuna kukwaniritsa pamapeto. Pamene aphuzitsi afotokozerana zolinga, zimenezi zimalembedwa ngati zinthu zimene ophuzira akuyenera kukwanitsa pamapeto pa phunziro.
3. Zimathandiza aphuzitsi pa maphunzitsidwe awo, chokonzero chawo komanso ndi zonse zimene zichitike pofuna kuphuzitsa.
 - Zimagwira ntchito pofuna kuona ngati kuphuzira kukuyenda bwino.
 - Zimathandiza kuti mukonze maphunzitsidwe anu.
 - zimathandiza ophuzira kuti akhale akuchita mau osati akungomva chabe.
4. Zolinga zazikukulu ndi zolinga zimene ophuzira amayenera kukwanitsa pamapeto paphunziro lonse. Pamene zolinga zazing'ono ndi zolinga zimene zimayenera akukwaniritsidwa pa phunziro linalilironse lophuzitsidwa.
5. Cholinga B ndiye cholondora. Chikufotokozerana zimene zikuoneka mwa ophuzira.
6. Cholinga chenicheni chophuzitsa Baibulo chafotokozeredwa pa Akolose 1:28.

CHAPUTALA 10:

1. Mphunzitsi wa mzeru amapangitsa kuphunzira kukhala kosangalatsa (Miyambo 15:2)
2. Fananitsani zimene mwapeza ndi zimene zakambidwa pa chaputala 10.
3. Chiyambi.
 - Thunthu.
 - Kugwiritsa ntchito.
 - Mathero.
4. Fananitsani kufotokozera mwanu mwachidule ndi zimene zakambidwa pa Chaputala 10.
5. Palibe yankho limene ndi londora kapena lobodza. Cholinga ndi cha izi ndi chakuti muthe kwakwanitsa kukonzekera phunziro pogwiritsa ntchito mfundo zimene mwaphunzira.

1. CHAPUTALA:11

kuti mukayese inu zinthu zosiyana; kuti mukakhale a mtima woona ndi wosalakwa, kufikira tsiku la Kristu; (Afilipo 1:10)

2. Kuunikirani ndi kusanthula zinthu zinthu mosamala zinthu.
3. Ndi zofunika kuunikira maphuzitsidwe athu ngati tikufuna kupititsa patsogolo mphatsi imene Mulungu anakupatsani.
4. Zolinga.
 - Mmene anthu alandilira zinthu.
 - Mayeso.
 - Kachitidwe ka aphunzitsi.
5. Fananizani kufotokozera kwanu ndi zimene zalembedwa pa Chaputala 11.
6. Mukhoza kugwiritsa ntchito zimenezi kuti zikuthandizeni kuti mukule moyo wauzimu. Komanso mukhoza kupititsa patsogolo mphatso yanu ngati mphuzitsi.

CHAPUTALA 12:

1. Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsi, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (II Timoteo 3:16-17)
2. Mau oti ndondomeko yamaphunziro amatanthauza zinthu zonse zimene anthu akuyenera kuphunzira mu maphunziro a Baibulo sukulu.
3. Fananizani yankho lanu ndi zimene zikupezeka pa chaputala 12.

CHAPUTALA 13.

1. cifukwa mau amene munandipatsa Ine ndinapatsa iwo; ndipo analandira, nazindikira koona kuti ndinaturuka kwa Inu, ndipo anakhulupira kuti Inu munandituma Ine. (Yohane 17:8)
2. Kuphuzitsa anthu kuti akhale aphuzitsi ndi kuphuzitsa anthu amene ndi aphuzitsi kale.
3. Fananizani zimene mwapeza ndi zimene zikupezeka pa chaputala 13.
4. Pakapezedwe aka ophunzira, werengani ndondomeko zimene zaperekedwa pa chaputala 14.
5. Fananizani zimene mwapeza ndi zimene zili pa chaputala 14.
6. Fananizani zimene mwapeza ndi zimene zili pa chaputala 14.
7. Mukhoza kuunikira aphuzitsi:
 - Pogwiritsa ntchito ukadaulo umene mwapeza pa chaputala 11.

- Pazimene apatsidwa kuti adzichita.
- Malingana ndi zimened analonjeza kuti adzakwanitsa kuchita.
- Pakuyang'anira akuphuzitsa.
- Pakuyang'anira zipatso zakuphunzitsa kwao.

CHAPUTALA 15:

1. Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? ndipo adzalalikira bwanji, ngati satumidwa? monganso kwalembedwa, Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino. (Aroma 10:14-15).
2. Kulalika ndi kulumikizana ndi anthu anthu pa mutu umene waunukiridwa mozama.
3. Fananizani zimene mwapeza ndi zimene zikupezeka pa chaputala 15.
4. Alaliki akuyenera kukhala chimene amalalika.
 - Ngati munaitanidwa kukhala mlaliki, simangachitirensa mwina koma kutero basi.
 - Kulalikirira kukuyenera kukhazikika pa mau a Mulungu.
 - Cholinga chikuyenera kukhala choyenera.
5. Kuonsetsera mphamvu ya Mulungu kumachitira umboni za mau amene akulalikiridwa.

CHAPUTALA 16:

1. lalikira mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace; tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitsa. (II Timoteo 4:2)
2. Kusiyana kwakulu pakati pa kulalika ndi kuphuzitsa ndi uku:
 - Njira zimene zimagwiritsidwa ntchito polalika ndi ndi zosiyana ndi zophuzitsira. Njira zimene zimene zimafuna kuti ophunzira atenge mbali sizimagwira ntchito polalika chifukwa chakuti ulaliki umachitika nthawi zambiri pakati apa anthu ambiri.
 - Kaperekedwa ka uthenga kamayenera kukhala kosiyana polalika chifukwa chakuti pamakhala anthu amisinkhu yonse choncho ndi zofunika kuti uthenga ukhale ogwirizana ndi msinkhu wa anthu onse.
 - Ulaliki sumakhala ndi ndondomeko yamaphunziro ngati mmene zimakhallira ndi sukulu Sunday. Pamene ulaliki munthu amachitira mmene akuonera.